# REFORMED CHURCH IN ZAMBIA
# HYMN BOOK. (COMPLETE EDITION)
EDITED BY ELIAS MUTEYA, LILANDA CONGREGATION

## 1
1. NDINU wakuyera! Wamphamvu zonse.
Nthaŵi ya m'mamaŵayi tiimba nyimboyi.
Mlengi wachifundo, tikuyamikani,
E! Mlungu Mmodzi mwa Atatuwo.
2. Ndinu Wakuyera! Anthu ochuluka
Akuimbirani, nakupempharanibe;
Akumwamba omwe nagwadira Inu,
Wachikhalire ndi wosafa 'yi.
3. Ndinu wakuyera! Ife akuchimwa
Zaulemerero zanu sitiona'yi;
Mwayera nokha, wina saoneka
Wangwiro m'mphamvu ndi m'kuyeramo.
4. Ndinu wakuyera! Zakumwamba zonse
Ndi zapansi zitamabe dzina lanulo;
Mlengi wachifundo, Mphambi, Ambuyathu,
E! Mlungu Mmodzi mwa Atatuwo.

## 2
1. INU Mulungu, tikuyamikani;
Tivomereza ndinu Ambuyathu;
Ponse, atate, akugwadirani,
Ndinu wamuyaya!
2. Nanu akukuzani amithenga,
Nanu zam'mwamba ndi zamphamvu zake,
Nanu angelo a mitundu yonse
Akuimbirani:
3. Mbuye Woyera! E, Woyera nokha!
Mbuye Woyera! Mbuye wa makamu!
Ponse ulemu wanu ndi wodzaza
Pansi ndi Kumwamba."
4. Nanu Atumwi akumveka aja,
Ndi Aneneri oyanjana omwe,
Ndi aunyinji anakuferani
Akuyamikani.
5. Mpingo woyera wa kwa anthu onse
Ukumverani Mfumu ndi Atate,
Mwana woona wa ulemu wonse,
Mzimu Nkhoswe yemwe.
6. Khristu Mfumuyo yaulemerero!
Mwana wosatha wa Atate ndinu!
Simunanyoza mimba ya Namwali
Potipulumutsa.
7. Imfa mutagonjetsa ndi zoŵaŵa.
Njira munatsegula tikaloŵe
Momwe mukhala Inu ndi Atate
Mwaulemerero
8. Kumva milandu yathu mudzabwera
Mutithandize, atumiki anu;
Mwatiwombola nawo mwazi wanu:
Mutipulumutse.
9. Mtiŵerengere m'Mwamba ndi oyera;
Mutidalitse, ndife anthu anu;
Moyo wosatha, mutipatse tonse,
Mutilamule.
10. Tsiku ndi Tsiku timalemekeza:
Nanu tikukuzani osaleka;
Mbuye, mtisunge tingachimwe lero;
Mtichitire nsisi.
11. Mbuye, chifundo chanu chitigwere
Monga tikhulupira inu nokha:
Ndakhulupira zedi mwanu, Mbuye
Ndisagome konse!

## 3
1. ATATE wa Kumwambako,
Munawombola ife ndi
Chikondi chanu chijacho;
Tiyamikira Inutu.
2. Ambuye Yesu Inutu
Munabadwira anthu 'fe;
Munatifera tonsefe;
Tiyamikira Inutu.
3. Mzimu Woyera, m'mtimamo
Tiyeretsedwe ndinutu;
Munatisunga bwinoli;
Tiyamikira Inutu.
4. Atate, Mwana, Mzimunso,
Ndinu Atatu Mmodzitu,
2
Ochimwa tikupemphani:
Mutikhululukire 'fe

## 4
1. LEMEKEZA Mulungu 'Tate,
Lemekeza Mulungu Mwana,
Lemekeza Mulungu Mzimu,

Mulungu Mmodzi ndi wamkulu,
Lemekeza, lemekeza
Mulungu wathu yemweyo.
2. Mlemekeze, anakonda
Natitsuka m'mtima mwathu;
Anatiwombola ife
Tikakhale ndi chifumu.
Lemekeza, lemekeza
Yesu Mbuye Nsembeyo.
3. Lemekeza Mfumu yathu,
Mfumu ya mipingo yonse,
Ipambana anthu onse
Akumwamba ndi apansi.
Lemekeza, lemekeza
Mfumu ya mafumuyo.

# 5

1. Ndi aleluya imbirani
   Tate wathu wakumwamba,
   Analenga zones,
   Chifundo chache chachikulu,
   Nzeru mphamvu ndi unfumu,
   Tayamike tonse.
2. Ndi aleluya imbirani
   Yesu Kristu Mpulumutsi,
   Anachoka kwawo,
   Nakhala munthu pansi pano,
   Nasauka, natifera,
   ……… mawu,
3. Ndi aleluya imbirani
   Mzimu wake wakuyera
   Amakhala nafe.
   Atilangisa na Mulungu
   Nayeretsanso mitima
   ya akristu ife.
4. Mulungu wathu tiyamika,
   "Tate, Mwana, Mzimu yemwe,"
   Aleluya inu.
   Woyera inu ndi wamphamvu,
   Muyenera anthhu onse
   Agwadira inu.

# 6

1 MITAMBO inu yakumwambako
Yogunda mvula m'mlengalengamo,
Mawu akulu muzinenadi:
Aleluya.
2 Paphiri paja papakulupo,
Pamwala ponse pakuŵala mbuu!
Mumvomereze mawu omwewo:
Aleluya.
3 Mphepo yay'kulu yakuwombayo,
Chisanu chija chozizirachi,
Ndi kabvumbulu muzinenadi;
Aleluya.
4 Mitengo yaitalitali 'nu
Yachiimire mumaimabe,
Mubvomereze ndi kunenabe:
Aleluya.
5 Zam'madzi zonse zakuopsyazo,
Nyanja, matiti ndi mitsinjeyo,
Chigumula chakulindimacho,
Aleluya.
6 Zamoyo zili m'thengo zonsezo,
Zodzuma, zina zobangulazo,
Zimene ndi kulira konseko:
Aleluya.
7 Inu mumvere anyamatawo,
Okondedwa kuseŵerako,
Mumtima mubvomere monsemo:
Aleluya.
8 Ndi anamwali obvekedwa mbuu!
Ndi ana osakula msinkhu 'nu
Ana a Mulungu mubvomeretu:
Aleluya.
9 Akulu nonse ndi mafumu 'nu
Magulu nonse apadzikopa,
Mumlemekeze Mbuye yemweyo:
Aleluya.
10 Ndi amithenga akumwambako,
Ndi anthu ndi zamoyo zonsezo,
Bvomerezani mau omwewo:
Aleluya.

# 7

1. TAMANI Ambuye,
Wamphamvu ndi Iye
Akhala m'ulemu
Kumwamba komweko:
Chikopa cholimba

Ndi kothaŵiranso
Kwa anthu akewo,
Kotero ndi Mlungu.
2. Uzani zamphamvu,
Imbani chisomo,
Za Mwini ulemu,
Ambuye wathuyo;
Powomba chimphepo
Mvulanso ndi bingu
Padziko, pathambo,
Akhala ponsepo.
3. Zozizwa za m'dziko,
Za m'mwamba zonsezi,
Mulungu wamphamvu,
Munalenga zonse;
Muyendetsa mwezi
3
Nyenyezi ndi dzuŵa:
Zolengedwa zonse
Zimvera Ambuye.
4. Sitiha ifedi
Kukamba zokoma
Za Inu Mulungu
Wolera anthuwa;
Zifika ndi mphepo
Ndi mvula ndi dzuŵa,
Zigwera ponsepo
Pa anthu onsewa.
5. Wamphamvu yosatha,
Chikondi changwiro,
Angelo akonda
Kutama Mulungu;
Ndiponso ifetu
Ananu tonsefe
Tiyimba nyimboyi
Yotama Ambuye.

# 8

1. TSOPANO linoli
Tiimbe nyimbo zathu;
Tiimbe nyimbozi,
Titame Mlungu wathu;
Masiku onsewo
Anatisungadi,
Anatipatsanso
Zabwino zonsezi.
2. Mulungu yemweyo
Akhale m'fupi mwathu;
Mtendere wakewo
Ukhale m'mtima mwathu;
Titsate Iyedi
Ndi nsoni zakezo,
Panjira yakeyi
Masiku onsewo.
3. Tilemekezetu
Atate wakumwamba,
Ndi Yesu Mbuyathu,
Ndi Mzimu Wakuyera;
Mulungu Mmodziyu
Wanthaŵi zonsezo,
Timlemekezetu
Masiku onsewo.

# 9

1. NDI mitima yokondwera
Mbuye wathu tiyamika.
*E, chifundo chake chonse*
*Ndi chosatha nthaŵi zonse.*
2. Dzina Lake Tibukitsa,
Mlungu ndiye yekhayekha.
3. Mphamvu yake inalenga
Dziko lonse ndi kumwamba.
4. Anatsogolera kale
M'chipululu anthu ake.
5. Ndi chifundo atipenya
Ife anthu osauka.
6. Amaŵeta nyama zonse.
Zingasoŵe kanthu konse.
7. Tiimbire Mlungu wathu
Waulemu ndi wamkulu.
8. Tithaŵire kwa Mulungu,
Ndiko tikapeze moyo.

# 10

1. NDITAMATU Ambuyangayu,
Moyo wanga wonse ndidzamtamatu,
Ndiponso dziko lakumwambako;
Masiku anga onse ndidzamlemekeza Iye;
Sindizaleka konsekonse m'mene ndili m'moyotu,
Padziko pano pena m'Mwambamo.
2. Ndiye wokondwa, E, munthuyo

Wokhulupirira Mlungu yekhadi,
Wolenga dziko, nyanja, zonsezi;
Choona chake chonse chingokhalatu chosatha;
Apulumutsa onse namadyetsa anthu akewo,
Wokonda ndiye Mbuye wathuyo.
3. Mlungu kuona athiratu
Inde m'maso awo osapenyawo.
Natuma akumvera mpumulo;
4
Amathandiza inde aulendo awo ofokatu,
Akazi amasiye maka ndi anawo onsewo,
Olira otonthoza mtimadi.
4. Nditama Ambuyangayu,
Moyo wanga wonse ndidzamtamatu
Ndiponso m'dziko lakumwambako;
Masiku anga onse ndidzamlemekeza Iye:
Sindidzaleka konsekonse m'mene ndili m'moyotu,
Padziko pano pena m'Mwambamo.

# 11

1. Paphiri ndi padambo
Ponsepo pali Mlungu,
Poyenda ife m'njira
Mpoima pali Mlungu;
Kokwera Maganizo,
Komwe kuli Mlungu,
Kumwamba ndi pansipo
Ponsepo pali Mlungu.
*(Mulungu ali nane!)*
*(Ali nane, ali nane, ali nane*
*Ali nane, Aa!*
*Mulungu ali nane!)*
2. Ndi maso Ambuyathu
Apenyetsetsa ife;
Amadalitsa onse
Okhulupira Iye;
Amamva timbalame,
Nabveka dziko lonse;
Sataya tizirombo,
Asunga zina zonse.
3. Okwaŵa pansi inu,
Oyenda m'madzi inu,
Oyesa dziko nkwanu,
Am'mlengalenga inu,
Nonsenu ntchito zake
Muona tsiku n'tsiku,
Saleka kusamala
Ndikudalitsa inu.
4. Nditama mphamvu yake
Ya Mlungu yondizinga;
N'kafoka an'limbitsa,
N'kadwala andichiza
Pakundisiya bwenzi
Mulungu ali paja;
N'kaloŵa imfa ine
Alipo Mlungu wanga.

# 12

1. Mtima wanga uyamike
MfumuYakumwambako;
Anandiwombola ine
Nanditsuka m'mtimamo
*Ife tonse, ife tonse,*
*Tiyamike Mlunguyo.*
2. Tiyamike Mulungu wathu,
Kaamba ka chifundocho;
Nthaŵi zonse sasanduka
Mlungu wathu yemweyo
3. Nthaŵi zonse monga 'Tate
Atisamaliratu,
Atisunga m'manja mwake,
Atipulumutsatu.
4. Anthu a mitundu yonse,
Ndipo a Kumwambako,
Yamikani Mungu wathu,
Ndiye wakukomatu.
*Anthu onse, anthu onse,*
*Yamikani Mlunguyo.*

# 13

1. YEHOVA ndiye Mbusa wanga,
sin'ngasoŵe konse:
Andigonetsa pali busa
la misipu yonse.
*(Ndiye Mbusa wanga,*
*Ndiye Mbusa wanga!*
*Yehova ndiye Mbusa wanga,*

*Sin'ngasoŵe konse.)*
2. Kumadzi kuli njiratu
5
andiyendetsa bwino,
Nalimbikitsa moyo wanga
ndi chifundo chino.
3. Pabande lolunjika
andilondolera njira;
Chifukwacho cha dzina lake
anandisungira.
4. Chigwa choopsacho cha imfa
ndikachiloŵera,
Ndilibe mantha, muli ndine,
ndodo ndiigwira.
5. Pamaso pa adaniwo
mwayala gome langa;
E, mutu mwaudzoza,
chisefuka chikho changa.
6. Zabwino ndi zokoma
zinditsata chitsatire;
E, m'nyumba ya Yehova
ndidzakhala chikhalire.

## 14

1. MTIMA wanga lemekeza
Mlungu wako ndi Chimwemwe.
Nthaŵi zonse ndimtamanda;
Ndimwimbira nyimbo zanga.
Moyo, mphamvu, nzeru zonse,
Zidzamlekeza konse.
2. Ndi wamwayi munthu uja
Amthandiza Mbuye wake
Akachita mantha iye
Amchotsera nkhaŵa yake,
Ndipo likamgwera tsoka
Amakhulupira kokha.
3. Mbuye ndiye wachifundo,
Achiritsa akudwala;
Anyamula akufoka
Naŵadyetsatu anjala.
Wakusunga mlendo ndiye,
Nathandiza amasiye.
4. Ndiye Mbuye wa ambuye;
Mphamvu yake ndi yokwana.
Adzakhala chikhalire,
Mfumu yathu yopambana,
Aleluya! Kondwerani!
Mlungu wathu yamikani!

## 15

1. MULUNGU ndiye Mbusa wanga,
sindisoŵa konse;
Amandiŵeta nandidyetsa
nandipatsa zonse.
*(Ndiye Mbusa wanga,*
*Ndiye Mbusa wanga!*
*Mulungu ndiye Mbusa wanga,*
*Sindisoŵa konse)*
2. M'mitsinje yamtendere mtima
wanga aumwetsa;
Mapazi omwe m'njira
Yolungama nayendetsa.
3. Za m'mdima, imfa, nkhondo ndi zoipa
sindiopa;
Ndikakhumudwa ndi kutopa,
Andipulumutsa.
4. Podwala ine pobvutidwa
Andisamalira;
Pondisauts' adani anga
nandithangatira.
5. Chisomo ndi zokoma zake
sizileka konse;
Ndi m'nyumba ya Mulungu
Ndidzakhala nsiku zonse.

## 16

1. ZOBVUTA zoopsya ndi zosaukazi
Sitingathe ife kuzithaŵa tokha.
Koma Ambuyathu timtamande Iye,
Uthenga Wabwino timveretu kokha.
2. Amadyetsa iye mbalame
zam'mwamba,
Timtamande ndithu potisunga ife;
Timvere malembo a m'kalata mwake,
Ambuye yemweyo atisungirabe.
3. Abramu kalelo anamvera bwino;
Timverenso ngatitu yemwe wakale.
Pokhala alendo atsogoza iwo,
Timkhulupirire Ambuye tonsefe.
6
4. Timtamande Iye ndi moyo wathunso
Pakutsatatsata malembedwe awo.
Tipezamo malembedwe awo.

Tipezamo malo okwanira ife
Ambuye wathu atipatsa kwawo.

## 17

1. POKONDWA ndi poona bvuto
Ndi tsoka pena mwayi,
Ndikumbukira, ndiimbira
Mulungu wangayo.
2. Kwezani nane Ambuyathu,
Timlemekeze yekha;
Popsinja mtima ndinamtchula,
Nandithangata 'ne
3. ANGELO amazinga nyumba
Za anthu olungama;
Mulungu ateteza omwe
Amkhulupirira.
4. Laŵani chikondano chake;
Mudzadziŵitsa msanga
Kudala kwawo kwa anake
Omkonda Mbuyeyo.
5. Opani iye, nimuleke
Kuopa kanthu kena;
Mumtumikire mokondwera,
Akusungani 'nu.
6. Mulungu wathu Mmodzi yekha
Atate, Mwana, Mzimu,
Akhale ndi ulemerero
Wachikhalirewo!

## 18

1. KUZANI Mlungu m'Mwambamo,
Mtamande m'kuyanso;
Nzozizwa nkhani zakezo,
Njolimba ntchito njo!
2. Pochimwa anthu onsewo
Nja Mlungu nzeruyi;
Adamu wachiŵiriyo
Wathetsa tchimoli.
3. Thupi la mwazi wathu 'li
Lochimwa kalelo,
Labweranso ku nkhondoyi,
Laposa monsemo.
4. Choposa nalo thupilo
Chikhale momwemu,
Chiyeretsetsa m'katimo,
Ndi Mulungu Iyeyu.
5. Anatikondakonda 'Ye,
Ndi Mlungu Iyeyo,
Anatifera anthu 'fe
Ndi Mulungu Iyenso.
6. Ndi m'munda muja chete, phee!
Pamtanda pati njo!
Anaphunzitsa 'bale 'fe
Titero ifenso.
7. Kuuzani Mlungu m'Mwambamo
Mtamande m'kuyanso;
Nzozizwa nkhani zakezo,
Njolimba ntchito njo!

## 19

1. KALELO anthu onse
Nachimwa kwa Mulungu
Mulungu anaona
Naona tchimo lawo,
Nafuna kwawononga,
Nafuna kwawononga.
2. Mulungu anatuma,
Natuma mvula ija,
Nadzaza dziko lonse
Anafa anthu onse,
Anafa m'mvula muja,
Anafa m'mvula muja.
3. Mulungu anatuma,
Natuma Nowa uja,
Wamanga chombo chake,
Ndi chachitalitali,
Nowayo nayendamo,
Nowayo nayendamo.
4. Nowayo anatuma,
Natuma chikwangwala,
Chatsika pansi pansi,
Chosabwerera konse,
7
Chithaŵa m'talitali,
Chithaŵa m'talitali.
5. Kutuma wabwereza,
Natuma nkhunda ija,
Yatsika pamadzipo,
Yathyolatu mayani,
Yampatsa Nowa yemwe,
Yampatsa Nowa yemwe.
6. Kalelo Mbuye Yesu
'Nafera anthu onse,

Ndiyeyo chombo chathu,
Tikabisala mommo
Tipulumuka mommo,
Tipulumuka mommo.

## 20

1. MULUNGU aŵakonda anthu
Ali pansi pano;
Afuna kuŵapulumutsa
Kumilandu yawo.
*A! Chikondi chachikulu*
*Mulungu ali nacho,*
*Chimam'tengera Mpulumutsi,*
*Andifere pano*
2. Ndikhulupira mwa Ambuye,
Mulungu namukitsa,
Imfayo indipulumutsa,
Mwazi und'yeretsa.
3. Chikondi chake chindidzera
M'mtima mwanga muno,
Chipulumutsa nditalema
Ndi machimo anga.
4. Mukondwe anthu a Mulungu,
Tere mulandira
Chimwemwe chija chakumwamba,
Chidzaloŵa m'mtima.
5. Mulungu atipatsa mphamvu
Yoletsetsa tchimo;
Pofika tsikulo la imfa,
Tidzakhala bwino.

## 21

1. TIIMBE nyimbo zotamanda
Mulungu wathu wabwino,
Pakuti akondana nawo
Anthu okhala padziko;
Tero natuma Mwana wake,
Wakukondedwa kalelo,
Kutiphunzitsa ife tonse
Za chikondano chakecho.
2. Mulungu ndiye wachifundo,
Nadzalandira onsewa
Akuulula mphulupulu
Ndi kukondana ndi Yesu
Tilondelonde njira yake
Yopapatiza yaing'ono;
Adzatilondolera ndiye
Kutifikitsa m'Mwambamo.
3. Pakuwoloka mtsinje wa imfa
Dzanja Mbuyathu agwira;
Tikadagwira ntchito zake
Atipatsatu korona;
Komwe kulibe masauko,
Pena misozi maliro;
Mulungu tidzamtamandira,
Inde kosalekezanso.

## 22

1. NDIKONDA Mlungu pomva
Mbuye wanga
Amva pemphero ndi kulira kwanga,
Namachereza khutu nditapfuula,
Andithandiza, nandipulumutsa.
2. Mulungu wanga ndiye wachifundo
Ndi wolungama mtima ndi wabwino;
Apulumutsa anthu akufoka,
Akathandiza nkhaŵa imachoka.
3. Mtimanga, bwera kuti upumule,
Wakuchitiranso zokoma Mbuye,
Wakuchotsera imfa ndi misozi,
Ndingakhumudwe asungira phazi.
4. Nditani ine kubwezera Mbuye
Zokoma zonse anandichitira?
Chipulumutso chake ndidzatama,
Ndinalumbira zija ndidzapatsa.
5. Imfa ya anthu ake imkomera,
Aŵalandira m'nyumba zokonzeka.
8
Mbuye, kapolo wanu ndipereka
Nsembeyi yonga yanu, ndine ndekha.

## 23

1. TITAME Mlungu Wakumwamba,
Timwimbire nyimbo,
Kukoma kwake kwatipatsa
Zonse tili nazo.
*(Timwimbire nyimbo,*
*Timwimbire nyimbo!*
*Kukoma kwake kwatipatsa*
*Zonse tili nazo)*
2. Poyamba paja analenga
Zonse dziko muno,
Tsopano lomwe azisunga
Zonse zili moyo.

3. Tinasokera ngati nkhosa,
Moyo tinataya,
Tinakondwera ndi zoipa
Zonse tinatsata.
4. Komweko titasaukira,
Titafuna kufa,
Atate anatilondola
Naitana ife.
5. Tiyeni tizipita kwathu,
Tisasokerenso,
Tilape m'mtima kuti
tikakhale ndi Mulungu.

# 24

1. OONADI mtima,
'Dzani mokondwera,
Tiyeni, tiyeni ku Betlehemu;
Modyera ng'ombe
Muli Mfumu yathu.
*Tiyeni timgwadire*
*Khristuyo.*
2. Mulungu wamkulu
Wakuyerayera
Kubadwa mwamkazi sanakana 'yi;
Mwana wa 'Tate,
Sanalengedwadi.
3. Angelo kwezani
Nyimbo zanu zonse,
M'wambamo mumveke zoyamikazo;
Lemekezani
Mulungu Wakumwamba.
4. M'dzikomo Ambuye
Mnabadwira ife,
Ulemu wosatha muyeneradi.
Mawu a 'Tate,
Munalowâ m'thupi.

# 25

1. NDIKULEMEKEZA
Ambuye Mpulumutsi wanga;
Moyo ndi mtima wanga
ndilikukondwa mwa Mulungu.
2. Ndiye anayang'ana
umphaŵi wa mdzakazi wake;
Onse adzandiyesa
ine wodala nsiku zonse.
3. Ndiye wamphamvu zonse
anandichitira zazikulu;
Dzina la Ambuyanga
lili loyera kopambana.
4. Ndiye amachitira
chifundo anthu a mibadwo,
E! a mibadwo yonse
yakumuopa ndi kummvera.
5. Iye amazichita
zamphamvu nawo mkono wake;
Iye nabalalitsa
omwe anyada nadzitama
6. Iye natsitsa kunsi
mafumu ku mipando yawo.
Iye nakweza konko
omwe afatsa nasauka.
7. Ife amakhutitsa
anjala ndi zabwino zake,
Ndi olemera onse
naŵaingits' opanda kanthu.
8. Monga anapangana
ponena kwa makolo athu,
9
Ali kuthandizadi
lero anake a Yakobo,
9. Poti akumbukira
atate wathu Abrahamu;
Inde chifundo chokha
akuchitira ana ake.

# 26

1. AMITHENGA a Mulungu
Anaimba nyimbo yomwe,
Posonkhana m'mlengalenga,
Natitu usiku womwe;
"Onse azilemekeza
Mlungu Wakumwambamwamba;
Akhalebe ndi mtendere
Anthu ali ponseponse."
*Amithenga anaimba*
*Ndi usiku m'mlengalenga.*
2. Anamva abusa omwe
Anaŵeta nkhosa zawo.
Mthenga nati: "Musaope;
Mumve ndikufotokoza:
Wabadwa usiku uno
Yesu Kristu Ambuyathu

Ndiye Mpulumutsi wathu;
Anabadwa m'Betlehemu."
*Amithenga anaimba*
*Ndi usiku m'mlengalenga.*
3. Yesu ndinu Mbuye wathu,
Munasiya za Kumwamba;
Munakhala mwana kuno;
Mnatifera mwaufulu.
Inu nonse amithenga,
Inu mumtamande Iye;
Anthu onse ali pansi
Adza akondane naye.
*Zoonazi amithenga*
*Anaimba m'mlengalenga.*

# 27

1. AMBUYE ngwodalitsika,
Mulungu wa Israyeli ndiye,
Poti anayang'ana
naŵawombola anthu ake,
2. Napulumutsa tonse
mwapfuko la Davide mwana wake;
Monga analankhula
mwa aneneri ake, kuti
3. Adzatipulumutsa
kudzanja la onse akutida,
Ndipo adzachitira
akulu chifundo ndi chisoni.
4. Ndiye akumbukira
pangani loyera lake lija,
Ndi chilumbiro chake
cha kwa atate Abrahamu,
5. Choti timtumikire
osaŵaopa 'dani athu,
Ndi kuyeranso mtima
mwa chilungamo nsiku zonse.
6. Mwana, adzakuyesa
mneneritu wa Wamkulukulu,
Ndiwe udzakonzera
njira ya Mbuye Wakumwamba.
7. Udzadziŵitsa anthu
za Mpulumutsi wawo yemwe
Aŵakhulululukira
Nafafaniza tchimo lawo,
8. Poti Mulungu wathu
ali ndi mtima wachifundo.
Ndiye kumwamba komwe
Ationetsa mbanda kucha,
9. Poŵalitsira omwe
ali mumdima ndi muimfa,
Ndi potilunjikitsa
tonse munjira yamtendere.

# 28

1. AMBUYE tsopano lino,
monga mwa mawu anu aja,
Lolani kapolo wanu
ndikachokere mumtendere;
2. Chifukwa chipulumutso
chanu mwandionetsa zedi,
Chimene munachikonza
akachione anthu onse;
3. Ndi nyali yakuŵalitsa
10
omwe sadziŵa mawu anu;
Ndiwo ulemerero
wa Israyeli mpingo wanu.

# 29

1. M'KATI mwa zobvuta zathu
Yesu aitana ife,
Tsiku lonse amanena:
"Tsata Ine mkristu iwe."
2. Kale ophunzira ake
Namvanso kunyanja kwawo,
Zinthu zonse anasiya
Kukatsata Mbuye wawo.
3. Yesu aitana ife;
Tikakonda chuma chokha,
Ati Yesu; "Mwana wanga,
Undikondetu koposa."
4. Mwachimwemwe, mwachisoni,
Pogwiritsa ntchito zonse,
Aitana Mpulumutsi
Kuti tizimkonda tonse.
5. Yesu aitana ife;
Mbuye, mutimvetse ndithu,
Tipereke mtima wathu,
Tikondane lero ndithu.

# 30

1. IFE timakufunani
Inu wotonthoza mtima.

Yesu, nyimbo zathu zonse
Ziyamika Inu nokha.
Munasiya zonse m'Mwamba,
Kudzakhala pansi pano
Kuwombola akapolo,
Kumasula anthu anu.
2. Yesu, ndi chifundo chanu
Chachikulu munadzera
Ife anthu osauka,
Tsoka lathu mnachotsera.
Mwazi ndi misozi yanu
Munakhetsa m'munda muja,
Kukonzera ife njira
Yonkako Kumwamba kuja.
3. Yesu munalaswa m'mtima,
Ndi zonyoza munafoka,
Mnasenzera anthu mkwiyo
Wa Atate, Inu nokha.
Chikho chija ndi choopsa
Munamwacho m'phiri lija
M'mene munalola mtanda,
E! chifundo chanu chinja.
4. Yesu ndinu moyo wathu,
Chuma chathu choposetsa.
E! tikondwerera mtanda,
Apo moyo munapatsa.
Mbuye tikondana nanu,
Yesu Mbuye Mwini zonse;
Ndi mitima ndi milomo,
Tikuyamikani tonse.

# 31

1. "SENZANI mtanda wanuwu."
Atero Yesu Mbuyathu;
"Mukanditsata Inetu,
Mudzikanize nokhanu."
2. "Senzani mtanda wanuwu."
Musaopsedwe nawotu;
Mphamvu za Yesu nzanunso;
Limba mtima wanuwo.
3. "Senzani mtanda wanuwu."
Bwanji manyazi mumva 'nu?
Yesu anapiriratu,
Kuti mupulumuketu.
4. "Senzani mtanda wanuwu."
Nawo muyende chetetu,
Mutsogoledwe nawonso
Kwanu Kumwamba komweko.
5. "Senzani mtanda wanuwu."
Tsatani Yesu m'njiramu;
Iye wakusalemayo
Ndiye alandiridwadi.

# 32

1. MUNTHU wacisoniyo
… .....dzina lakelo,
Mpulumutsi linanso;
Alleluia, ndiye Yesu.
2. Anapeputaidwako,
Nandifera m'mtandamo,
Anandowombolayo;
Aleluya ndiye yesu
3. Ife tinacimwadi,
Iye sanachimwa ayi,
Anachotsa chimoli,
Aleluya, ndiye Yesu.
4. Anapachikidwathu
Watha nchito yake……
Azakwera m'mwamba……
Aleluya, ndiye Yesu.
5. Azdabwera Iyenso
Kudzatenga okhawo;
Nyimbo tidzakaimbanso,
Aleluya ndiye Yesu.

# 33

1. Unakhetsedwa mwazi dol
Wa Yesu Mfumuyo,
Poweramira mutuwo
Pamtanda pakepo.

*Mbuye mthandiza inetu*
*Kukonda inidi,*
*Ndi kuli mpando wanuwo*

*Ndufuna kuzdako.*

2. Zochimwa zanga zonsezo
Anaziferadi,
Chikondi chake chonsecho
Sindingadziwe ayi.
3. Linadetsadi dzuwa bii,
Pakufa iyeyo
Pakumwalira indedi
Wakundilengayo.
4. Pokumbukira mtandawo
Wa mpulumutsiyu,
Ndiphimba nkhope yangayi,
Ndi nsoni n'chitatu.
5. Zofuna zanga zosenzo
Za mutima wangawu
Ndipereka kwa inu,
Mundiweruzetu.

# 34

1. KU Mzinda wakuyerawo
Wapachikidwa Mbuyeyo,
Nasautsidwa Mbuyeyo,



Akatipulumutsa 'fe.
2. Padzanja lachifundolo
Linapenyetsetsa 'khunguwo,
Lachiza nalo nthendazo,
Papyolatu msomaliwo.
3. Mapazi ake namvatu
Zoŵaŵa zopambanazo,
Napachikidwa kaamba ka
Zoipa zathu zonsezi.
4. Ambuye, tikondweratu
Kupulumutsa kwanuko;
Satana tisammvere 'yi
Komabe Mpulumutsiyo.

# 35

1. TIYENI, dzalireni nane,
Tidze ku mtanda wa Ambuye,
Tionse tichitetu maliro;
Wapachikidwa Ambuyathu.
2. Kodi misozi itisoŵa,
Poona anthu amanyoza?
Onani umo apirira;
Wapachikidwa Ambuyathu.
3. Anena mawu m'mtanda momwe
Mawu ochepa achifundo,
Apempherera 'dani ake;
Wapachikidwa Ambuyathu.
4. Mtima wangawe, uyenera
Kuduka ndi manyazi lero,
Zamlasa ndi zoipa zako;
Wapachikidwa Ambuyathu.
5. Ona chikondi cha Mulungu,
Ona zoipazo za anthu,
Koma chakula ndi chikondi;
Wapachikidwa Ambuyathu.

# 36

1. PAMTANDAPO Ambuyeyo
Anatifera ifetu,
Nakhetsa mwazi wakewo
Kutiwombola tonsefe.
*Pamtandapo, pamtandapo*
*Ambuye wanga 'nafatu;*
*Pamtandapo, pamtandapo*
*Anandiwombolerapo.*
2. Kwa munthu wosokerayo
Kudziko lakutaliko,
Atero Yesu: "Bweratu
Ukhale nawo moyowo."
3. E! Yesu Mbuye wangadi,
Ndipatsa Inu mtimawu;
Ndithandizeni inedi
Ndisalekane nanu 'yi.
4. Zochimwa zanga zonsezo
Wandichotsera mwaziwo;
Mumtima mwanga muli mbee!
Mwayeretsedwa indetu.

# 37

1. ZATHEDWA zonsetu
Za moyo wakewo,
Ambuye anatsikayo
Nafika pansipa.
2. Zintchito zakezi
Zofuna 'Tatewo
Anatsiriza zonsedi,
Sanazisiya 'yi.

3. Pa Iye padzapo
Chisoni m'mtimamo,
Mpweteko wonse wathuwo
Wa dziko lonseli.
4. Pamutu minga kwe!
Pamoyo wakewo
Zoipa zathu zonsezo,
Zinaikidwapo.
5. Anandiferatu 'Ye,
Afera inedi;
Athetsa nsembe zonsezi
Ambuye Nsembeyi.
6. Pakugomedwapo Pa
mlandu wangawo,
Ndidzaitana Mbuyeyo
Andilanditsepo.


## 38

1. A! MUTU wakuyera,
Wolaswa wachisoni,
Abveka Inu anthu
Ndi minga ya udani;
Ambuye mwafokatu
Ndi masauko aja,
Mwatuŵa m'maso mwanu
Mumayerera kale.
2. Ambuye Mwini moyo,
Kokoma mnafumako;
Ndizizwa pomva mawu
Umo mwachitiramo.
Chisoni chija chanu
Ncha pamachimo anga,
Mwasaukira Inu
Kupalamula kwanga.
3. Nditani! Bwezi langa
Kulemekeza Inu
Chifukwa cha chifundo
Ndi imfa ija yanu?
Mundikhalitse wanu,
Wokhulupira inu;
Musandilole konse
Kufulatira Inu.
4. Pakufa ine Mbuye
Mukhaletu pafupi,
Mundithandize ine,
E, mudzandimasula;
Ndipenyetsetsa Yesu,
Ambuye Mfumu yanga,
Ndikafa ndine wanu,
Ndikhale nanu m'Mwamba.

## 39

1. POKUMBUKIRA mtandawo
Ambuye 'nandiferapo,
Ndiyesa zingochepazo
Ndinazitama kalelo.
2. Mndiletse ndisatame'yi
Zachabe, koma imfayi;
Zijazo ndinakondazo
Ndazilekera mwaziwo.
3. Onani m'mutu, m'manjawo
Mudzera nsoni m'mwazimo.
A! panalibe kalelo
Wondibvalira mingayo.
4. Chinkana dziko lonselo
Lichepa ndithu mtulowo,
Chikondicho chagwirabe
Mtimanga, moyo, ndense 'ne.

## 40

1. LERO Kristu anauka, Aleluya.
Ndilo tsiku lokondwera. Aleluya.
Iye kale anafera, Aleluya.
Nawombola otaika Aleluya.
2. Timwimbire zomtamanda Aleluya.
Ndiye Kristu wa Kumwamba
Aleluya.
Natsikira kumanda, Aleluya.
Nalanditsa akuipa. Aleluya
3. Koma masauko ake Aleluya.
Anatiwombola ife. Aleluya.
Ndiye Mfumu ya mafumu Aleluya.
Mwana ndithu wa Mulungu.
Aleluya.
4. Timwimbire Mulungu wathu,
Aleluya.
Kuti atikonda ndithu: Aleluya.
Mtamenso angelo inu, Aleluya.
Ndiye 'Tate, Mwana, Mzimu
Aleluya.

## 41

1. NLA Mlungu dzuŵali:
Pa mbanda kuchapo
Angelo ‘nadzatu
Nachotsa mwalawo.
*Ndi mtima wonse mwimbedi,*
*Wauka Mbuye leroli.*
2. Akonda onsewo
‘Nagwidwa manthadi
Poona zo’psyazo
Zoonekerazi.
3. Mulibe m’mandamu,
Wadzuka Mbuyetu;
Woposa imfayo

Ndi Mwini moyowu.
4. Dzukani nayetu,
Oyera inunso,
Lekani m’mandamo
Zakufa zanuzo.
5. Titama Yesuyo,
Ambuye m’Mwambamo,
Wofera anthu ’Ye,
Timkondakondako.

## 42

*ALELUYA, Aleluya, Aleluya!*
1. Nkhondoyo yatha, imfa yagonja,
Yesu wamoyo anaiposa,
Msampha woipa wonse nawonja,
Aleluya!
2. Mphamvu za imfa ndi za Satana
Naye Ambuye zinalimbana,
Komatu Yesu anapambana.
Aleluya!
3. Atha masiku aja ansoni,
Mbuye wauka, ali ndi mboni;
Lero chimwemwe, chatha chisoni,
Aleluya!
4. Nsinga za imfa Iye ’nadula,
Khomo la m’Mwamba, nalitsegula;
Yesu timtama tonse tipfuula,
Aleluya!
5. Mbuye mabala anu olimba
Atichotsera mantha a imfa;
Tsono ndi mtima wonse tiiimba:
Aleluya!

## 43

1. KONDWERANI dzuŵa lino,
Aleluya.
Yesu wanka m’Mwamba momwe:
Aleluya.
Wachokera m’dziko lino, Aleluya.
Wabwerera kwawo komwe. Aleluya.
2. Zomkwezetsa zili m’Mwamba,
Aleluya.
Zodikira Mbuye wathu; Aleluya.
Mloŵetseni n’kumlambira, Aleluya.
Mfumu yathu yaulemu. Aleluya.
3. Yesu nkana saoneka, Aleluya
Atipempherera komwe: Aleluya.
M’nyumba yake yokonzeka Aleluya.
Atilinda ife tomwe Aleluya.
4. Tiyamike Dzina lake, Aleluya.
Mfumu ya ulemu wonse. Aleluya.
Tibukitse mbiri yake Aleluya.
Pansipa padziko lonse. Aleluya.

## 44

1. LAMBIRA, Mfumuyo,
Ndi Yesu Mbuyathu,
Tamvani nyimbo za ‘mithenga a
Kumwambako;
Nafenso pansipa
Timyamikire ’Yo,
Ndi Mpulumutsi wathu wotifera
kalelo.
2. Lambira Yesuyo
Wokonda tonsefe;
Mabala ake achikondi aonekabe;
Tisaiwale ’yi
Zoŵaŵa zakezo,
Tileke kumchimwira, kumsautsa
Yesuyo.
3. Lambira Yesuyo,
Uthenga wakewu
Uyanjanitsa anthu onse m’dziko
munomo:
Amaiŵala za
Kudana kwawoko,
Nayamikira Mfumu yamtendere
monsemo.
4. Lambira Mfumuyo

Wolenga zonsezi:
Nyenyezi, dziko, dzuŵa, mwezi ndi mitamboyi;
Tikweze dzinalo
La Mbuye Yesuyo,
Timyamikire pansi pano ndi
Kumwambako.

## 45

1. YESU wakukoma mtima,
Akondadi!

Wakuposa mbale ndiye,
Akondadi!
Wina asautsa iwe,
Pena adzasiya iwe,
Yesu sadzanyenga iwe,
Akondadi!
2. Kumdziŵitsa ndiko moyo,
Akondadi!
Akhumbira mtima wako,
Akondadi
Mwazi wake ngwowombola,
M'chipululu akufuna,
M'khola mwake akusunga,
Akondadi!
3. Akufuna kumdziŵitsa,
Akondadi!
Udzimpatsa moyo wako,
Akondadi!
Kodi umachita mantha?
Pena umadera nkhaŵa?
Yesu amasangalatsa,
Akondadi!
4. Bwenzi ndiye wakufera,
Akondadi!
Nthaŵi zonse sakusiya,
Akondadi!
Anthu ena akunyenga,
Yesu sadzanyenga iwe,
Zakubvuta adzachotsa,
Akondadi!
5. Akhululukira iwe,
Akondadi!
Nadzainga mdani wako,
Akondadi!
Adzakudalitsa iwe,
Nadzaletsa tsoka lonse,
Nadzakutsogoza kwawo,
Akondadi!

## 46

1. Msandipitirire, Yesu,
Mundimvere ine;
Mukudalitsa ena,
Msandipitirire.

*Yesu mbuye,*
*Khutu munditchere*
*M'mene muitana ena*
*Msandipitirire.*

2. Ndigwadira inu, Yesu,
Musandikanize;
Ndizalapatu machismo
Mbuye mndithandize
3. Nkhope yanu ndifunitsa
Sind'yenera konse;
M'mtima mwanga muchiritse
Nthenda zanga zones.
4. Yesu ndinutu chitsime cha
chimwemwe chokha,
Sindifuna wina konse,
Koma inu nokha.

## 47

1. Idza wolema,
Akupumitsa;
Womva chisoni,
Akutonthoza;
Mulendo limbika,
Mphamvu apatsa
Amtisunga, yesu ambuye.
2. Ndiye mtsamiro
Pogona ine;
Pofika kufa
Andidzutsanso;
Podzichepetsa;
Andikwedzanso;
Moyo wa moyo,
Yesu abuye.

3. Ndikakhumudwa
Andilimbitsa;
Ndikadzitama;
Andichepetsa;
Ndikasokera;
Andilondola;
E! wokondedwa
Yesu Ambuye.

4. Ndimachitira
Inu umboni
Ndikukuzani
Moyamikira;
Mphamvu ndi nzeru
Moyo, zonsezi,
Si zanga, nzanu,
Yesu ambuye.

## 48

1. MBUYE , mutsaganetu
Nane ndingachimwenso;
Nanu ndisungidwedi,
Mwa chikondi chanucho.
*Mbuye Yesu,*
*Mundiperekeze inetu;*
*Ndine mlendo, Mbuye 'Nu,*
*Mutsagane nanetu*
2. Inu mundibisadi
M'mene ndabvutidwamo,
Ngati muli ndinedi
Bwino ndidzakhalamo.
3. Mbuye, mutsaganebe
Mpaka moyo watha zi!
Kwanu mundifitseko,
Kwanu nsoni zathadi.

## 49

1. E, MOYO wanga'we
Utsitsimuketu;
Ambuye Yesuyo
Akhala m'Mwambamo.
Pampandopo
Akhalabe, natchula dzina langali.
2. Kwa Mlungu m'Mwambamo
Amapempherako;
Chikondi chakenso
Chikhala chosatha;
Ndi mwaziwo
Akhalatu Wansembe wanga Yesuyo.
3. Mabala ajawo
A m'thupi mwakemo
Amukumbutsanso Za
ine pansipa;
Zoipazo
Achotsadi kotero sindingafe 'yi
4. Mulungu ali wokhulula
mtimatu,
Ndilibe mantha 'yi,
Andisungiradi;
Ndibwera kwa
Atatewo, titayanjana leroli.

## 50

1. M'KHOLA mwa ng'ombe ku
Betlehemu
Anabadwamo Ambuyangayo;
Etu, ndizizwa! natsikirako,
Kufuna inetu.
*Kufuna inetu, kufuna inetu,*

*Etu ndizizwa! Natsikirako*
*Kufuna inetu.*
2. Popachikidwa pa Golgotapo
Yesu anandiwombola ine,
Etu, ndidziŵa! Nakondetsadi
Nafera inetu.
*Nafera inetu, nafera inetu,*
*Etu ndizizwa! Nakondetsadi*
*Nafera inetu.*
3. Mbusa wokoma ndi Mbuyangayo,
Nandiitana posokerapo,
Konse koipa nalondolako
Kubweza inetu.
*Kubweza inetu, kubweza inetu,*
*Konse koipa nalondolako*
*Kubweza inetu.*
4. Uko kumwambako Mbuyangayo
Andikonzera mokhaliramo;
Tsiku linalo adzabweranso
Kutenga inetu.
*Kutenga inetu, kutenga inetu,*
*Tsiku linalo adzabweranso*

*Kutenga inetu.*

## 51

1. Alinkuza wansoni munthu
Wakukhala kumwamba,
Alinkudza m'ulemelero
Ndi mwamuna wa mtanda.

*Aleluya, aluluya*
*Alinkudza kwa ife;*
*Ndi chimwemwe ……………..*
*Pakufika Ambuye.*

2. Alinkudza Ambuye Yesu
Wakuphedwa pa dziko,
Alinkudza kukhala mfumu
Yoweruza maiko.

3. Pakufika asonkhanitsa
Anthu ake oyera;
Adzafuna m'mitundu yonse
Omwe iye anafera.

## 52

1. PAKWITANA Mbuye wanga
Potsiriza dzikoli,
Pakufika tsiku la kuŵalalo,
Posonkhana akumvera,
Pakuona Yesuyo,
Ndidzakondwerera naye komweko.
*Pakwitana Mbuye wanga,*
*Pakwitana Mbuye wanga,*
*Pakwitana Mbuye wanga,*
*Ndidzakondwerera naye komweko.*
2. Potuluka m'manda mwawo
Anthu ake onsewo,
Tidzasanganatu nawo nthaŵiyo.
Pakuuka osankhidwa,
Kunka naye Yesuyo,
Ndidzakondwerera naye komweko.
3. Tisaleke kugwirabe
Ntchito ya Mulunguyo,
Tibukitse mbiri yake m'dzikoli,
Ndi podzatha moyo wathu
Ndi zintchito zathuzo,
Tidzakondwerera naye komweko.

## 53

1. MBUYE Yesu adzabwera,
Asekere anthu onse;
Mawu awa achimwemwe
Azimveka m'dziko lonse.
Adzabwera, adzabwera;
E! bwerani Mbuye wathu.
2. Dziko lino linaona
Masauko a Mbuyathu,
Lidzaonanso ulemu,
M'mene adzabwera Iye.
Adzabwera, adzabwera;
Timvomera, E! mubwere
3. Anthu anu amafoka,
Pa ulendo nasokera;
Ha! Adzaonana nanu
Atabvalanso zoyera.
Mudzabwera, mudzabwera;
Inde Mbuyetu mubwere.
4. Ndi chiyembekezo ichi
Sitikhala chete ife:
Tiimbitsa nyimbo zathu
Zakulemekeza Mlungu.
Adzabwera, adzabwera
E!! mubwere msanga YESU.

## 54

1. YANG'ANANI, anthu onse,
Yesu Mbuye wathuyo:
Alinkudza ndi ulemu,
Kuoneka m'Mwambamo.
*Anthu onse amlambire*
*Yesu Mwana wa Mulungu*
*Alinkudza ndi ulemu*
*Wopambana, indetu.*
2. Adzatenga anthu ake
Akumvera pansipo
Iwo adzakhala naye

M'dziko la Kumwambako.
3. Koma anthu onse omwe
Anamnyoza pansipo,
Nthaŵi Yesu alinkudza
Adzaopa m'mtimamo.
4. Ife tonse tikumbuke
Mawu ake onsewo;
Timuyang'anire Iye,

Yesu Mbuye wathuyo.

## 55

1. *A MULUNGU,*
Munatuma Yesuyo,
Mwana wanu Yekhayo.
2. *Anabadwa,*
Anabadwa motere,
Monga mmphaŵi m'kholamo.
3. *Anakonda*
Anakonda anthuwo,
Naŵapulumutsanso.
4. *Anafera,*
Anafera m'mtandamo,
Anafera ifenso.
5. *Anadzuka*
Anadzuka m'mandamo,
Anatenga moyowo.
6. *Anakwera,*
Anakwera m'Mwambamo
Kwa Mulungu 'Tatewo.
7. *Adzabwera,*
Adzabwera Iyeyo
Tsiku lomalizalo.
8. *Aleluya,*
Aleluya Yesuyo,
Tizitama dzinalo.

## 56

1. IDZANI nonse 'nu
Okonda Yesuyo;
Libuke Dzinali,
Timtame konseko.
Uzani onse m'Mwambamo,
Uzani onse pansipa,
Wafera Iye anthuwo.
2. Waleka kronayo,
Nasiya 'Tatewo,
Natsika m'Mwambamo,
Nalira, nafatu.
Zoŵaŵa zake zonsezo
Nazimva, zinaposatu
Kuti tipulumukedi.
3. Nadzuka m'mandamo
Moopsya m'mdimamo,
Nigonja imfayo
Ndi mdani waketu;
Nakweradi Kumwambako,
Nakhala Mfumu monsemo,
Ambuye wathu Mlunguyo.
4. Adzadza indetu
Kudziko linoli;
Tidzanka nayeyu
M'ufumu wakedi.
Momwemo tidzampenya 'Ye,
Momwemo tidzakhala 'fe
M'kuŵala kwake koti mbee!

## 57

1. Yesu, dzina lakukonda,
Lopambana onse ena,
Tonse tidzaligwadira
Ndi mitima yochepetsa.
2. Yesu, dzina lokondwetsa
Akuipa a padziko,
Kale linatidziŵitsa
Mpulumutsi ndiye Yesu.
3. Yesu dzina lakufatsa,
Anamutcha 'kali Mwana,
M'mene analoŵa kale
M'dziko lino lakudana.
4. Yesu, dzina ndi lomweli
La pa dziko lino lonse,
Ndi lamphamvu yolanditsa
Anthu mu masoka onse.
5. Yesu, dzina lakukonda

La Mwanayo wa Mulungu,
Ife anthu osauka
Tithaŵira nalo kwanu.

## 58

1. Inde ndifuna kumvatu
Za chikondano chakecho
Cha Yesu mbuye wangayo
Zomwe anmva kalelo.

*E! zina za Yesu*
*E! zina za Yesu*
*Inde, ndirira m'mtima*
*Chipulumutso chakecho*

2. Zina za Yesu Ndimvetu,
Kuti ndichite zakezo;

Mzimu woyera, mudzetu
Ndiphunzitseni zonsezo.
3. M'mawu a Yesu mbuyeyo,
Inde, acheza nanemo;
Liu ndimamva m'bukumo
Ndilo la Yesu Mbuyeyo.
4. Zina za Yesu m'mwambamo
Ali pampando pakepo;
Udze ufumu wakewo,
…………………………

## 59

1. Wina atikonda ife,
Bwenzi lathu ndiyeyu,
Atifunafuna ife,
Inde nthawi zonsetu.

*Chikondano chakechi*
*Nchachikulukuludi*

2. Ndani mwa abale athu
Angatifere ife?
Koma yesu m'malo mwathu
Anapachikidwatu
3. Anamnyoza pansi pano,
Bwenzi la ochimwawo;
Mu'ulemerero wake
Alizonda Dzinali.
4. Timchimwira kopambana,
Ndi kumsautsa iye,
Koma Bwenzi lathu Yesu
Atikondakondabe.
5. Mtiphunzitse, mbuye Yesu,
Tikondane nanutu;
Tisaiwalire konse
Bwenzi lathu ndinutu.

## 60

1. NDITAME Mlungu m'mtimamo,
Wakundifera pansipo,
Nafafaniza tchimolo,
Nanditengera dipolo
*Wandiwombola inetu*
*Pokhetsa nwazi wakewo;*
*Timlemekeza Iyetu*
*Wotilipira dipolo.*
*2.* Ndinasokera kalelo,
Ndamkana Iye Yesuyo,
Koma ndiimba leroli:
Wandiwombola inedi.
*3.* M'mtima ndimakondweramo
Popenyetsetsa Yesuyo
Pamtanda pake pomwepo,
Pakundifera inenso.
4. Sizitha ntchito zangazo
Kundiyeretsa m'mtimamo;
Anandiyesa inetu
Wakulungama Yesuyo.
5. Tsono mubwere inunso;
Mtetezi wanu ndiyedi.
Apulumusa onsewo
Akumkhulupiriradi.

## 61

1. Konda dzinalo la Yesu,
Mwana wosauka iwe;
Ndilo lothandiza anthu;
Khala nalo ponse phee.

*Dzina la Yesuyo*
*Nlokondetsa onsewo,*
*M'mwambamo, ponsepo*
*Litonthoza m'mtimamo.*

2. Konda dzinalo la Yesu
M'moyo mwakomo
M'mene ulikuyesedwa,
Tchula Dzina lakelo.
3. Dzina ili ndi lokoma
La mtetezi wathuwo;
M'mene adzatilandira
M'mwamba, tidzakondwa.
4. Mbuye Yesu timtamanda
Ndi nyimbo zathuzo;
Mfumu ya ma mfumu onse
Yesu timavesadi.

## 62

1. KHAMULO liliko
Kumwambako mbuu!
Pakukhala ndi Yesu

Aimbirako:
*“Kwa Iye atikonda*
*Natsuka ’fe mbuu!*
*E! kukhale ulemu*
*Kwa Mbuyathuyu.”*
2. Onsewa ’nachimwa
Nadetsedwa bii,
Nthaŵi yino ayera
Naimbiradi:
3. Akhala mafumu
Kwa Mbuyathuyo,
Anawombola onse
Ndi mwaziwo pyu!
4. Akadakhalabe
Osaukako
Ngati Yesu sakana-
Wombolatuwo.
5. Ndi nyimbo yabwino
Tidzamtamako,
Kuti ena pakumva
Amwimbirenso:
*“Kwa Iye atikonda*
*Natsuka ’fe mbuu!*
*E! kukhale ulemu*
*Kwa Mbuyathuyu.”*

## 63

1. TAMANI mphamvu ya Yesu,
Angelo agwade;
Tulutsanitu korona,
*Mumbveke, mbveke, mbveke,*
*Mbveke Mbuyeyo!*
2. Inu osankhidwa ake,
Owomboledwa ’nu,
Tamani Mpulumutsiyo,
*Mumbveke, Mbveke, Mbveke,*
*Mbveke Mbuyeyo!*
3. Anthu onse ndi mitundu
Pa dziko linotu,
Amlemekeze Mfumuyo.
*Mumbveke, mbveke, mbveke,*
*Mbveke Mbuyeyo!*
4. Tifuna kuti komweko
Tikamgwadire ’Ye;
Tidzaimba kosaleka:
*Mumbveke, mbveke, mbveke,*
*Mbveke Mbuyeyo!*

## 64

1. MUBWERE Mzimu Wakuyera,
Kuyatsa moto m’mtima mwathu;
Ntchito ndi yanu kudzozera
18
Ndi kutininkha mphatsozo.
2. Kudzodza kwanu kutipatsa
Chimwemwe, moyo ndi mtendere;
Kuŵala kwanu kupenyetsa
A m’mdima ndi a m’ndendemo.
3. Mtima wodetsa mukonzere,
Chisomo chanu chakwanira;
Adani athu muthaŵitse
4. Mutidziŵitse ‘Tate wathu, Ndi
mwana wake ndinu Mmodzi.
Mnafuma kwa aŵiri onse,
Koma Mulungu Mmodziyo.

## 65

1. MZIMU Woyera, mudze mumitima mwathumo,
Mufike nazo mphamvu zanu zazikuluzo.
2. Mufike monga nyali younika m’mtimamo.
Mutidziŵitse zakuipa zakukhalamo.
3. Mufike monga moto wakuotcha zomwezo.
Mutiyeretse ifetu m’mitima mwathumo.
4. Mufike monga ngati njiŵa yamtenderewo.
Kutitu anthu anu onse akondanetu.
5. Mufike monga ngati mphepo yokokomayo,
Tikhale tonse nazo mphamvu zanu zonsezo.

## 66

1. MZIMU Woyera, mudzetu kwa ine
E, ngati mvula m’dziko lakuuma,
Ndikhale munda wanu wakupatsa
Zipatso zoyenera Mbuyeyo.
2. Mphunzitsi, ndinu mudziŵitse ine
Chikondi chanu chija chachikulu;
Lembani mawu anu pamtimanga,
Kuti ndikhumbukire zanuzo.

3. Wosangalatsa, ine ndikalira
Muchotse nsoni, m'mtimamo mudikhe;
Mundigoneke pachifuwa chake
Cha Yesu kuti ndikakondwepo.
4. Wotsogolera, munditsogolere
Kuti n'kafike kwawo kwa Atate,
Nditsate Yesu ndikuyendayenda
M'njira yomweyo anapondamo.
5. Mthandizi ndinu, mndithangate ine
Kupempha bwino izo zindisoŵa.
Kupempha monga Mlungu amafuna
Kulingalira zake zokhazo.
6. Mzimu Woyera, n'dzipereke ndense,
Mundichitire ntchito yaikulu;
Mtima woyera ndi womvera mpatse,
Wodzala ndi chikondi chanucho.

## 67

1. MPUME pa inetu, Mpweya wa Mulungu,
Ndi kundidzaza moyo wanuwo,
Kuti ndikonde zomwe mukondanso,
Ndichite chomwe mumachitanso.
2. Mpume pa inetu, Mpweya wa Mulungu,
Mpaka mtimanga ukayeretu,
Ndipo zokhumba zanga zilingane
Nazo zanuzo zakuyera mbuu!
3. Mpume pa inetu, Mpweya wa Mulungu,
Mpaka ndikhale wanu nokhatu;
Ayeretsedwe makhalidwe anga
Ndi mphamvu yanu yondisunga nji!
4. Mpume pa inetu, Mpweya wa Mulungu,
Kuti inedi ndisafe 'yitu,
Koma ndikhale nanu m'moyo womwe
Wangwiro ndi wa nthaŵi zonsetu.

## 68

1. MUBWERE Mzimu Inu
Woyera wakufatsa,
Muchotse mdima m'mtima mwathu
Tikapenye m'maso.
2. Mtisangalatse m'zonse,
Ndi wachifundo Inu,
Tiyembekeze kumapazi
A Mbuyathu Yesu.
19
3. Mtitsitsimutse ife
Kuchotsa nkhaŵa zathu,
Muyatse moto wachikondi
Mu mitima yathu.
4. Mtitsutse titachimwa
kutilapitsa m'mtima,
Mwonetsenso chikondi chokhulululukira tchimo.
5. Kutiyeretsa m'mtima
Ndi ntchito yanu yokha,
Kupatsa moyo watsopano
M'mene timafoka.
6. Mukhale m'kati mwathu,
Mutichotsere mantha,
Tidzayamika 'Tate wathu,
Mwana wawo ndi 'Nu.

## 69

1. IDZANI, Mzimu Inu,
Mundidalitse kuno;
Ndafoka mtima ine
Polendo wanga uno;
Kwambiri ndakhumudwa
Panjirayo ya moyo;
Mkaleka kutsogola
Ndiwonongeka pompo.
2. Wakunga mwana ine,
Sindidziŵitsa konse;
Mundilangize Mzimu
Panjira yanga yonse;
Mundiyendetse bwino
Ndifike ine ndemwe
Panjira yolungama,
Kudziko lachimwemwe.
3. Mundilimbitse m'mtima
Pogwira ntchito izi;
Ndikapumula pena
Mukhale ndithu ndine;
Zolingirira zanga
Ziyere zonse m'mtima
Zoipa muzichotse,
Sindidzazichitanso.

## 70

1. MZIMU Woyera, mudzetu,

Tiyeretsedwe m’mtimamu;
Mupatse anthu anuwa
Mitulo yanu yonseyo.
2. Kudzoza kwa Kumwambako
Kutitonthoza m’mtimamo,
Ndi kutidzutsa m’moyomu,
Tikhale okondanatu.
3. Pankhope pathu mthirepo
Chisomo chanu chijacho;
Mtendere mutininkhebe,
Mutiyendetse ponse phee!
4. Tionetseni tonsetu
Umodzi wanu wonsemo,
Atate, Mwana, Mzimu ’Nu
Tiimbe Nthaŵi zonsezo:
*Titamire Nthaŵi zonse*
*’Tate, Mwana, Mzimu, Nonse.*
*Amen.*

## 71

1. MUBWERE kuno Mzimu ’Nu
Chitsime cha chikondicho;
Mudziŵa ndimaliratu,
Mukhale m’mtima mwangamo;
Ndipatsa inu mtimawu,
Masiku onse mkhalemu.
2. Mukonze mtima wangawu,
Muyere ndithu m’katimo;
Ndilinda tere, Mzimu ’Nu,
Mupatsetu chikondicho;
Lichepa dontho lokhali,
Ndipempha mundidzazedi.
3. Ndilira Mzimu leroli,
Mutsimikize Mawuwo;
Ya Mbuye Yesu mphamvuyi,
Ikhale yathu, yanganso;
Mulowe m’mtima, mdzazetu
Ndi mphamvu, nzeru, moyowu.

## 72

1. Mbuye wondipulumutsa
Mulandire mtima wanga,
Mwandipatsa mzimu wanu
Womeretsa zipatsomo.

*Ndiye mzimu wakuyera*
*Atipatsa ife makhalidwe*
*Ofanana naye Yesu,*
*Anatsika kumwambako.*

2. Naye mzimu mndiphunzitsekuko
Kukondwera nsiku zones
Ndi kukhara ndi mtendere
Osadaratu nkhawa ayi!
3. Mndithandize kukondana
Ndi kuthangatira onse
Ndi kukhululukirabe
Akundichimwirawo.
4. Mndirimbitse ndipirire
Osadandaura konse,
Ndi kulamulira thupi
Ndi zofuna zakezo.
5. Kudzirala ndi kufatsa,
Inde, zonse muzikonda,
Mndiphunzitse pondipatsa
Mzimu wanu woyerawo.

## 73

1. MBUYE, Mawu anu
Atikondweretsa,
Atitsogolera,
Salephera konse.
20
2. Poyesedwa ife
Atipambanitsa,
Natonthoza mtima
Natipulumutsa.
3. Tikaona bvuto
Tikaloŵa m’dima,
Kuunika kwake
Kusonyeza njira.
4. Atisangalatsa,
Atilemeretsa
Poŵerenga mommo
Nawo mtima wonse.
5. Ndiwo alimbitsa
Omwe akufooka,
Naŵapatsa moyo
Akufuna kufa.
6. Mbuye, mtiphunzitse
Nzeru zake zonse,
Tikayenderane

N’tiyanjane nanu.

## 74

1. Cholimbitsa mtima ndi
   Chonditsogolera
   M’njira ya Mulunguyo,
   Ine ndili nacho.

   *M’Bukuli ine ndi*
   *Onse owerenga*
   *Mawu a Mulunguwo,*
   *Timapeza moyo*

2. Dzinthu zakumundazo
   Zilimbitsa thupi
   Zolembedwa m’Bukumo
   Zimadyetsa mtima.
3. Ndikachimwa, Bukuli
   Lindiyambotsutsa
   Limanditonthoza ndi
   Mau a mtendere.
4. Pakudera nkhawa ine,
   Pakuchita mantha,
   N’kawerenga m’Bukuli
   Lindipatsa mphamvu.
5. Lindionetsela ‘ne
   Chifuniro chake
   Cha mbuynga Yesuyo,
   Ndikamvera bwino.
6. Zonse mwazilembamo,
   Mzimu wakuyera,
   Kuzimvera zonsezo
   Mundithangatire.
7. M’Buku lakuyerali
   Powerenga ife,
   Mbuye mutipatsemo
   Moyo, moyo, moyo.

## 75

1. MUNDINYEMERE ’ne
Mkate wamoyo
Monga kunyanja kuja kalelo;
Ndipyola Mawuwo,
Ndifuna Inu,
Ndikhumba Inu mwini moyowo.
2. Mkate wamoyowo
Ndinu Ambuye;
Mawu oyera anu n’khumbanso,
Mun’dyetse onsewo
Ndikhale moyo,
Ndikonde zakuona zanuzo.
3. Mtume tsopanoli
Mzimu Woyera,
Kuti andikonzere m’masomo;
Abvumbulutse zinsinsi za m’Mawu,
Kuti ndionemo Ambuyeyo.
4. Mndidalitsire ’ne
Mawu amoyo,
Monga munadalitsa mkatewo;
Ndikhale mfuludi,
Wosamangika,
Mukhale moyo wanga wonsewo.

## 76

1. MBIRI yakalelomwe
Mundisimbiretu
Ya Yesu Mbuye yemwe
Anandiferatu.
2. Simbani bwinobwino -
Ndilibe nzeru ’yi -
Ndimve tsopano lino
Mbiri ya moyowo.
*Mbiri yakalelomwe,*
*Mbiri yakalelomwe,*
*Mbiri yakalelomwe*
*Mundisimbiretu.*
3. Mawu amveke bwino,
Alowê m’mtimamo,
Ndizindikire tsono
Chipulumutsocho.
4. Simbani mobwereza,
Ndisaiŵale ‘yi
Koma ndisunge bwino
Mumtima Mbiriyi.
5. Simbani Mbiri yonse
Ya Mbuye wangayo;
Zochimwa zanga ndizo
Zinapha Yesuyo.
6. Simbanitu mwachete
Mbiri ya Yesuyi,

Pakubvutidwa ine
Inditonthozepo.
7. Simbani Mbiri yomwe,
Ndikhulupiredi,
Kuti pakuyesedwa
Ndipulumukepo.
8. Inde, pakufa panga
M'maso mukhale mbee!
Mbiri ya Mbuye wanga
Mundisimbirebe.

## 77

1. Kodi ulikulemedwa
Ndi zoipazo?
Idza kuno, ati Yesu,

Pumako.
2. Ndikamzindikira ninji
Mbuye wangayo?
Ali ndi mabala m'manja
Mwakemo.
3. Kodi ali ndi chilemba
M'phumi mwakemo?
E, chilembacho chaminga
Chilimo.
4. Ndikampeza, ndikamtsata
Ninji pansipa?
Masauko ndi misozi
Zilipo.
5. Ndikamfunafuna Iye,
Ndipezenjiko?
Kumaliza kwa chisoni
Chonsecho.
6. Ndikampempha anditenge,
Akataniko?
Ati Yesu, "Idza msanga,
Idzatu."

## 78

1. MUSAŴALOLE mawuwo
Apite ngati mphepozi,
Musaumitse mtimatu,
Polira Yesu Mbuyedi.
*Idzanitu, idzanitu,*
*Idzani kwa Ambuyeyo.*
*Idzanitu, idzanitu*
*Apulumutse inunso.*
2. Musachitenso nthantha 'yi,
Mufulumire inutu;
Tsiku labwino nleroli,
Mulandirenso moyowu.
3. Zokondweretsa m'dzikomu
Nzosakhutitsa m'mtimamu,
Koma za Yesu zonsezo
Zikwaniritsa inudi.
4. Sakukanani Yesudi,
E, mukalapa m'mtimamo;
Lolani kuti Mzimuyo
Agwire ntchito zakezo.

## 79

1. PAKUPEMPHA ife pano,
Pakwitana 'Tatewo,
Pakudziŵa tsoka lako,
Bweratu kwa Mbuyeyo.
*Idzatu, idzatu*
*Kwa Mbuyathu Yesudi*
*Idzatu, idzatu,*
*Iwe bwera leroli.*
2. Unachimwachimwa ndithu,
Wasokera m'talimo
Unachedweranji kudza
Pakulinda Yesuyo?
3. M'dziko lino pansi pano
Sungapeze kanthumo
Kokwanitsa mtima wako;
Bweratu kwa Mbuyeyo.
4. Bvumbulutsa zonse zako
Zobisika m'mtimamo;
Ayeretse moyo wako
Nawo mwazi wakewo.

## 80

1. MIPINGO iyo idzatu,
Yoyenda mangu pajapo,
Afuma kuti anthuwo?
Afika bwanji komweko?
*Anena anthu onsewo,*
*"Yesu Sing'anga apitapo."*
*Anena anthu onsewo,*
*"Yesu Sing'anga apitapo"*
2. Azizwa anthu ajawo,
Nafunsa, "Ndani mlendoyo?
Wanzeru monga Iyeyo

Kulibe wina konseko."
3. Ndi Yesu yemwe kalelo
'Nakhala munthu pansipa;
Anthenda onse nthaŵiyo
Nachira yake mphamvuyo.
22
4. Afika Yesu leroli,
Chifundo m'mtima mwakemo,
Timfitse msanga kwathuko
Akhale nafe ponsepo.
5. Timsankhe Yesu Mbuyeyo,
Timyese Mfumu yathuyo,
Chifukwa tikamkanatu
Tikhala otayikawo.
*Tsopano inu 'dzanitu,*
*Asanapitirirepo.*
*Tsopano inu 'dzanitu,*
*Asanapitirirepo.*

# 81

1. Ukapenya kwa yesu uliko moyobe,
   Inde, moyo tsopanopanotu;
   Olakwira upenye kwa Yesu mbuyeyo,
   Kuwombola naferatu 'we.

   *Ona! Ona! Anatu!*
   *Kuli moyo kwa yense apenya yesuyo*
   *Wakuferatu pamtandapo.*

2. Anasenza pa bwanji uchimo wonsewo
   Ngati wanu pa Yesu sulipo?
   Bwanji mwazi wakhetsa kutsuka ifetu,
   Ngati uwu sutikwanako.
3. Zilepheradi zonse kugula moyowu,
   Koma mwazi wa Yesu mbuyeyo.
   Khulupira mwa phamvu ya mlungu wathuyu.
   Nuyeretsa 'we m'timakoma
4. Anathera pamtanda zintchito zonsezi
   Zowombola mizimu yathuyi,
   Ndipo yense akadza mokondwakondwadi
   Moyo apeza kwa Yesuko.

# 82

1. AMBUYE wathu Yesu
Akhala Mfumunso;
Zoipa zazikulu
Azigonjetsa 'Ye;
Anena mawu ake
Ochotsa zonsezo,
Kalelo nalamula:
Pakhala bata duu!
2. M'ulemerero mwake
Anenanenabe:
Munkhondo apambana
Ndi mawu akewo.
Akristu akondwera
Poona mphamvuyo
Ya Mbuye wathu Yesu
Wotiwombolayo.
3. Zobvala zake zonse
Nza mwazi woti pyu!
Pamphumi pake pomwe
Korona waketu.
Unyolo wa Satana
Umasulidwako;
Kumwamba amithenga
Atama Mbuyeyo.
4. M'kufatsa kwake komwe
Anena nafenso,
Tonsefe omangidwa
Ndi zakuipazi;
Ambuye amanena
Zotichenjezazi:
Ananu, msiye zonse,
Mupulumuketu.
5. Chikondi cha Mbuyathu
Chiposa zonsetu;
Chisomo chake chomwe
Chikondweretsabe;
Ulemu wake wonse
Umapambanadi;

Tiyeni, tikondwere
Popita m'Mwambamo.

## 83

1. Sing'anga 'mkulu ndiye Yesu,
Mwana wa Mulungu;
Asangalatsa achisoni,
Ali wachifundo.

*Dzina la Yesu ndi lokoma,*
*Dzina la Yesu lipambana,*
*Dzina lake lakukonda,*
*Yesu, inde Yesu.*

2. ……………. Sakhululukidwa
Yesu amatero;
Tiyende bwino mnjira yake
…………………..

3. Nditama nsembe ya mulungu,
Ndilandira Yesu;
Ndikonda dzinalo labwino,
Dzina lanu Yesu.

4. Akulu inu mbwere nonse,
Ana inu nomwe,
Ambuye akuitanani;
Bvomerani nonse.

## 84

1. UTHENGA wa Mulungu
Walowâ m'mtimamu,
Wochotsa zakuipa
Zakundidetsazo.
*Pakuti anthu akumvera*
*Yesu aŵapulumutsa,*
*Ine, aŵapulumutsa, indetu.*
2. Ndidziŵa kuti Yesu
Anafa kalelo,
Nafafaniza zonse
Tinazichimwazo.
3. Satana ndi unyolo
Anandimanga nji!
Ambuye Yesu yekha
Nandimasuladi.
4. Ambuye mulowêtse
Mtendere m'mtimamo,
Ndimvetse mawu anu
Masiku onsewo.
*Akuti anthu akumvera*
*Yesu aŵapulumutsa,*
*Inde, aŵapulumutsa, indetu.*

## 85

1. OKOMA ndiwo mawu
A Yesu Mbuyeyo,
Wopatsa ife anthu
Mtendere wakewo.
Kwa ife akumvera
Kulibe mantha 'yi;
Timamva liu lake
Lingoti, "Mudze 'nu."
23
*Inu akutopawo*
*Yesu aitana 'nu;*
*Mudze kwa Ambuyeyo,*
*Mudze msangatu.*
2. Mukana Iye bwanji,
Wokoma Bwezilo?
Mutsate Yesu yekha,
E, mpaka imfayo.
Mwafoka osokera,
Mwadetswa nazozi
Zoipa mwazichita;
Mumvere Mbuyedi.
3. Ambuye, musendeze
Pafupi nafedi,
Timvetse Inu msanga,
Poyenda m'dzikoli.
M'ulendo m'moyo uno
Titsate Inutu;
Kumwamba mutifitse,
Tidzamve: "Idzani."

## 86

1. Inu nonse obutidwa,
Mbuye alipanopa;
M'maso mwanu muli msozi;
Dzani kwa Mbuye wathuyo.

*Yesu ngwachifundodi*
*K! wafera inutu,*
*K! wafera inutu.*

2. Yesu ndiye bwenzi lanu,
Ali wachikondicho;
Kodi inu mumkanabe?
Mlape msanga m'mtimamo.
3. Pena imfa idza mawa,
Manda ali mfupimo;
Nthawi yino niyabwino,
Mlole Yesu m'mtimamo.
4. Ndi angelo akumwamba
Anke ndi uthengawo
Kuti wina adza lero
Kwa mbuyathu yesuyo.

## 87

1. Wochimwa iwe bweratu
Kwa Yesu mbuyeyo;
Atero iye; pumatu;
Umvere mawuwo.

*Khulupira mawu onse*
*A mbuyeyo;*
*Ulinawo pakumvera*
*Inde, moyowo.*

2. Ambuye Yesu anatsira
Mwazi wake pyu!
Ubire m'mwazi omwewo,
Uyereyere mbuu!
3. Wamoyo ndiye Yesudi,
Nzoona zakezo;
Akhala iye njiratu
Yofika m'mwambamo.
4. Tiyeni tonse, tinkeko
Ulendo wakewo
Mudziko lake m'mwambamo,
Tikhale nayeko.

## 88

1. YESU ndi wokonda;
Ati "Idzatu,
Yense wakufuna,
Bwera msangatu."
Ali wachifundo
Ndi wamphamvunso
Nthaŵi zonse Yesuyo
Alindatu.
*Yesu akukonda,*
*Idza msanga 'we,*
*Adikira iwenso;*
*Wachedwatu.*
2. Iwe afuna,
Inde, kalelo;
Leronso adika
Mbuye wathuyo.
Uza Iye zonse
Za uchimowo;
Yesu ati leroli:
"Wachedwa 'we."
3. Yesu alindira,
Inde, iwetu;
Idza ndi kukhala
Ndi chimwemwenso
Ndi mikono yake
Yachikondiyo;
Sankha Iwe msangatu;
Wachedwatu.

## 89

1. Lero lino mbale wanga,
Ndilo dzuwalakukoma;
Talandira mpulumutsi
M'mene ali kuitana.
2. Lero lino mbale wanga,
Usazengereze ayi;
Ngati ulindira Yesu
Lero udzachita mwayi.
3. Lero lino ndi la bwino;
Moyo wako ulinawo;
Pena mawa umwalira,
Uzdatani mlandu wako?
4. Lero lino mbale wanga,
Lapa mtima, lapa tchimo,
Yesu adzakulandira,
Ukapempha lero lino. 5.
Ndiwe mlendo lero lino,
Mvera ndikupepha iwe;
Yesu mwana wa Mulungu
Akufuna ndithu iwe.
6. Inde, lero lino Yesu
Aitana inu nonse.
Landirani Mpulumutsi,
Musazengereze nonse.

## 90

1. PENYETSETSA Yesu,
Mtima wosauka;
Anafera iwe,
Idza, nupumule.
Iye anachotsa
Nsoni ndi zoipa;
Penyetsetsa Yesu,
Ndi kukhulupira.
2. Penyetsetsa Yesu
Likatentha dzuŵa;
Yachuluka ntchito,
Mphamvu idzakula.
Akonzera kwawo
Nyumba zokhalamo;
Penyetsetsa Yesu,
Mtsatetu tsopano.
3. Penyetsetsa Yesu
Pogwirana nawo;
Nkhondo ikabvuta
Tamva Mbuye wako.
Achuluka ’dani,
Iwe ungofoka;
Penyetsetsa Yesu,
Mantha adzachoka.
4. Ndipo pakuloŵa
M’dziko la Kumwamba,
Udzapeza komwe
Onse adzatama.
Mwa zoŵala zija
Za Kumwamba kwawo,
Udzapenya maso
Yesu Mbuye wako.

## 91

1. MALO anachepa,
Nyumba anammana,
Agona m’modyera,
Mutu paudzuwo.
Anthu sanamtama,
Nyimbo panalibe,
24
M’nyumba ya alendo
Malo munalibe.
*Apempha malo Ambuye;*
*E, mlandiretu m’mtimamo,*
*Ungamvetu Kumwambako,*
*“Akusowanso malo.”*
2. Wina panalibe
Kumlandira Iye,
Wakumsangalatsa,
Wamkonda nasowa.
Anthu sanafuna
Chuma chosatha,
Sanamkondweresa,
Malo unalibe.

## 92

1. ATATE,’nu, atate ’nu,
Mverani Ambuye.
*Khulupirani kuti mukaloŵe m’Mwambamo,*
*Khulupirani kuti mukaloŵe M’Mwambamo.*
2. Amayi ’nu, amayi ’nu
Tsatani Ambuye.
3. Abale ’nu, abale ’nu,
Kondani Ambuye.
4. Alongo ’nu, alongo ’nu
Kondani Ambuye.
5. Abwezi ’nu, abwenzi ’nu,
Tamani Ambuye.
6. Oipa inu nonsetu,
Mverani Ambuye.

## 93

1. NDICHITENJI kukapeza
Moyo? thandizeni!
Ndili wakutopa; Mzimu,
Muthandize ine.
*Zonse zinathedwadi;*
*Yesu watha zonsezo;*
*Sutha ntchito, ungomvera*
*Mawu ake omwewo.*
2. Iye anatsika m’Mwamba,
Anachoka kwawo,
Anafera anthu, nati:
“Ndatha zonse zawo.”
3. Mbuye wanga ndilikumva,
Ndikondana nanu;
Umapuma mzimu wanga,
Kwathu ndiko kwanu.

## 94

1. KODI mwalandira Yesu?
Iye anakuferani.
Afunitsa inu nonse;
Kodi mumufunanso?
*Kodi mufunatu Yesu?*
*Bvomerani msangatu:*
*“Inde Yesu ndifunadi,*
*Ndinu Mbuye wangatu.”*
2. Nthaŵi zonse mufunabe
Zinthuzo za pansi pano;
Koma munyozabe Yesu
Wopachikidwa kalelo.
3. Yesu akuitanani
Kwanja kwake kwakukulu;
‘Mvani mawu ake lero,
Musachite nthantha ’yi
4. Imfa idzafika msanga;
Ndipo mdzaikidwa m’manda;
Nthaŵi yomwe simudzamva
Kutitana kwakeko.

## 95

1. ’MVANI liu lomwe
M’khutu mwakomo,
Alikuitana
Mpulumutsiyo:
*“Undipatsetu*
*Mtima wakowo;*
*Ndinakuferau*
*Kalekalelo.”*
2. Ati: “Undiuze
25
Nsoni zakozo;
Ine ndidzachotsa
Zonse zomwezo.”
3. Kodi ukafuna
Kupumulatu?
Yesu aitana:
“Udze kunoku.”
4. Tula mtolo wako
Pali mtandapo,
Akaunyamula
Mpulumutsiyo.

## 96

*1*. YESU ponong’oneza, *idzanitu;*
Mupempherera ife, *idzanitu;*
Njabwino nthaŵi yino, *idzanitu*,
Yodziŵa Mpulumutsi, *idzanitu*.
2. Tulani zoipazo, *idzanitu*;
Yesu adzatha zonse *idzanitu*;
Olema ndi ochimwa, *idzanitu*;
Sakambukira izo, *idzanitu*.
3. Imvani mawu ake, *idzanitu*;
Mudzalandira dalo, *idzanitu*;
Nacho chisomo chake, *idzanitu*,
Yesu alinda inu, *idzanitu*.
4. Mverani Iye ati: *Idzanitu*
Tiyeni mudzamwone, *idzanitu*;
E! akuitanani, *idzanitu*;
Ife tibvomereza, *Tibweratu*.

## 97

1. *IWE tiye*, iwe tiye,
Tiye tsopanoli;
Pano tiye kuti Yesu,
Tiye tsopanoli.
*(Ndaima pano, ndaima pakhomo!*
*Loŵa, loŵa, loŵa, loŵa!*
*Ndaima pano, ndaima pakhomo!)*
2. *Akukonda*, akukonda,
Tiye tsopanoli:
Pano akukonda iwe,
Tiye tsopanoli.
3. *Akupeza*, akupeza,
Tiye tsopanoli;
Pano akupeza iwe,
Tiye tsopanoli.
4. *Salephera*, salephera,
Tiye tsopanoli;
Pano salephera Iye,
Tiye tsopanoli.
5. *Mvera Yesu,* mvera Yesu,
Tiye tsopanoli;
Pano mvera Yesu iwe,
Tiye tsopanoli.
6. *Aleluya,* aleluya,
Aleluya, Amen;
Aleluya, Aleluya,
Aleluya, Amen.

## 98

1. Tadza kukudyaku,
Kwakonzedwatu;
Mkate wamoyodi, idyatu ’we;
Bwera wochimwanso,
Yesu adikatu,
Akuitanaku; mvetsatu ’we
2. Tadza kumtsinjeku
Wa moyo weni,
Chiza zoŵaŵazo za m’mtimamo;
Mtsinje wodzalawo,
Wokwaniratuwo
Yesa sakana ’yi; idzatu ’we.
3. M’dzina la Yesuyo
Pemphatu iwe,
Iye adzamvatu, dikirapo.
Wamphamvu Mlunguyo,
Ndiye apatsatu,
Dalo labwinolo; idzatu ’we
4. Yamba ulendowo
Wonka Kumwamba;
Pano mpoipatu padzikoli;
Komwe tikondwako,
Tidzasekeranso;
Tinke Kumwambako; idzatu ’we.

# 99

26

1. MWAMVA Mawu a Mulungu;
Mukabvomeranjiko?
Kodi musandula mtima
Ndi kumvera Yesuyo?
*Bvomerani, Bvomerani*
*Bvomerani msangatu,*
*Musazengereze ayi,*
*Landirani Yesuyo.*
2. Munachita nthantha kale,
Musazengereze ’yi;
Yesu akulindirani,
Sadzakana inu ’yi.
3. Musaope pokumbuka
Zakuipa anuzo;
Khulupilirani Yesu,
Adzachotsa zonsezo
4. Perekani mtima wanu
Kwa Mulungu wathuyo;
Khulupirirani Yesu,
Wotifera kalelo.

# 100

1. YESU wathu Mbuyeyo
Alandira onsewo
Akuipa omwewo,
Osokera m’talimo.
*Imba kaŵiri ndi kaŵirinso,*
*Yesu Ambuye sakanatu,*
*Mvetsa Uthenga Wabwinowo,*
*Wakukchimwa adzatu.*
2. Idzatu kwa Yesuyo,
Apumitsa inunso,
Inde m’mtima mwanumo
Ndi mtendere wakewo.
3. Walandira inetu
Tsiku lija kalelo,
Wanditsuka ine mbuu
M’mtima mwanga momwemo.
4. Wandifera Yesuyo
Pansi pano kalelo,
Sindiopa mlanduwo
Pakubwera Iyeyo.

# 101

1. A! MBUSA wathu amvatu
Uko kuchipululuko
Zilira nkhosa zakezo,
Zili kuthengo kunjako.
*Bwezatu, bwezatu,*
*Bwezatu zonse m’moopsyamo;*
*Bwezatu, bwezatu*
*Bweza zakezo kwa Yesu*
2. Ndani afuna kunkako
Kukazipeza nkhosazo?
Ndani adzathandizako
Kuti zifunde m’kholamo?
3. M’tali mutali m’phirimo
Mvetsa, zilira nkhosazo; A!
Mbusa wathu atitu;
“Bweza zothodwa m’kholamo.”
4. Etu, zilira konseko
Zili m’phiri moopsyamo.
Imva, anena Mwiniyo:
“Kweye, upeze nkhosazo.”

## 102

1. Thanthwe long'ambikatu,
Ndibisale momwemu!
Madzi ndipo mwaziwo
Zotuluka mthitimo
Zinditsuke m'mtima mbuu!
Zindilimbikitsetu.
2. Ntchito zanga zonsezo
Sindikondweretsa 'Nu;
Ndikazigwiritsadi,
Ndikalira nsonizi,
Zonse sizikwanazi,
Koma Yesu yekhayo.
3. M'manja mopanda kanthu,
Mtanda ndingogwiradi;
Maliseche mbveke 'ne;
Ndili ndekha, msunge 'ne;
Ndithawira m'mtsinjewo,
Munditsuke m'mtimamo.
4. M'moyo uno kunsiku
Pena ndinawaliratu,
M'mene ndidzakwerako
Tionane masowo;
Thanthwe long'ambikatu
Ndibisale momwemu.

(*maiwe! Thanthwe long'ambikatu ndibisale momwemu)*

## 103

1. AMBUYE 'naitan 'ne;
"Dzapumulire kuno,
Tsamira mutu, mwana 'we
M'chifuwa mwanga muno."
2. Ndabwera kwa Ambuyeyo;
Wolema, wachisoni;
Anandipulumutsako,
Nakondweretsa ine.
3. Ambuye naitana 'ne;
"Ndipatsa anthu madzi,
Wotopa ndi waludzu 'we
Dzamwere moyo kuno."
4. Ndabwera kwa Ambuyeyo.
Ndamwera madzi awa;
Laleka ndithu ludzulo,
Tsopano moyo wadza
5. Ambuye naitana 'ne;
"La dziko ndine Dzuŵa,
27
Yang'ana Ine, kwacha 'we,
Wachoka mdima uja."
6. Ndayang'anira Mbuyeyo
Ndzapeza Dzuŵa langa
Londiyendetsa bwinoli
Pa njira yonse yanga.

## 104

1. YESU wondikondadi,
Ndithaŵire mwanumo
Pakugunda mvulazi.
Pakubvuta madziwo,
Yesu mundibise 'ne!
Ikaleka mphepoyo
Tsidya lija chete phee!
Mundilandire momwemo
2. Pothaŵira pena 'yi
Ndikhulupirira 'Nu;
Musasiye inedi,
Mundigwirizizetu.
Ndinu wothandiza 'ne
Wolimbitsa mtimawu;
Pansi pamapiko phee!
Mundifungatiretu.
3. Wina sindifuna 'yi,
Zokhutitsa nzanuzo;
M'utsetu akugwawo,
Mchizetu odwalawo.
Ndine wakuipa bii,
Ndinu wakuyera mbuu!
Ndimadzala tchimoli
Wolungama ndinutu.
4. Zindichulukirazi
Nsoni zanu m'mtimamu;
Zindichiza nthendazo,
Zindiyeretsetsa mbuu!
Pachitsime panupo
Moyo ndimwe ndimwebe;
Mubukatu m'mtimamo,
Mundilanditsetu 'ne
*(Mulungu ali nane!)*

*(Ali nane, ali nane, ali nane, ali nane, Aa!*
*Mulungu ali nane!)*

## 105

1. NDI inetu sinditha 'yi
Kunenako milanduyi
Kupempha zachisonizi;
Ndagonjatu Mbuyanga 'Nu.
*(Aa! Mulungu wanga,*
*Mundilembe pamphumipo:*
*Chidzakhala chizindikiro*
*Cha mpumulo ulinkudza ndi Yesu.)*
2. Ndi ine sizitheka 'yi
Kuchoka zakuipazi;
Ndisambe m'mwazi wanuwo;
Ndagonjatu Mbuyanga 'Nu.
3. Ndi ine pondibvutapo
Kugwira nazo m'mtimamo,
Mundithandize monsemo;
Ndagonjatu Mbuyanga 'Nu.
4. Ndi ine ndasaukadi,
Zabwino m'mtima zonsezi
Mwa Inu ndingapezezi;
Ndagonjatu Mbuyanga 'Nu.
5. Ndi ine simufuna 'yi
Ndingatayike m'mdima bii,
Ndimvere mwandiuzazi
Ndagonjatu Mbuyanga 'Nu
6. Ndi ine, m'mtima Mwanu mbee!
Mokoma ndingakhalebe,
Ndikhale wanu wanudi;
Ndagonjatu Mbuyanga 'Nu.
7. Ndi inetu ndidziŵedi
Chikondi chodabwitsachi
Pansipa ndi Kumwambako;
Ndagonjatu Mbuyanga 'Nu

## 106

1. NDIKHULUPIRA 'Nu,
Mwana wa Mlungutu,
Mbuyangayo;
Mumve popempha 'ne,

Tchimo muchotsebe,
Lero ndikhale 'ne Wa
Mlunguyo.
2. Mzimu mndipatseko,
Wondilimbitsayo
Mumtimamu.
Munandiferadi;
Ndiyambe leroli
Kukonda Inu ndi
Mtimangawu.
3. Poyenda m'mdima bii,
M'mtimamo nsonizi
Mndigwirepo;
Mdima uchoke zi,
Msozi ulekedi,
Ndisasokere 'yi
Kwa Inuko.
4. Moyo ukatha zi,
Pofika imfadi,
Mndisungepo:
Yesu Mbuyanga 'Nu
Mantha mthaŵitsetu
Ndifike m'Mwambamo,
E, wanuyu.

## 107

1. CHITSIMECHO cha mwaziwo
Udzera mwa Mbuyanga;
Wochimwa ndikasambamo,
Nditaya tchimo langa.
2. Wakuba uja nachiona,
Nangokhulupira,
Ambuye namva pempholo,
M'Mwambamo namlandira.
3. Ambuye, mwazi wanuwo
Siitha mphamvu yake,
E, Mpingo wonsewo
Wayera m'kati mwake.
4. Chionerere mwaziwo
Wofuma m'bala lanu,
Sindinaleke ineyo
Kutama mtima wanu.
5. Kumwamba komwe n'dzaimbira
Mpulumutsi wanga,
Chifukwa ayeneratu,
Wakonza m'mtima mwanga.

## 108

1. Yesu mundimve ndikuliratu,

‘Dzani kwa inetu;
Mtimangawu ufuna unidi,
Bwerani, Yesudi.

*Ndinasokeratu kutaliko,*
*Ndalekana naye Mulungudi;*
*Tsopano koma mndirandirenso,*
*Bwerani Yesudi.*

2. Ndilibe malo mokhaliramo,
‘Dzani kwa inetu;
Khalani nane m’mtima mwangamo,
Bwerani Yesudi.
3. Njobvuta njira ndimayendamo,
Dzani kwa inetu;
Adetsa m’maso ndimapunthwamo,
Bwerani Yesudi.
4. Wolap mtima simunyozadi,
Dzani kwa inetu;
Pemphero mumve langa lonseli,
Bwerani Yesudi.

# 109

1. Ndilinkudza kwa ambuye
Ndasauka ,ndinachimwa;
zonse zanga ndizisiya,
kudzapeza moyo wina.

*Yesu ndikhulupirira*
*Munafera ine nemwe!*
*Mwa umphawi ndipemphera*

2. Kale ndinalira inu,
Kale lomwe ndangochimwa;
Mund’itana, “idza bwino,
Kuti nkuchotsere tchimo”.
3. Yesu n’kupatsani zonse,
Zili nanu zokhazokha,
Thupi lonse, mtima womwe,
Mwini wake ndinu nokha.
4. E, ndikukhurupirirani,
Ndauona mwazi wanu;
Tere ndikugwadirani,
Tere ndapachikwa nanu.
5. Wadza Yesu wandidzoza,
Ndakonzeka mwa iyeyu;
Ndine wake, tokondana,
Ndiyamika mbuye Yesu.

# 110

1. NDIKHULUPIRIRA, Yesu,
Inu nokhadi
Mundipulumutsa konse
Leroli.
2. Kuti mukhulululukira
Tchimo langalo
Ndi chifundo chachikulu
Chanucho
3. Kuti muyeretsa mtima
Ndibvomeratu;
Mwazi wanu unditsuka
M’mtimamu.
4. Kuti munditsogolera
Paulendopo;
Mukwanitsadi zosoŵa
Zangazo.
5. Kuti mundipatsa mphamvu
Yopambanayo;
Mau mundilonga m’kamwa
Mwangamo.
6. Ndikhulupira, Yesu,
Mndibvomereko;
Ndine wanu lero, maŵa,
Konseko.

# 111

1. NDASIYA zonse ndi Yesu kalelo,
Inde zakuipa zangazo;
Anafera ine m’phirimo:
Pomva Mawu ake n’kondwako;
Mumachoka m’mtima
Mwangamo nsonizo,
Mumachoka m’tima

Mwangamo nsonizo.
2. Chisoni andichotsera Mbuyeyu,
An'thandiza ine teretu;
Ndikhulupirira Iyeyu
Andisunga m'manja mwakemu;
Alimbitsa mtima
Wangawu teretu,
Alimbitsa mtima
Wangawu teretu.
3. Mtima 'we siya ndi Yesu nsonizi,
Usabisa tchimo lakoli
Zichuluka mphamvu zakezi,
Likusunga dzanja lakeli;
Bwera kwa Mbuyathu
leroli mwana 'we,
Bwera kwa Mbuyathu
leroli mwana'we.

# 112

1. KWA Inu Yesu ndilira,
Wopanda Inu ndidzafa;
Mupulumutse ined,
Mundilandiretu.
*Mundilandiretu,*
*Ndiipa m'mtimamo*
*Kotero mnandiferatu*
*Mundilandiretu.*
2. Ndifoka ndi zoipazo,
Ndidzalatu ndi machimo,
Sinditha kuzitayazo;
Mundilandiretu.
3. Ndayesa kudzikonzadi,
Ndapeza mphamvu ndilibe,
Zoipa zakanikadi;
Mundilandiretu.
4. Onani Mbuye ndigonja,
Kuyesa kwanga ndaleka;
Chitani Inu mumtima;
Mundilandiretu.
5. Muyambe ntchito yanuyi,
Musalekenso, chitani
Ndidzipereka leroli;
Mundilandiretu.

# 113

1. YESU, mulikundipempha
Munaterodi;
"Mwana, gonja, ndikupatsa
Chimwemwe."
2. Kale ndinakana Inu,
Ndinathaŵatu:
Ndinazengereza, ndati:
"Maŵatu."
3. Lero mtima ungolema,
Usaukadi;
Wina wakundimasula
Ndilibe.
4. Mbuye, ndingogonja tere,
Ndibvomerapo;
Mundithyole, mundikonze
M'mtimamo.
5. Chifuniro changa, Mbuye,
Ndiperekachi;
Mutsogole, ndidzatsata
Inudi.
6. Tere moyo wanga wonse,
Mawu, ntchitonso
Zidzakondweretsa Inu
Zonsezo.
7. E, chimwemwe chachikulu,
N'taperekadi
Mtima wanga, ndimapeza
Mtendere.

# 114

1. Chitha nchianikudyeretsa;
Mwazi wa Ambuye Yesu;
Nchiani chindipulumutsa?
Mwazi wa Ambuye yesu.

*Chitsime ndi chokoma*
*Chindiyeretsa bwino,*
*Chinanso sindifuna,*
*Mwazi wa Abuye ndiwo.*

2. Mtanda m'mtima ndiyangana,
Mwazi wa Abuye yesu;
Ndikhulukidwa nawo
Mwazi wa Abuye Yesu.
3. Zonse zina sizikwana,
Mwazi wa Ambuye ndiwo;
Ntchito zanga sinditama,

Mwazi wa Ambuye ndiwo.
4. Ndikhulupirira bwino
Mwazi wa Abuye Yesu;
Chilungamo change ndicho
Mwazi wa Ambuye Yesu.

# 115

1. MNDILANDIRE ine Mbuye
Yesu wondifera ‘ne;
M’mtima mwanga muzikhala
Mawu anu okhawa.
2. Ndasokera m’tali ndithu
M’njira zopwetekazo;
Wolemedwa ndingopempha,
Mndilandire inetu.
3. Pakukumbukira zanga
Ndili ndi manyazitu;
Ndingogwera pansi, ’Tate,
Mlapo wandigwiratu.
4. Ndingopatsa Inu Mbuye
M’manja mwanu mtimawu,
Moyo, mzimu, zonse zanga,
Mzilandire Mbuyetu.
30
5. Mukhulukukire ine,
’Tate mundikondadi;
Mundisunge nthaŵi zonse
Ndi chikondi chomwechi.

# 116

1. A CHIKONDI chopambana,
E, chinadza ndi Mbuye;
Chinasangalatsa m’Mwamba,
Chinaloŵanso mwa ’fe
Yesu ndinu wachifundo, Wa
chikondi changwiro, Ee,
muloŵetu m’mtimanga,
Mumuyese mwanutu.
2. ’Dzanitu Wamphamvuyonse,
Mtilanditse konseko;
Musachedwe, thandizeni
Musachoke mwangamu;
Inu nokha timakuza
Nditumikirabe;
Tinyadira chikondicho,
Tichitame konseko.
3. Tsirizani ntchito yanu
Yakulenganso ife;
Idzakhalatu yangwiro,
Ndiyo yoyenera ’Nu
Usinthika ’lemu wathu,
Udzakhala momwemo,
Mpakatu Kumwamba komwe
Tidzalemekeza ’Nu.

# 117

1. NDILIKUMVA m’mtima mwanga
Mau ake a MbuyAnga,
Ati, “Ndakukonda iwe,
Kodi undikonda Ine?”
2. Ati; “Mwana, kumbukira
Zonse ndinakuchitira;
Ndakukonda, ndakufera,
Ndakufuna posokera.
3. “Ku zoipa zonse zako,
Goli la pakhosi pako,
Ndi kunthenda zosautsa
Ndine ndakupulumutsa
4. “Kodi mayi wobereka
Mwana wake adzamleka
Pena adzamwiŵalira,
Koma ndikukumbukira.
5. “Nthaŵi ilikudza yonse
Sindisinthanika konse;
Imfa sindiletsa Ine
Ndisakondekonde iwe.
6. “Ine ndidzakuonetsa
Zonse zakukondweretsa
Za Kumwamba zanga izo,
Mwana, sundikonda ine?”
7. Ambuyanga, ndalephera,
Mwachisoni ndipemphera
Mundipatse ine ndithu
Mtima wakukonda Inu.

# 118

1. ATI Yesu Mbuyeyo:
“Ofoka ndinutu,
Mudikire, m’pemphedi,
Ndidzapatsa mphamvutu.”
*Yesu wathadi*
*Za mangaŵatu,*
*Inde ndinaipa bii!*
*Watsuka ine mbuu!*

2. Mbuye ndimva leroli
Za mphamvu zanuzi
Zomwe zisandutsadi
Mtima wanga woti bii!
3. Ine kanthu ndilibe
Kogula moyowu;
Ndingotsuka m'mtimamo
M'mwazi wa Ambuye 'Nu
4. M'mene ndifa inedi,
Kumwamba mzimuwu
Udzakwera komweko
Kuonana Mbuyeyo.
5. Ndipo pakuima phe!
Pokhala Yesuyo,
Ndidzamama Mlunguyo
Kosaleka konseko.
31

# 119

1. LINDIKOMERA dzina la Ambuye Yesu wanga,
Lisangalatsa, lichiritsa, lin'chotsera mantha.
*Dzinalo la Yesu,*
*Dzinalo la Yesu1*
*Lindikomera dzina la Ambuye Yesu wanga.*
2. Lichiza mzimu wophwetekwa ukakhale
bata,
Lidyetsa mtima wonse, lipumitsa thupi langa.
3. Nlokoma dzinalo la Yesu, ndilo thanthwe langa,
Chikopa changa, linga langa m'mene ndibisala.
4. Ambuye ndinu Mbusa, Bwenzi, ndi Wansembe wanga,
Ndi Mfumu, Moyo, Njira yomwe,
Inde ndimatama,
5. Tsopano ndibukitsabe chikondi chanu chija,
Pakufa ine Dzina lanu lindilimbikitsa.

# 120

1. Ndidzaimba za Mulungu,
Zakukondakwakeko,
Anatuma mwana wake
Kundifera kalelo

*Inde ndidzaimba nyimbo*
*Za kukonda kwakeko,*
*Ndidzaimba ndi Angelo*
*Akukhala m'mwambamo.*

2. Ndinachita mphulupulu,
Waiwala zonsezo;
Ndinakhala ndi zoipa,
Wazichotsa zonsezo!
3. Wandipatsa moyo wake,
Moyo wakuyera mbuu!
Ine ndili mwana wake,
Wandilera inetu.
4. Ndiyamika mbuye wanga
Ndidzamulemekezabe.

# 121

1. BWENZI ndinamkomanayo
Anandikonda kale;
Kukonda kwandigwirako,
M'kukondamo nditsale.
Kumtima kundimangako
Kosamasuka konse;
Ambuye ndine wanutu
Kunthaŵi nthaŵi zonse.
2. Bwenzi ndinakomanayo
Anandifera yekha,
Anandipatsa moyowo,
Ndatenga ine ndekha.
Zimene ndili nazozi
Nza Yesu mwini zonse, Ndi
moyo wanga wonse ndi
Wakenso nthaŵi zonse.
3. Bwenzi ndinamkomanayo,
Ndapeza mphamvu zanga,
Zakundisunga inemo,
Ndiyende m'njira mwanga.
Zolemera zoti mbee!
Zindilimbitsa monse;
Ndalema kuno, komweko
N'kupuma nthaŵi zonse.
4. Bwenzi ndinamkomanayo

Wokoma mtima wake,
Wotsogolera nzeruzo
Zisunga m'njira mwake.
Palibe wondichotsa 'ne
Kwa Iye wondikonda;
Pamoyo, imfa, nayeyo
Ndilipo nthaŵi zonse.

## 122

1. NDIMKONDE Kristuyo,
Ndimkondebe;
Pemphero langali
Mlandiretu;
Ndipempha Inutu,
Ndimkonde Kristuyo,
Ndimkondebe,
Ndimkondebe.
2. Ndatsatatsatabe
Za pansipa;
Ndisiye zonsezi,
Nditate 'Nu.
M'mtimanga wonsewu
Ndimkonde Kristuyo,
Ndimkondebe,
Ndimkondebe.
3. Chisoni chonsecho
Chidzatha phe!
Angelo anuwo
Afiketu;
Nawo, ndiimbetu,
Ndimkonde Kristuyo,
Ndimkondebe,
Ndimkondebe.
4. Pakufa pangapo
Ndinenebe;
Myamiko wangawu
32
Ndikwezebe,
Ndidzapempheradi,
Ndimkonde Kristuyo,
Ndimkondebe,
Ndimkondebe.

## 123

1. MWAKHULUPIRIRADI
Yesu Ambuyathu;
Muli nazo zakezo,
Zidzatu zinanso.
Mlungu wachisomocho
Mbuye wathu ndiye,
Ati zinthu zonsezo
Nzathu mwa Iyeyo.
*(Zina ndi zinanzo*
*Zidza kwa ifedi,*
*Inde mtima wakewo*
*Uli wokomadi.)*
2. Mwamva Yesu m'mtimamo,
Adzanso kaŵiri,
M'mene ali nanutu
Muli ndi Chimwemwe.
Ntchito zachifundozi
Iye watha izi,
Kuti mwawo m'Mwambamo
Naye tikhalebe.
3. Mwamva Mzimu wakewo,
Zake zimvekanso
Kugwa ngati mvulayo
Yachisomo chake.
Mzimu ndiye mphamvudi
M'moyo mwathu muno,
Mpaka tidzafikako
Komwe kuli Yesu.

## 24

1. Poyambapo ndakondwadi,
N'tapeza inu Mbuyetu,
Ndiimba nyimbo yomweti,
Kukondwa sindikhala duu!

*Kalelo! Kalelo!*
*Wandisambitsa m'mtimamo,*
*Wandiweruza lomwelo,*
*Kupempha ndi kukondwako,*
*Kalelo! Kalelo!*
*Wandisambitsa m'mtimamo.*

2. Mnyamata wake ndinetu,
Ndimvera mawu akewo;
Ndimpatsa mtima wonsewu
Ndimtumikira pansipa.
3. Kumwamba ndidza……….
Za chipangano chathucho,

Wamoyo sindimsiya ‘yi,
Nditafa ndinka kwawoko.

## 125

1. AMBUYANGA Yesu,
N’kukondani Inu;
Ndisiya zoipa
Chifukwa cha Inu.
Ambuye wabwino
Mundipulumutse konse;
Ndikonda tsopano
Koposa kale lonse.
2. Ndikonda chifukwa
Mnayamba kukonda;
Mnafera pamtengo,
Munandiwombola.
Mukhululukira
Zoipa zanga zonse;
Ndikonda tsopano
Koposa kale lonse.
3. Ndidzakukondani
Mwa moyo ndi m’imfa;
Ndidzakutamani;
Chikondi n’dzaimba.
Mpakatu ndidzafa,
N’dzanena nthaŵi zonse;
“Ndikonda tsopano
Koposa kale lonse.”

## 126

1. AMBUYE, m’imfamo
Munandikonda ine;
Sindikaniza ’Nu
Kanthu konse ’yi.
Ndimagwadira ’nu.
Ndikonda m’mtimamu,
Ndidzaperekatu
Nsembe yangayi.
2. Kumwamba kwanuko
Mundipempherere;
Ndikhulupirako,
N’dzalandiradi;
Ndisenze mtandawo,
Ndikhale mboniyo,
Ndiperekeko
Mitoloyi.
3. Ndikhumba mtimawo
Wofatsa ndithu,
Kuti ndiyambe ’ne
Ntchito zanuzi;
Akusokerawo,
Abwere kwawoko,
Inde,kwanutu.
4. Zambiri zangazo
Mnandipatsa kale,
Ndibweza zonsezi
Kwa Mbuyanga ’Nu;
Ndikadzaona ’Nu,
Mbuye wabwinotu,
33
Nsembe yokomatu
Ndidzakhalabe.

## 127

1. WAFUNAFUNA ine
Ambuye Yesuyo;
Wapeza ine ndithu
Wodwala m’mtimamo:
Zochimwa zanga zonsezo
Wachotsa izo zomwezo.
*E! chikondi ndithu,*
*E! chikondi ndithu,*
*Ndi chisomo chake chonsecho,*
*Ndi zozizwa zake zonsezo.*
2. Ndafoka ine kale
Ndafuna kufaku;
Zinthenda zangazo;
Ndi mwazi wake woti pyu!
Ndayera nawo m’mtimamu.
3. Mabala ake m’manja
Ndaona indetu,
Ndi minga ya pamutu
Yolasa Mbuyeyu;
Etu, wakonda inedi,
Pamtandapo kufera ’ne.
4. Ndikhumba ine ndithu
Madalo akewo;
Ndifuna kumyamika
Masiku onsewo;
Ndikafa ine pansipa,
Kumwamba ndizamtamanso.

## 128

1. AMBUYE Mulungu,

Ndikondwera maka,
Ndapeza chimwemwe
Ndi moyo wosatha.
*Aleluya, mlemekeze,*
*Aleluya, ndiye Mfumu;*
*Aleluya, mumpembedze*
*Ambuye Mulungu.*
2. Ambuyanga Yesu
Nandikhetsera mwazi,
Nakonza ine
Milandu yangayi.
3. Pamtanda woopsya
Adakandifera,
Natsika m'mtimanga
Mukhale moyera.
4. Tsopano Mulungu
Alandira ine,
Popeza Mbuyanga
Nawombola ine.
5. Padziko lapansi
Ndikumva chisoni,
Komatu kumwamba
Ndikhala ndi Mboni.

## 129

1. IMFA ndi mfumu ya mdimawo,
Anthu oipa imangawo,
Akhristu amapulumuka.
Omwe aimbira moyo,
Moyo ndi moyo ndi moyo,
Wosalekana ndi moyo
Wosamaliza Mulunguyo.
2. Yesu anafa pamtandapo,
Mzimu woipa nugomapo,
Ndi ife titame Mulungu.
Ndife tamasudwa m'moyo
Imfa ithedwa ndi moyo,
Tsiku lomaliza moyo
Wosamaliza Kumwambako.
3. M'mitima mwathu mwakhala mbee!
Mtambo wamdima wang'ambwa ke!
Panyanjapo pagawanika.
Ndife tipita ku moyo,
Mtima wabwino ndi moyo;
Kumbanda kucha kwa moyo
Kumatiuza za dzuŵalo.
4. Akumangidwa ndi mzimuwo,
Mudze ndi ife kwa Yesuko,
Akuchotsereni magoli,
Nadzakupatsani moyo,
Mlandu walipa ndi moyo,
Moyo ndi moyo ndi moyo,
Tambirana za moyowo.
34

## 130

1. ADALITSIKA munthuyo
Wopeza dalo lomwelo,
Chisomocho cha Mlunguyo
Chogwera m'Mpingo wakewo.
2. Chikhulupiro chomwenso
Chogweratu m'chikondicho;
Akhala nazo nzeruzi
Zofumatu mwa Mbuyedi.
3. Adalitsika, indetu,
Wodziŵa wadza Yesuyu
Nafera iye kalelo
Ampatse moyo wosatha.
4. Akondwerera nthaŵiyi
Pomvera mwini Mlungudi;
Mtendere ngwake panotu,
Nakhala nawo m'Mwambanso.

## 131

1. NDIDZIŴITSITSA Yesu ndi wanga,
Tsiku ndi tsiku ndimakondwera.
Anandigula ndi mwazi wake,
Anandipatsa Mzimu woyera.
*Mawu omwewo, nyimbo yomweyi,*
*Yesu ndimtama tsiku lonseli;*
*Mawu omwewo, nyimbo yomweyi,*
*Yesu ndimtama tsiku lonseli.*
2. N'kamvera Yesu ndikakondwera,
Ndiyang'anitsa nkhopeyo yake;
Ndipo angelo anditengera
Ine chisomo ndi chuma chake.
3. Ndine kapolo wa Mbuye wanga;
Andigwiritsa zintchito zake.
Ndimyembekeza adzabweranso,
Adzanditenga kwawo ndikhale

## 132

1. SINDINANYENGEDWA konse

Pakutsata Yesuyo;
Yesu apambana zonse
Ndinalingalirazo.
Pakuyenderana naye
Ndimamdziŵa ndi woona;
Ndifunitsa anthu onse
Adziŵenso Yesuyo!
Ndifunitsa anthu onse
Adziŵenso Yesuyo!
2. Sindinanyengedwa konse:
Yesu wachotsera phe!
Zakuchimwa zanga zonse
Zakupsinja mtimazo.
Yesu potsagana nane
Wandidzaza ndi mtendere;
Kundisunga, kundikonda
Sadzaleka konse 'yi!
Kundisunga, kundikonda,
Sadzaleka konse 'yi!
3. Sindinanyengedwa konse,
Yesu adzabwerabe;
Mtima wanga undiuza
Akuyandikiradi
Omwe sangamzindikire
Andinyoza nandijeda,
Koma Yesu ati zedi;
"Ine ndidzabweradi."
Koma Yesu ati zedi;
"Ine ndidzabweradi."
4. Sandinyenga, salephera;
Yesu wadalitse 'ne
Mpulumutsi ndi Myeretsi
Ndi Mchiritsi yemweyo
Wandiyanjanitsa naye,
Mtima wanga nakhutitsa;
Sindinanyengedwa konse,
Yesu akwaniradi!
Sindinanyengedwa konse,
Yesu akwaniradi!

## 133

1. MULUNGU wanga,
Ndapeza moyo;
Ndili wokondwera
Masiku onse.
*Aleluya, muyenera!*
*Aleluya, Amen.*
*Aleluya, ndidzamtama*
*Mulungu wanga.*
2. Mwazi wa Yesu
35
Unditsukatu,
Ndiye Mbuye wanga
Ndi Mpulumutsi.
3. Pamtanda wake
'Nafera ine,
Ndi zoipa zanga
'Nazichotsadi.
4. Mulungu wanga
Andilandira,
Chifukwa cha Yesu
Mwana wakeyo.
5. Adzabweranso
Kundilandira
Ndikhale ndi Iye
Masiku onse.

## 134

1. TILI ndi mtendere
Wopambanatu,
Monga ngati mtsinje
Mumitimamo;
Koma mtsinje uno
Umayenda phee,
Nthaŵi zonse mtima
Nutonthozabe.
*Tikakhulupira*
*Mlungu wathuyo,*
*Tidzaona mwayi*
*Ndi mtenderewo.*
2. Dzanja la Mulungu
Litisunga nji!
Nkhondo ya Satana
Sitiopa 'yi.
Zaphokoso zonse
Ndi zoopsyazo
Sizibvuta mtima,
Sizilowâmo.
3. Masauko athu
Ndi zokondwazo,
Azilola zonse
Ndi Atatewo.

Pokhulupirira
Tidzapezabe
Kuti mtima wake
Utikonda ’fe.

## 135

1. YESU ndiye Mbuye wanga,
Ndamva Mawu akewo
Andilandira ine,
Nandipulumutsatu.
*Mwalembedwa mukalata*
*Mawu ake omwewo,*
*Kuti iwo akumvera*
*Akalandiridwatu.*
2. Ndinakahala wakuipa,
Ndinamkana kalelo;
Koma Yesu waiŵala
Mphulupulu zangazo.
3. Wapumitsa mtima wanga,
Kaamba ndaphunziratu
Mau ake olembedwa
Mukalata mwakemo.
4. Mumvetu abwenzi athu,
Musakanirire ’yi;
Yesu aitana inu,
Zalembedwa zomwezi.

## 136

1. MTENDERE uli m’mtima mwathumu,
Chifukwa mwazi watitsuka mbuu!
2. Zakutsogolo sitidziŵa ’yi;
Adziŵa Yesu wathu zonsezi.
3. Abale angakhale m’talimo
Mbuyethu asungira onsewo.
4. Imfa ndi manda sitiopa ’yi,
Chifukwa Yesu wazithetsadi.
5. Mtendere wopambana m’Mwambamo
Pakufa ife tidzaonanso.

## 137

1. Ndiimba mumtima mokondwa
Ndi nyimbo yokoma, yoyera;
Ndiimba na Yesu Mbuyanga,
Anditonthora ‘na…………
*Chete! Chete!*
*M’tima mtendere ‘phee!*
*Udzera kwa Yesu wokonda*
*Mtendere mumtimamu.*

2. Pamtanda mbuyanga ‘nafera,
Akandichotsera zochimwa;
Anandigulira mtendere;
Anditonthoza ‘ne phee!
3. Pomlambira Yesu Mbuyanga,
Mumtima mtendere walowa;
Mdaliso woposa ndapeza,
Anditonthoza ‘ne phee!
4. Pokonda Yesuyo, mtendere!
Kanthawi kosatha, mtendere!
Potsata Mbuyanga apatsa
Mtendere mumtimamu.

## 138

1. KHALANI duu! Ambuye adzatu;
Senzani chete mtanda wanuwu;
Mulungu adzakonza zanuzo,
Sangasinthike mtima Iyeyu.
36
Khalani duu! Bwenzilo Yesuyo
Atsogolera m’njira mwathumu.
2. Khalani duu! Mulungu wanuyu
Akonzeratu nthaŵi zonsedi;
Musakayike mtima; zo’psyazo
Zimasulidwa pomalizapo.
Khalani duu! A Yesu Mawuwo
Ngamphamvu lero monga kalelo.
3. Khalani duu! pakufa mnzathuyo,
Pakumlirira ndi misoziyo;
Pa nthaŵizo abwera Yesutu,
Mitima yathu natonthozadi.
Khalani duu! Ambuye athadi
Kutibwezera zochotsedwazi.
4. Khaladi duu! pakufa ifetu,
Ndi Yesu tidzakhala indetu
Popanda mantha ndi zoŵaŵazi,
Chikondi chokha koma m’mtimamo.
Khalani duu! pakutha zonse phe
Tidzasonkhana tonse kuli ’Ye.

## 139

1. NAMONDWE akawombabe,
Mafunde akakulanso,
Palipo pobisala ’fe.
Ndi popemphera Yesuyo.
2. Paja athira Yesutu,
Chimwemwe muli m’manthamo,
Paja pokometsetsatu,
Mwazi wa Yesu nukhapo.
3. Pakulekana ifetu
Mitima ikomanapo;
Tikumbukana ’bwenzi ’fe,
Popempherana komweko.
4. Tidzathaŵira kuti ’fe
Pochita mantha nkhaŵanso?
Pakuyesedwa, tinke ku?
Tipemphe Yesu mphamvuyo.
5. Tikhale ndithu pomwepo;
Zapansi zisaloŵe ’yi.
Sitidzapempha m’Mwambamo;
Tidzayamika Mlungudi.

## 140

1. MULUNGU anditsogolera,
Ndapumula m’mtimamo;
Ayang’anira njira zanga
Nsiku zanga zonsezo.
*Mulungu anditsogolera*
*Nsiku zanga zonsezo;*
*Ndidzatsatira Mbuye wanga*
*M’njira mwake momwemo.*
2. Masiku ena pali mdima,
Ndivutidwa m’mtimamo;
Masiku ena ndikondwera
Ndi zabwino zangazo.
3. Masiku onse m’mtima mwanga
Ndili ndi mtenderewo,
Chifukwa ndimakhulupira
Mtsogoleri wangayo.

## 141

1. M’MENE ine ndisauka
Ndi zoipa zangazo,
Ndidzapita kwa Mulungu,
Adzandilandiratu.
*Mlungu adzandilandira,*
*Iye ndiye ’Tate wanga;*
*Watumiza Mwana wake*
*Andifere kalelo.*
2. Ngatitu abwenzi anga
Sandikonda ine ’yi,
Ndikhulupirire Mlungu,
Iye sandikana ’yi.
3. Pansi pano ndili mlendo,
Kwathu ndi Kumwambako;
M’mene ndimalira ine
Ndidzapita komweko.

## 142

1. MBUYANGA Yesu, mundigwire
Dzanja.
Kuyenda ndekha sindikwana ’yi;
Mukandigwira dzanja langa, Mbuye
Sindikaopa kanthu kena ’yi.
37
2. Mbuyanga Yesu, mundisunge ine
Pafupi ndi ’Nu nthaŵi yonseyo;
Ndikasoŵatu Inu, Mpulumutsi,
Ndingosekera m’talimo.
3. Mbuyanga Yesu, ndikapanda Inu
Ukadza mdima m’mtima mwangamu;
Koma ndinutu dzuŵa langa ndithu
Lakuwalitsa m’mtima momwemu.
4. Mbuyanga Yesu, mundigwire dzanja
Pamene ine ndimwalirapo.
Mkhaletu m’fupi nthaŵi yomwe Mbuye,
Mundiloŵetse ine m’Mwambamo.

## 143

1. NDIFUNA Inu, Yesu
Ndadzala ndi machimo,
Mumzimu muli mdima,
Ndikufatu m’katimo.
Ndifuna kutsukika
M’chitsimecho cha mwazi
Wa Inu wokondedwa,
Munandifera kale.
2. Ndifuna Inu, Yesu,
Lisoŵa bwenzi lina
Losungiritsa ine,
Londithandiza mwina.
Ndifuna mtima wanu
Wodziŵa nkhaŵa zanga,
Wondisezera mtolo
Wa tchimo lonse langa.

3. Ndifuna Inu, Yesu,
Ndimasauka ndithu,
M'ulendo andisoŵa
Kambayo wa padziko.
Ndifunanso chikondi
Cha Inu chondisunga,
Chakundisangalatsa
Panjira ponse panga.
4. Ndifuna Inu, Yesu,
Ndidzaonana nanu,
Mudzadza pamitambo
Ikhale mpando wanu;
Pamodzi ndi ananu
Ndidzakondwera kuti;
Ndilemekeze Inu,
Ambuye, Mpulumutsi.

# 144

1. Ndifuna yesuyo
Ambuyanga,
Mtendere ndinkemo
Mwa iyeyu.

*Ndifuna inu Yesu,*
*Nthawiyi ndifuna!*
*Kwa Yesu Mbuyathu*
*Ndifunako.*

2. Ndifuna Yesuyo
Mobvutamo,
Ndipulumukemo
Mwa iyeyu.
3. Ndifuna Yesuyo
Mokondwa ndi
Mowawa, adzemo
Ndi moyodi.
4. Ndifuna Yesuyo,
Ndichite 'ne
Zofuna zakezo,
Ndidzazabe.
5. Ndifuna Yesuyo
Woyeratu,
Ndikhale wakeyo
Wa iyeyu.

# 145

1. Mtima wa mbuyako
Ukukonda 'we;
Ndiye mukaona
Wopirirabe;
Ukasowa bwenzi,
Usaope 'yi;
Chikondano chake,
Chikwaniradi.
2. Akukumbukira
Yesu yemweyo;
Mkuyanjana naye
Muli moyomo.
Uderanji nkhawa!
Mpulumutsiyo
Atisamalira,
Atisungatu.
3. M'munda mwa Mbuyako
Muli ntchitomo;
Amithenga ake
Aigwirayo.
Usaime chabe,
Usakhale duu!
Yesu akufuna
Umthandizetu
4. Kwawo kwa Mbuyeko
Udzafikako;
Mwa ulemerero
Udzapuma 'phee!
Usalowerere,
Mvera Yesuyo,
Ati: "mwana wanga,
Bwera kwathuko."

# 146

1. PAMENE ndisauka,
Pamene ndivutidwa,
Mizimu yakuipa
Ikadza nindiyesa,
*Mulungu wanga,*
*Mwini mphamvu,*
*Mkandikumbukire 'ne.*
2. Pamene ndilemedwa
Ndi zakuipa zanga,
Poloŵa mdima m'mtima,
Pochita ine mantha,
3. Masiku anga onse
Mulungu mundisunge;

Pamene ndimwalira,
Ndi tsiku lomaliza,

# 147

1. KHALA chete mtima wanga
Mlungu wako ndiye Mfumu;
Zinthu zonse zisinthika,
Mlungu ndi wachikhalire.
*(Khala chete,*
*Chidzakupinga ninji?*
*Usaope,*
*Mulungu ali nawe.)*
2. Anthu onse pansi pano
Sakhutitsa mtima wawo;
Amadera zinthu zawo,
Namakhumba zakutali.
3. Khala chete mtima wanga,
Zikwanire zinthu zako;
Usakhumbe zapansipa
Koma Mlungu wako yekha.

# 148

1. NGATI mtima sumakonda
Yesu supumula bwino;
Mbuye, suwu mtima wanga,
Ndiwo wanu, mulandire.
38
2. Dziko lonse ndilitaya;
Ndikondetsa Yesu Mbuye;
An'komera kopambana
Andikondweretsa ndiye.
3. Ndakudani, mnandikonda
Ndi kukhetsa mwazi wanu.
Simuleka kundikonda;
Ine sindidzalekanso.
4. Mndisungire mtima wanga,
Uzikhulupira Inu,
Kuti moyo wanga wonse
Ubisaletu mwa Yesu.

# 149

1. NJIRA yanga sindiziŵa,
'Tate muikonza;
Komatu muzindikira
Kuti mundikonda.
2. M'mene mantha andigwira,
Andidetsa m'mtima,
Mbuye, ndithaŵire kwanu
Poti mundikonda.
3. Sindidziŵatu zamaŵa,
Koma sindiopa;
Ndidzakhulupira Inu
Kuti mundikonda.
4. Inde wakukonda ndinu;
Mawuwo oona
Andidzaza ndi chimwemwe:
Mlungu andikonda.

# 150

1. Odala ndi onsewo
Oyera m'mtima mwawo;
Adzaonana ndi Mulungu,
Yesu ndiye wawo.
2. Ambuye anachoka
Mumwamba, mwini moyo,
Wofatsa anakhala nafe,
Mfumu yachisomo.
3. Mumtima wakufatsa
Anaconda kukhalabe
Asankha mtima wakuyera,
Ndiwo nyumba yake.
4. Tifuna inu mbuye,
Mtininkhe mtima uwu
Wodzichepetsa, wakuyera,
Woyenera inu.

# 151

1. MNDIYANDIKITSE nanu. Yesu,
Ndiyenderane nanu;
E, nditsamire panu, Yesu,
Panjira yonseyi.
2. Ndionetsere kuunika
Kokoma kwanu, Yesu!
Yabwino mbiri ndibukitse
Yokondweretsayo.
3. Chitsime chakuyera ine
Ndifanefane nacho;
Mundigwiritse ntchito zanu
E! zanu zokhazo.
4. Mulamulire mtima, Yesu,
Ndi chifuniro changa;
Muloŵe mwanga ngati Mfumu;
Mundimveretsedi.

## 152

1. “KHALA mwa Ine,” Yesu anatero;
Mawu abwino, koma Mbuye wanga
Sin’ngathe ndekha, mukhalitse ine
Mwa ’Nu ndikhale nawo moyotu.
2. “Khale mwa Ine,” munachotsa tsoka,
Mletse Satana anganyenge ine:
Mibvi yamoto yake muizime
M’mtimamo, ndikhulupirire ’Nu.
3. “Khala mwa Ine,” ndinu mwini mphamvu,
Mundithandize ine ndikafoka;
Mzimu Woyera andiululire
Zoona zanu m’mtima mwangamu.
4. “Khala mwa Ine,” ndinu mwini moyo.
Nthambi zouma zidulidwa m’mtengo: Ine wopanda Inu ndifokanso,
Zipatso zikasoŵa msadze ’ne.
5. “Khala mwa Ine,” Mbuye, ndifunitsa;
Mzimu Woyera mlonge m’mtima mwanga,
Akagonjetsetu machimo anga,
Mtima woyera andipatsenso.

## 153

1. AMBUYE mundisunge
Pafupi ndinutu;
Palibe malo pena
Popuma pansipa.
Adani andizinga,
Zoipa m’katimo;
Chifundo chanu Yesu
Chikonze m’mtimamo.
2. Ndikabisala mwanu
Ndilibe mantha ’yi;
Ndikasungidwa kwanu
Mumtima muti phee!
Ndi mphamvu yanu yokha
39
Ndiposa ’daniwo;
Chifundo chanu Mbuye
Chitchinjirize ’ne
3. Ndidzaonana nanu
Mokondwakondwadi.
Oyera mtima onse
Apenya Mbuyeyo.
Kumwamba n’dzaimbira
Kukoma kwanuku;
N’dzatama nthaŵi zonse
Chikondi chanucho.

## 154

1. KHALATU woyera, pempheratu m’tseri;
Werengani Mawu masiku onsewo.
Uthenga omwe ali akufoka,
Madalitso ake ufunefunebe.
2. Khalani woyera, dziko laipadi;
Pemphera kolimba kwa Yesu Mbuyathu.
Yang’anitsa Yesu ndi kumutsatira,
Kuti anthu ena aonenso Iye.
3. Khalatu woyera, akutsogozetu;
Usamtsogolere munjira zakozo.
Pokondwa ndi m’nsoni tsata Ambuyako
Khulupira Yesu ndi Mawu akewo.
4. Khalatu woyera, khalatu wofatsa;
Alilamulire ganizo lakolo.
Utatsogozedwa ndi Mzimu wakeyo,
Msanga udzagwira m’Mwamba ntchito yake.

## 155

1. MUDZAZE Yesu mtima wanga ndi chikondicho,
Ukhazikike pa Mulungu wosachokapo.
2. Mwa ine myatse moto wanu waku yera mbuu,
Utenthemo zoipa zonse zidakhalamo.
3. Mubweretu nomwe ’Nu munatsika kalelo;
Ndilira Inu mundidzaze mphamvu yanuyo.
4. Ndikhazikike inetu, mumtima muli mwai,
Ndi Yesu ndikondanetu, si kanthu kena ai.

## 156

1. MBUYE ndamva mwawazira
Anthu ena madalitso;
Mvula yanu yawagwera;
Mbuye, ine mudalitse.

*Etu ine, etu ine,*
*Mbuye, ine mudalitse.*
2. ’Tate, msandipitirire,
Ndimaipa mtima ine;
Ndiyenera munditaye,
Koma mukhulukukire.
3. Yesu, msandipitirire
Kuti ndinu ndikondane;
Ndinalira Inu Mbuye,
Msandileke poitana.
4. Mzimu, msandipitirire,
Mupenyetsatu akhungu
Mboniyo ya Mbuye Yesu,
Mundipatse ine mphamvu.
5. Ndinagona mwa zoipa,
Ndinakunyozani ine,
Dziko lino ndinakonda,
Mbuye, mukhululukire.
6. Ha! chikondi cha Mulungu,
Mwazi wa Mbuyathu Yesu,
Chiyanjano cha Mzimuyo
Zonse zidzalemekeza.

# 157

1. AMBUYE, thandizenitu
Ndi mphamvu zanuzo;
Pantchito zathu zonsezi
Mthandize Mbuyathu.
2. Zochimwa zathu m’mtimamo
Tilira nazotu;
Mumtima mwathu muti zii;
Mthandize Mbuyathu.
40
3. Mthandize Mbuye, timvetu,
Tikalandiredi
Zimene muperekazo
Zakudalitsa ’fe.
4. Kumwamba Yesu mthandize,
Tilibe wina ’yi:
M’moyo, muimfa mthandize,
Tikhale kwanuko.

# 158

1. POKHALA mtendere mu mtimangamu,
Pamene ndisaukanso,
Pamene mabvuto ndi akuludi,
Moyo wangawu ngwabwinotu.
*Moyowo*
*Ngwabwino,*
*Moyo wanga ulitu bwino.*
2. Ngakhale Satana andizunza ’ne,
Chilipo chitonthozacho;
Chifundo cha Kristu anafera ’ne,
Kundipatsa ’ne moyo wake.
3. Uchimo unapachikidwa pomwe
Pamtanda wa Yesu Mbuye;
Machimo angawo anatherapo;
Mbuye wanga, ndiyamika ’Nu.
4. Ambuyathu, ndikhumba tsiku lija
Limene ndidzaona ’Nu;
Lipenga limveke, ndidzakondwatu
Pakukomana ndi Yesuyo.

# 159

1. NDILIRA ine kukayenda
M’njira ndi Mulungu;
Ndilira nyali ndikaone
Njira Ya kwa Yesu.
2. Chimwemwe chija chamumtima
Ndinalaŵa kale
Poyambutsata ine Yesu,
Chili kuti tere?
3. Kalelo m’mtima ndinakondwa,
Tere ndingolira,
Zokoma zonse zapadziko
Sizindikwanira.
4. Mubwere, Mzimu wa mpumulo,
Mundileze m’kati;
Ndidana nazo zoipazo
Zinakuchotsani.
5. Mundichotsere tchimo lonse
Ndinakonda kale,
E, muligwetse kuti ndinu
Mfumu mukakhale.
6. Mkatero ndidzayenda m’njira
Ndi Mulungu wanga,
Idzandiunikira nyali
Njira ya Kumwamba.

# 160

1. NDILIRA mtima wotamanda
Mlungu, ndi woyera,
E, mtima woyamika mwazi

Munandikhetsera.
2. Mtimatu wopirira ndi
Wofatsa mkati mwake,
Mumveka Mbuye Yesu yekha,
Ndiye Mfumu yake.
3. Ndilira mtima wakulapa
Ndi womvera Yesu,
Wosasiyana ndi Ambuye
Wakukhala m’mwemo.
4. E, mtima watsopano ndi
Wodzala ndi chikondi,
Wangwiro ndi wokoma, Mbuye,
Wonga wanu wonse.
5. Mkhalidwe wanu mundipatse
Ndifanane nanu
Mulembe m’mtima mwanga Dzina
La chikondi chanu.

## 161

1. Zoipa zangazi
Zidetsa m’mtimamu;
Mnditsuke, Yesutu,
Kutsuka koti mbuu!
41
2. Ndafoka inetu,
Ndalema m’mtimamu;
Andilimbitsa ’Ye,
Kulimba koti njo!
3. Zin’soŵa indedi
Zabwino m’mtimamu;
Ambuye, mdzazebe,
Kudzaza koti tho!

## 162

1. AMBUYE, ndifuna nditsukenitu;
Mukhalire ndine mumtimangamu;
Muthyole zonsezo zodetsa ’netu;
Musambitse ine, ndiyeretu mbuu!
*Ndiyere mbuu! E, ndiyere mbuu!*
*Musambitse ine, ndiyeretu mbuu!*
2. Ambuye, chotsani zonse zomwezo
Zakundisautsa mumtimangamu;
Ndileke zangazo zoipsa ’netu
Musambitse ine, ndiyeretu mbuu!
3. Kumwamba ndiona Ambuyangayo,
Mudzandithandiza, nditsate ’nemo;
Mudzandichotsera zoletsa ’netu;
Musambitse ine, ndiyeretu mbuu!
4. Chifukwa cha ichi ndipempheratu,
Ndidikira Inu Ambuyangayu;
Ndikhulupirira pa mwaziwo pyu!
Musambitse ine, ndiyeretu mbuu!

## 163

1. USAFUNE, chuma chokha,
Pena maseŵera okha,
Koma za Mulungu zokha
Zipambana zinazo.
2. Ukafuna kulemera,
Pempha chuma chosathera,
Ndiwo mtima wakuyera
Ndi wokonda Yesuyo.
3. Zosauka ubvomere,
Ndipo Yesu chaulere
Chikondano ndi mtendere
Aloŵetsa m’mtimamo.
4. Zonse umazinyadira
Udzaleka kusirira;
Uli nazo zokwanira
Pakupeza Yesuyo.
5. Mbiri yake ubukitse,
Anthu onse nuphuzitse,
Kwa Mulungu nufikitse
Osokera onsewo.
6. Yesu sakusiya konse;
Mphamvu, nzeru, chuma chonse
Akupatsa nsiku zonse;
Tsata Yesu yekhayo.

## 164

1. MKRISTU, ulimbike
M’ntchito yakeyo;
Yesu anafera
Anthu akewo.
2. Mphamvu zathu zonse
Tionetsenso,
Kuti kudziŵike
Tili akewo.
3. Mtima wakufatsa
Amakondako;
Ndipo anthu onse
Angatengero.
4. Mapemphero athu
Tikakwezebe,

Dzina lake lomwe
Tiyamike ’fe.
5. Limbikani nonse
Mpaka imfayo.
Ndipo Mfumu yathu
Idzakondwako.

## 165

1. GWIRA zintchito zako,
Pomva usiku udza;
Yamba mamaŵa ndithu
Potuluka dzuŵa.
Gwiranso m’msana monse
Dzuŵalo likatentha;
Gwira tsopano ntchito;
Msanga udzaleka.
42
2. Ntchito za Yesu gwira
Pomva usiku udza;
Lero lonseli gwira,
Bwino udzapuma.
Gwiratu tsiku lonse
Ntchito zakuyenera;
Gwira tsopano ntchito,
Tere udzaleka.
3. Mkristu gwiratu ntchito
Pomva usiku udza;
Dzuŵalo lopendeka
Tere lidzaloŵa.
Gwiranso ’dzulodzulo
Kutada mdima bii!
Tsono zintchito zonse
Zatha zonsezi.

## 166

1. TITHAŴIRENJI ifetu
Mphamvu za Yesu nzathunso.
Kristu atithangatatu.
M’nkhondo ya moyo wathuyo.
2. Yendani bwino m’njiramo
Ya kwa Mulungu wathuyo;
Kwezani maso kuli ’Ye;
Kristu ndi njira yomweyo
3. Nkhaŵa tilbe; Yesuyo
Atsogolera m’njiramo;
Tikhulupire Iyeyo,
Kristu ndi moyo wathuwo.
4. Tioperanji ifetu?
Ali pafupi Mbuyeyu;
Sangasinthike mtima ’yi;
Kristu akonda ifetu.

## 167

1. MBUYE, nditsate bwanjiko?
Ine ndikonde bwanjinso?
Bwanji kuyenda m’njiramo
Yonka Kumwamba kwawoko?
2. Kodi m’njiramo ndimvadi
Nsoni zoŵaŵa, nkhaŵazi
Ndi masauko, mingayi?
E, nkana izi n’tsatabe.
3. Anasauka Mbuyeyo,
Mwini nalola zonsezo;
Anatsiriza ntchitozo,
Osabwerera imfayo.
4. Ndikamayenda m’dimamo,
Mletse zodandaulazo;
Mundikumbutse mtandawo;
Zanga zichepa zonsezo.
5. Ine nditaya chumacho,
Ndikondweretse Mbuyeyo,
Thupi liopa mingayo,
Koma mlimbitse mtimawo.

## 168

1. YESU, afuna iwe unke kwawoko,
Loŵa m’njira yake yakuyerayeratu;
Anadzera m’Mwamba kutiperekezako;
Yamba msanga iwe kunka kwanuko.
*Tsata, tsata, nditsatadi Yesu;*
*Iwetu, iwetu, ukatsatanso.*
*Tsata, tsata, nditsatadi Yesu;*
*Inu nonse mukatsate Mbuyeyo*
2. Ngati umtsata Mpulumutsi wakoyo,
Udzakhaliranso kuli Mbuye wakoyo;
Adzapulumutsa thupi, mzimu wakonso,
M’mphamvu ndi chilango cha zoipazo.
3. Kunsi kudambo, pena m’mwamba m’phirimo,
Pomwe pali Yesu ndidzayenda yendapo:
Andiperekeza bwino m’njira yakeyo,
Kuli Mzinda wa Mulungu wangayo.

## 169

1. MBUYE, mwatiuza 'fe
Tizikhala mchere
Wokometsa onsewo
Akumanga kwathu.
Mcherewu ndi ifetu;
Mtifanize nanu,
Tikakope ndi chitsanzo
Onse akuchimwa.
2. Mbuye, mwatiuza 'fe
43
Tizikhala nyali
Yoonetsa onsewo
Njira yonka kwanu.
Nyali ndi ifetu;
Kuunika kwanu
Mutipatse tiŵalire
Osokera onse.
3. Tisasungaluke 'yi,
Tisasiye Yesu.
Tisabise nyaliyi
Pakuchita mantha.
Mcheretu ndi nyaliyi
Tizikhala tonse;
Mbuye, mtiyeretse m'mtima
Tikatero ndithu.

## 170

1. M'MAŴA tizifesa
Mbewu zakukoma,
Msana ndi usiku
Tizifesa momwe.
Nyengo yamasika
Tidzatema m'munda,
Tidzabwera tonse
Ndi zipatsozo.
*Ndi zipatsozo*
*Ndi zipatsozo*
*Tidzabwera tonse*
*Ndi zipatsozo.*
2. Tizifesa m'dzuŵa
Tizifesa m'mthunzi,
Sitiopa ife
Mtambo ndi chisanu.
Athatu masika
Ntchitozi zidzatha;
Tidzabwera tonse
Ndi zipatsozo.
3. Tingolira kaya,
Koma tidzafesa
Mbewu za Ambuye;
Ntchitoyo nja Yesu.
Adzachotsa msozi,
Adzatilandira,
Tidzabwera tonse
Ndi zipatsozo.

## 171

1. M'MENE umauka m'maŵa,
Sunagwire ntchitozo,
Sunayambe kukayenda,
Ugwadire Mlunguyo.
Pena uli kusekera,
Pena nkhaŵa m'mtimamo,
Wachimwemwe, wachisoni,
Uza Yesu zonsezo.
2. Wakuchezacheza naye
Ukagwira ntchitozo;
Pakukumbukira Yesu,
Nkhaŵa zidzachokanso
Ndi zapansi zikafuna
Kukudzaza m'mtimamo,
Utsogole kopemphera,
Uza Yesu zonsezo.
3. Ndi m'kutero udzadziŵa
Chifuniro chakecho;
Iye adzakuthandiza
Uthangate enanso:
Ndi ofoka ulimbitse,
Akulapa bwezatu;
Ndi za ntchito zake izi
Uza Yesu zonsezo.
4. Ndipo ngati ungolema,
Ulefuka m'dzulomo,
Ndi Satana akayesa
Kukukola m'mtimamo:
Wakufoka, wakuopa,
Penyetsetsa Iyeyo;
Udzakhazikika m'mtima
Pakumuza zonsezo.

## 172

1. HAYA! 'nzanga taonani

Yoonekayo
Yakumwamba iti: “Yesu
Alikudzako.”
*Kanganani nkhondo yanu*
*Ndi mbendera mbuu!*
*Tibvomere: ‘Inde Mbuye*
*Mtithangatetu.”*
2. A! mizimu yakuipa
Isautsabe,
44
Tikaniza zakuipa
Zotizinga ’fe.
3. Mdani adza nazo mphamvu,
Koma ifetu
Tidzamthetsa nkhondo yake
Timwingitsetu.
4. Yesu ati, “Ndidza msanga!”
Thangateni phee!
Mbweze mawu akulimba:
Tikanganabe.

# 173

1. ANATILEMBA Yesu tikagwire nkhondo yake,
Natilimbitsa tipirire osaopa kanthu.
Kwa Satana n’ziwembu zake
Sitigonja konse;
Tiyenderana naye Mfumu
yathu yopambana.
2. Amaliwongo ochuluka amaloŵa m’mtima
Nafuna kuipitsa usana ndi usiku;
Tikatsatabe Mfumu yathu
Sitidzagwa konse,
Pakuti atipatsa mphamvu
tipambane nazo.
3. Amatininkha zida zoteteza mtima, Ndizo;
Kupempherabe, kukhulupirira ndi kufatsa;
Mtheradi, ndi lupanga ndilo
Mawu a Mulungu;
Pogwira zida zakezi sitilephera konse.
4. Mafumu atiuza tikaletse ukapolo,
Ndi kumasula goli la anzathu akuopa
Tiyeni, tiŵauze za Mbuyathu
Mpulumutsi
Nitiŵanditse mbiri yake
M’dziko lonse lathu.

# 174

1. LIMBA mtima mbale wanga
Usapunthwe m’njirayi;
Onatu nyenyezi ija
Ikutsogoleradi.
Tamveratu Mlungu yekha,
Chita zolungama ’we,
Yenda bwino, khulupirira
Mbuyeyo, Mbuyeyo,
Ndikuchita zakezi.
2. Taya zako zochenjera,
Taya zamumdimanso;
Nthaŵi zonse khulupira,
Chita zolungamazo.
Usayang’anire wina
M’khondo yake yomweyi,
Koma m’zonse khulupirira
Mbuyeyo, Mbuyeyo,
Ndi kuchita zakezi.
3. Leka zakuipa zako,
Myambi yonse yoti bii,
Usakhulupire mommo:
Tamveradi Mbuyedi.
Adzadana nawe ena,
Ena adzakonda ’we;
Kweza maso, khulupirira
Mbuyeyo, Mbuyeyo
Ndikuchita zakezi.
4. Mawu ake atipatsa
Mphamvu ndi mtenderenso,
Bwino atitsogolera,
Tikhulupirira ’wo
Limba mtima, usapunthwe
M’njira yamumdimayi;
Yenda bwino, khulupirira
Mbuyeyo, Mbuyeyo,
Ndi kuchita zakezi.

# 175

1. POYESEDWA ine
Yesu mudzetu,
Mundipempherere

Ndisachimwetu.
Mukaona kuti
Ndilefukatu,
Mbuye mndilimbitse
Nazo mphamvutu.
2. Ndi zapansi pano
Ndikokedwadi,
Koma ndi chisoni
Mndiphunzitsedi;
Ndisaiŵalire
45
Za Getsemane,
Pena mtanda wanu
Yesu Mbuye ’Nu.
3. Mukandipweteka,
Ndipirirapo:
Nsembe yanga ndiyo,
Landirani ’yo.
Ndikachita mantha
Sindithaŵa ’yi:
Mtima udzalimba,
Ndidzaima nji!
4. Pakumalizidwa
Moyo wangawu,
Pomwalira ine,
Mudze Mbuyetu.
Ndidzadzipereka
M’manja mwanumo:
Mpulumutsi Yesu
Mndilandireko.

# 176

1. AMBUYE wa Kumwamba,
Mundithangatetu
Kuyenda bwino lomwe
M’ulendo unowu.
Kaŵiri ndi kaŵiri
Ndipunthwa m’njiramo
Mlimbitse mtima wanga,
Ndingatayikeko.
2. Ndikhumba Mzimu wanu
Kundiyeretsa mbuu!
Pang’ono ndi pang’ono
Mundiphunzitsetu;
Ndifuna nzeru zanu
Zakundifitsako
Kumwamba kuli Inu,
Ambuye wangayo.
3. Yochita ndi yodikha
Mupatse mphamvuyo,
Ndikhale wochenjera,
Wogwira ntchitozo.
Zoipa zanga zonse
Mufafanizezo,
Ndiyende nanu nokha
Masiku onsewo.

# 177

1. TIYENI Akhristu,
Nkhondo tigwire;
Yesu Mbuye wathu
Atitsogolera.
Mfumu yathu mwini
Atipatsa moyo;
Taonanitu mbendera
Yailoŵa nkhondo!
*Tiyeni Akristu,*
*Nkhondo tiigwire;*
*Yesu Mbuye wathu*
*Atitsogolera*
2. Nkhondo ya Satana
Idzakuthaŵani;
Tiyeni Akristu,
Kaipambaneni.
Idzanjenjemera
Mukapfu’litsatu;
Imbitsanitu anzathu,
Mau mukwezetse.
3. Mpingo wa Mulungu
Uli ngati nkhondo;
Titsagane nawo
Ana a Mulungu.
Sitipatukana,
Ndifetu amodzi;
Ch’yembekezo, chikondano,
Chonse ndi chimodzi.
4. Zonse zapadziko
Zidzamalizira,
Koma mpingo wake
Uli chikhalire;
Udzakhala ndithu
Mphamvu za Satana,

Yesu analonjezetsa,
Mawuwo sakana.
5. Tiyeni anzathu
Tizithandizana;
Imbirani nafe
Nyimbo zopambana
Kristu ayenera
Mphamvu ndi ulemu;
Komwe kuli Yesu.
46

## 178

1. TIYENI, Akristu inu,
Mumenyane nkhondo iyi,
Mukafoka nonse, koma
Yesu akulimbitsani.
2. Muyendanso kunka komwe,
Mugonjetse mdani wanu;
Musafoke, musaleme,
Musagone konse inu.
3. Musagonje, anthu inu,
Mtamiretu Yekha Mbuye;
Ipambana mphamvu yake,
Ya Mtsogoli wanu yemwe.
4. Mtima wanu wonse ndithu
Udzakhala ndi chimwemwe.
Zida zanu mbvale bwino
Zakudzera m'Mwamba momwe.
5. Limbikani inu nonse,
Msangalalo ngwanu nokha;
Musaope kanthu kena
Mumtamire Mbuye Yekha.
6. Tiyeni ku nkhondo iyi,
Mugonjetse zonse konko;
Muingitse mdani uja,
Muyendetse m'njira momwe.

## 179

1. AKRISTU limbikani,
Imani mtima nji!
Mbendera nyamulani,
Msatenthemere 'yi.
Wotsogolera wathu
Ndi Mwana wa Mulungu;
Adzagonjetsa onse
Adani athuwo.
2. Tigwire nkhondo yomwe
Ya Mbuye wathuyo;
Tileke zakuipa
Zokhala m'mtimamo.
Sitikwanira tokha
Kuleka zathu zomwe,
Koma Mbuyathu Yesu
Atithangatatu.
3. Tsopano timenyana
Ndi zakuipazi;
Pamene nkhondo yatha
Tidzanka kwathuko.
Yesu adzalandira
Ankhondo ake onse;
Adzakhalika naye
Kumwamba komweko.

## 180

1. MBUYE, ndapangana
M'njira yanuyi,
Kuti ndidzayenda
Osaleka 'yi.
Mundipatse mtima
Wopiriramo,
Wakukana zonse
Zondipingazo.
2. Mzimu wakuipa
Undiyesa 'ne;
Mundithangatire
Ku'thaŵitsabe.
Akandisautsa
Kum'dzi kunoku,
Muloŵetse mphamvu
M'mtima mwangamu.
3. Akathira nsembe
Ku mizimuyo,
Ndipenyera kwanu,
E, Kumwambako.
Tsoka ndi zonyenga
Za ufitizo,
Yesu mndilimbitse
Ndisaopezo.
4. Pena kumwa nawo,
Ndisateroko,
Pena kukaona
Gule woipa,
Pena kuwombeza

Sindifuna ’yi;
Yesu mundithandize
Kuzikanazi.
5. Ndinu mbusa wanga;
Mndithandizetu;
Ndisaipse nazo
47
Mtima wangawu.
Osaopa konse,
Osachimwa ’yi.
Mundiyendetse Yesu
M’njira yanuyi.

# 181

1. AULENDO, munka kuti Ndi
zindodo m’manja mwanu?
Paulendo tizipita;
Aitana Mbuye wathu;
Pamapiri, pamadambo
Tizipita komwe kwawo.
Tizipita komwe kwawo
Kuli dzikolo labwino,
Tizipita komwe kwawo
Kuli dzikolo labwino.
2. Kodi simuopa njira,
Inu anthu akufoka?
Ayi, atiperekeza
Mbuye wathu wotikonda.
Iye amakhala nafe,
Natitsogolera ife.
Atitsogolera ife
Kuli dzikolo labwino.
Atitsogolera ife
Kuli dzikolo labwino.
3. Mundiuze, aulendo,
Muli chiani m’Mwamba muja?
Atibvekako zoyera
Akorona natininkha;
Moyo, moyo atipatsa,
Kwa Mulungu tidzakhala.
Kwa Mulungu tidzakhala
Kuli dzikolo labwino,
Kwa Mulungu tidzakhala
Kuli dzikolo labwino.
4. Kodi inu, aulendo,
Ife titsagane nanu?
Inde, mudze inu nonse,
Mudze nafe paulendo.
Inde, mutiperekeze,
Yesu atilinda ife.
Yesu atilinda ife
Kuli dzikolo labwino,
Yesu atilinda ife
Kuli dzikolo labwino.

# 182

1. ANA akumwamba ndife,
Paulendo timaimba;
Timatama Mbuye wathu
Wa ulemerero wonse.
*Tilikupita kwathu kuja*
*Munjira ya atate athu,*
*Amakondwera lero lomwe;*
*Tinka kuonana nawo.*
*2.* Mbuye anatiitana
Kukagwira ntchito yake,
Kuitana anthu onse
Atsatenso njira yino.
3. Inde Mbuye, tibweradi,
Zathu zonse tizisiya,
Mtsogoleri wathu ndinu
Titsatabe inu nokha.

# 183

1. MBUYE munditsogolere,
Ndine mlendo m’dziko muno;
Ndikafoka mundikweze,
Mundisunge m’manja mwanu;
Mundidyetse, mundidyetse,
Sindingamve njalayo.
2. Mundimwetse madzi anu,
Andichize nthenda zanga;
Utsogole mtambo wanu,
Ndikadziŵe njira yanga;
Mpulumutsi, Mpulumutsi,
Munditchinjirizetu.
3. Ndikaloŵa m’mtsinje muja,
Mndichotsere mantha osne;
Mndiwolotse tsidya lija,
Ndikondwere nthaŵi zonse;
Nyimbo zanga, nyimbo zanga
Zidzalemekeza ’Nu.

## 184

1. NDIMAYENDA paulendo
Ndi yaminga njira yake;
Tsoka ndikapeza, koma
Ndinka kwa Atate;
48
Pena m'mtima mwanga mwada,
Pena andibvuta 'dani,
Ndikatenga nkhaŵa, mantha,
Amadziŵako.
2. Ichi chindisangalatsa
M'mene nkhondo indigwira,
M'mene nsoni zazikulu
Zimanditsatira;
Mtima ukhazika m'mene
Kwathu kuja ndikumbuka
Kuti Mlungu ali ndine,
Andisungako.
3. Mbuye andipeza lero,
Andikonda, andisunga;
Adzapitikitsa mdani
Akamandibvuta.
E, ulendo wanga utha,
Tsono ine ndimwalira;
M'mene ndidzafika kwawo
And'landirako.
4. Komwe ndi chimwemwe ine
N'dzaonana ndi Atate,
N'dzagwadira ndi kumtama,
Amandikondabe.
Sakandisautsa kanthu
M'dziko lija lakukoma;
Adzandidalitsa Yesu,
Ndidzakondwako.

## 185

1. MUNDIŴALIRE m'njira mwangamo,
Mbuyanga 'Nu.
Kwada usiku, ndasokerako,
Mtsogoletu.
Phazi langali mndisungirenso,
Ndilonde Inu m'njira monsemo.
2. Sindidapempha kale Mbuye 'yi,
Mtsogole 'Nu;
Ndisankha ndine, koma leroli
Nditsatatu.
Ndidadzikuza osaopa 'yi;
Ambuye, msakumbuke zomwezi.
3. Ndi kale lonse mnandisunga 'ne;
Tsopanonso.
M'khwawâ, paphiri, mundisungebe
M'tsogolomo.
Ndipo mamaŵa n'dzaonana ndi
Abale anga adafikadi.

## 186

1. TIYENI nonsenu okonda YESUYO,
Tiimbe nyimbo yabwino,
Tiimbe nyimbo yabwino,
Ku mpando wakewo,
Kumpando wakewo.
*Tiyeni pamodzi*
*Tilikupita Kumwamba;*
*Akristu tilikupita*
*Ku mzinda wa Mlungu.*
2. Ngakhale enawo aleke kwimbako,
Akristu 'fe tidzaimba,
Akristu 'fe tidzaimba,
Kumlemekeza 'Ye,
Kumlemekeza 'Ye.
3. Akristu tonsefe, tikondwe m'Dzikoli
Koposa anthu enawo,
Koposa anthu enawo,
Tisanafikeko,
Tisanafikeko.
4. Tiimbe mokondwa, misozi iume;
Poyenda kunka kwathuko,
Poyenda kunka kwathuko,
Kwa Mlungu wathuyo,
Kwa Mlungu wathuyo.

## 187

1. NDAMVATU kuti tifika komweko
Kuli Ambuye, Mtetezi wathuyo.
Ine, pakutha zobvuta zathuzo
Iye tidzamwona maso ndi maso.
*Ndi Mbuyeyo tikhalamo,*
*Kupenyanso wokondatu;*
*Tidzakondwera, E, nthaŵi zonsezo*
*Ndicho chimwemwe ndi ulemutu.*
2. Kaamba chisomo cha Mbuyathu uyu,

Malo okoma tipeza m'Mwambamo;
Kumva mtetezi amene ndi Yesu,
49
Ndicho chimwemwe ndi chachikulutu.
3. Onse aliko takonda kalelo,
Kale napita kwa Yesu Mbuyawo;
Koma kumwona Mtetezi wathuyo
Ndicho chimwemwe choposa, nchathucho.

## 188

1. UKATHA moyo wanga
Kumwamba kundichera;
Dzuŵalo ndimalira
Lafika lokomera.
Usiku m'nali mdima,
Tsopano mbanda kucha;
Kudzaŵalitsa ndithu
Ku Dziko la Mulungu.
2. Chitsime chachikondi
Ndi Yesu Mbuye wanga;
Ndalaŵa mtsinje pano
Ndzamwetsa ine m'Mwamba.
Komweko zidzakula
Chisomo ndi chifundo,
Pondiŵalira kuja
Ku Dziko la Mulungu.
3. A! Yesu Bwenzi langa
Inenso bwenzi lake,
Woipa 'ne alola
Ndilowe m'nyumba mwake;
Ndikhulupira Iye
Achotsa mphulupulu;
Kudzandiŵalitsira
Ku Dziko la Mulungu.
4. Ambuye andisunga
M'chifundo chachikulu;
Zisoni zisanduka
Chimwemwe cha Mulungu.
Dzanjalo ndilitama
Ndi mtima wachifundo,
Mpakatu kwaŵalitsa
Ku Dziko la Mulungu.

## 189

1. TIKAGWIDWA ndi chisoni,
Ikayendanso misozi,
Poliriratu abale,
Yesu mutimveretu.
2. Munabvala thupi lathu,
Munadziŵa masauko,
Mnalirira bwenzi lanu;
Yesu mutimveretu.
3. M'mene imfa yathu idza,
Mweya wathu ukaleka,
M'mene ife timwalira,
Yesu mutimveretu.
4. Mnamwalira Inu paja,
Mwazi wanu munakhetsa,
Koma Inu munadzuka;
Yesu mutimveretu.
5. Mtima ukachita nkhaŵa
Ndi zoipa zotimanga,
M'mene tikachita mantha,
Yesu mutimveretu.

## 190

1. KODI uli ndi chisoni
Choliritsa mtima wako?
Kweza maso, ndi Atate
Akumvetsa zonsezi.
2. Kodi umadandaula;
"Mbale wanga waferanji?"
Kumbukira Wakumtenga
Saphophonya konse 'yi.
3. Mbale wako unamkonda,
Koma Yesu amkondetsa;
Anamfuna nagomtenga;
Usammane Yesu'yi
4. Pakutsazikana nanu
Ndi potseka maso ake,
Imfa, bii! Anangogona
Koma adzadzukanso.
5. Usalire; Mpulumutsi
Analaŵa imfa Yekha;
Imfa yomwe nagonjetsa
Potuluka m'mandamo.
6. Chikondano sichifera;
Mbale wako udzamwona
Kwathu komwe; zipirira
50
Mpaka ukafikako.
7. Leroli chisoni chokha,

Tsiku lija kungokondwa;
Kweza maso osalira,
Yesu akukondadi.

## 191

1. NTCHITO yonse yakeyo
Yatha m'dzikoli linoli
Mlendo wafikatuko
Pokocheza leroli.
*'Tate, mwa kusunga kwanu*
*Timusiya mwana wanu.*
*'Tate, mwa kusunga kwanu*
*Timusiya mwana wanu.*
2. Yathatu misoziyo
Zobisika zonse mbee!
Aweruza bwinoko
Ndiye Wolungamayo.
3. Komwe Mbusa kwawoko
Atengera nkhosa zonse,
Zake asungiramo
Zosaopa kanthu konse.
4. Onse akulapawo
Ayang'ana mtanda wake;
Aphunzira komweko
Zonse za kukonda kwake.
5. Dothili kudothilo,
Pfumbili kupfumbi tere;
Mpaka adzadzukanso
Timusiya mumtendere.

## 192

1. MUMZINDA wa Mulungu
Moyera mulimo,
Ndiye amathu omwe
Olera ifewo;
Mitima yathu yomwe
Ikondwereratu,
Nikhala nawo Mzinda
Wakukongolawu.
2. Akondwerera anthu
Zokoma zonsezi
Za midzi ya padziko
Lapansi lonseli;
Mtendere wake koma
Wa Mzinda wathuwo
Upambanditsa zonse
Zapansi pomwepo.
3. Ndi nkhondo ikaleka
Kwa Mlungu komweko,
Ndi ukapolo watha,
Udani wathanso;
Ndi zakuopsa zonse
Ndi zosauka zii!
Ndi mwayi wa kwa Mlungu
Udzoza mutu tho!

## 193

1. Nlokoma dziko langa!
Ndiyang'anirapo,
Ndilira ndi chikondi
Poona dzinalo;
Pakumva mbiri yanu
Mumtima muti duu!
Ndi moyo ndi mtendere
Imalowetsamo.
2. Mokhala mokhamokha
Mokondwa momwemo;
Misozi yatha yonse,
Angosekeramo;
Panyezimira ponse,
Panyumba pati mbee!
Pamyala pakongola
Yoyala ponsepo.
3. Makomo afanana
Ndi myala yoti mbuu!
Ndi kristu wopambana
Aonekeramo;
Ndi mtanda woyeretsa
Wopachikidwapo,
Amamlambira Mfumu
Namlemekezanso.
4. Kulibe gombe, Nyanja,
Kulibe nthawi 'yi,
Alendo alandira
Zoziziritsazi;
Pa mwala wa muyaya
Amanga nyumbayo,
Ndi omwe opambana
Adzakondweramo.
5. Nlokoma dziko langa!

Kopita onsewo
Mulungu awasankha,
Tifuna kunkako.
Ambuye, mutsogole
Ku dziko komweko;
Tidzakuimbirani
M'ulemerero.

# 194

1. NDIKONDWA kuganizirabe
Za Dziko la Mulungu;
Momwemo muli abwezitu
Okhala mumtendere.
*Iwo salekana, iwo salekana,*
*Ayi salekana abwenzi omwewo.*
2. Komweko akhala Yesuyo
Mtetezi wa inedi
Pakati pa 'womboledwawo;
Sadzamva kuŵaŵanso.
*Iwo asekera, iwo asekera,*
*Inde asekera kumwona Yesuyo.*
3. Mulibe zoipa m'Dzikolo,
Nzokomazo zabwino;
Ndi nthenda, imfa, misoziyi
Kumwamba kulibenso.
*Dziko labwinotu, Dziko labwinotu,*
*Nawo mtenderewo, tikhumba ilotu.*
4. Ndikonda kuganizirabe
Za Dziko la Mulungu,
Za zonse zotikondweretsamo,
Nzosathanso chikondi.
*Ife tikondwera, ife tikondwera,*
*M'mene tidzampenya Ambuye wathuyo.*

# 195

1. 'TATE wa Kumwambako,
Likayere Dzinalo,
Udzetu Ufumu wanu;
Chifuniro chanucho

51

Chichitike pansipa
Monga chachitika kwanu.
2. Mutipatse leroli
E, chakudya chathuchi
Tsiku n'tsiku tichilira.
Mukhululukiredi
Tchimo lathu, monga 'fe
Iwo adatichimwira.
3. Musatifikitsemo
Muli mayeserowo,
Koma mutipulumutse.
Wanu ndi ufumuwo,
Mphamvu ndi ulemunso
Kufikira nthaŵi zonse.

# 196

1. Mtima wanga ndikonzera,
Mbuye Yesu aitana;
Ati: "Mwana, tapemphera,
Ine sindidzakukana."
2. Mbuye ndinu Mfumu yanga
Yolemera ndi yamphamvu;
Ndikapemphatu zambiri,
Simundimanira kanthu.
3. Ndikabwera nd katundu
Wa zoipa zanga zonse;
Mwazi wake wa Ambuye,
Udzandiyeretsa konse.
4. Mbuye ndinalema ine,
Mloŵe Inu m'mtima mwanga;
Mkhale m'mwemo mwini wake,
Mantha mwandichotsera 'ne.
5. Ndine mlendo pansi pano,
Mndilimbitse ndi chikondi;
Bwenzi mundilondolere
Njira pa ulendo wonse.
6. Mndidziŵitse ntchito yanga,
Mphamvu yake mundipatse;
Mundilimbikitse m'mtima
Ndikhale kwa Atate.

# 197

1. PEMPHERA m'mbanda kucha,
Pempheranso usana;
Pemphera m'dzulo momwe,
Pemphera ndi usiku.
Ndi mtima wonse idza,
Tulutsanso zachabe;
M'nyumbamo ugwadire
Ndi kukapempherabe.
2. Kumbuka 'bale ako
Ndi onse uŵakonda;
Pemphera 'dani ako
Amene akutonza.

Dzipempherere wekha
Mulungu akusunge;
Tchulanso popemphera
Dzinalo la Ambuye.
3. Akakusoŵa malo
Opempheramo m'tseri,
Komatu m'mtima mwako
Mwaloŵatu zoyera;
Anazilonga m'mwemo
Ndi Mzimu Wakuyera;
Zolingirira zija
Kwa Mlungu zidzakwera.
4. Tilibe madalitso
Akulingana n'lino
Atate atipatsa,
Kupempherabe bwino.
Ukamvatu chisoni,
Kwa Mbuye kapemphera.
Adzakusangalatsa,
Pemphero adzamvera.

# 198

1. POKUPEMPHERANI
Mundiphunzitse 'ne
Ndi Mzimu wanu Woyera,
Ndikayanjane nanu, Atate,
Ndi kukulemekezani 'Nu
2. Mdikumbutse zomwe
Munandichitira
Ndikakuyamikireni,
Ndikweze Dzina lomwe angelo
Aliimbira Kumwambako.
3. Mndimvetse chisoni
Pakuululira
52
Zochimwa zanga zambiri;
Mumtima ndi kupatsa mtendere
Mutachotsera zoipazo
4. Chikondi, chimwemwe,
Chifatso, chiletso,
Zipatso zonse za Mzimu
Mundibalitse, ndikafanane
Ndi Mbuyathu popempherapo.
5. Pakupempherera
Anzanga ndi onse
Akusokera mumdima,
M'wapulumutse ndi k'ŵachitira
Zomwe mufuna k'ŵapatsawo.
6. Poloŵa ndi Inu
M'chipinda cham'tseri,
Posonkhananso pamodzi,
Muyandikire nafe, Atate,
Mtibvomere, mtidalitsepo,

# 199

1. Bwenzi lathu ndiye Yesu
Atikonda ifetu;
Zifunsiro zathu zonse
Tipemphere mbuyathu.
Mtima phee tisowa tonse,
Zitibvuta chabeko,
Kaamba sitimanka konse
Kupemphera Mlunguyo.
2. Tili nazo zotiyesa,
Zitidetsa nkhawamu;
Tisadandaule chabe,
Timpemphere Mbuyathu.
Kodi tikaona wina
Timkhulupiriremo?
Yesu adziwa bwino,
Timpemphere yekhayo.

3. Kodi tikulema nazo
Zotiwawa m'mtimamo?
Atipulumutsa Yesu,
Timpemphere iyeyu.
Kodi adathawa 'balo?
Pempheratu Bwenzilo;
Akusunga m'mkono mwake,
Udzapumuliramo.

# 200

1. ZOKOMA ndithu nthaŵizi
Kwa Mlungu zondifitsadi;
Kumpando wachifumuwo
Ndiuza zanga zonsezo.
Pobvuta ine mtimamo
Nditulapo pa Yesuyo;
Pakuyesedwa ndinkatu
Kwa Mbuye, sindikhala duu.
Pakuyesedwa ndinkatu
Kwa Mbuye, sindikhala duu.

2. Zokoma inde nthaŵizi
Zotama Dzina lomweli
La Yesu, ndiwoonayo
Wopatsa dalo lonseli
Ndilakalaka Iyeyu
Wofera ine pansitu;
Pakuda nkhaŵa ine bii
Nditchula Dzina lomweli,
Pakuda nkhaŵa ine bii
Nditchula Dzina lomweli.
3. Zokoma etu nthaŵizi
Ndicheza naye Mlungudi;
Koma kwathu m'Mwambamo
Kumwona ndi koposako.
Pobvula ine thupili,
Ndiloŵa Dziko lakedi;
Ndidzati nthaŵi yomweyo;
"Tsalani bwino pansipo."
Ndidzati nthaŵi yomweyo;
"Tsalani bwino pansipo."

# 201

1. MTIDZUTSE, Mbuyetu,
Mtionekeremu:
Munene zakukmvekazi,
Timvere ifetu.
*Mtidzutse, Mbuyetu,*
*Mtipatse moyonso;*
*Mudzetu Mbuye, mudzetu,*
*Tidalitseni 'fe.*
2. Mtidzutse, Mbuyetu,
Tikweze Dzinali:
Tiuzireni Mpweyawo
M'mitima yathuyi.
3. Mtidzutse, Mbuyetu,
Timvere Mawudi;
Zoona zanu tonsefe
Tikhulupire 'zi.
4. Mtidzutse, Mbuyetu,
Mthirenso moyowo;
Ulemu ngwanu nokha 'Nu,
Dalitso nlathulo.

# 202

1. AKRISTU ndi abale, tiziyenderana tonse,
Mulungu mmodzi tili naye, ndi Ambuye yemwe,
Chitsime chomwe, njira yomwe yokhulupirira;
Tiyeni tonse, m'Mpingo 'modzi tiziyenderana.
2. Atate yemwe anatuma Mpulumutsi mmodzi
Kudzatifera kuti atiyanjanitse tonse,
Ndi Mzimu yemwe ayeretsa akumvera onse;
Tiyeni tonse, m'Mpingo 'modzi tiziyenderana.
53
3. Anatipatsa Mawu omwe olimbitsa mtima;
Kumwamba komwe tinka ndi kulonda njira yomwe.
Tibalalikiranji ife akutsata Yesu?
Tiyeni tonse, mMpingo 'modzi tiziyenderana.
4. Satana apambana tikayamba kusiyana;
Tikayanjana, yemwe adzagonja ndi kuthaŵa;
Mbuyathu adzamthyola konse ndi kumlamulira.
Tiyeni tonse, m'Mpingo 'modzi tiziyenderana.
5. Tiphatikane tonsefe okonda Yesu Kristu;
Tisalekane pakugwira ntchito za Mbuyathu;
Tilimbitsane pakuyenda m'njira yonka kwathu.
Tiyeni tonse, m'Mpingo 'modzi tiziyenderana.

# 203

1. MBUYE, Mpingo wanu usauka kwakukuludi;
Kale lija munatsitsa Mzimu wanu Wakuyera;
Lero linonso muchite, ulimbike Mpingo wanu.
2. Tidza kwa Mulungu Inu, ndinu wachifundodi;
Mutipatse Mzimu wanu tsopanoli,

tere lino;
Tikakhale ndi chimwemwe kuti tili
mbike ndithu.
3. A! maliro m'Mpingo mwanu kulirira
'balewo
Adasokerera kale ndi zoipa zapa
dziko.
Muwabwezerenso kwanu kuti akakhale
mommo.
4. Ndi chikondi mtithandize kuigwira
nkhondoyi;
Mwa kulema ndi kulimba
mutipempherere
ife,
Kuti tilimbane naye Satanayo,
osamwopa.
5. Pakubweradi Woyesa tidzamlaka
ifetu;
Angelonso adzabwera kutithandizira ife,
Kuti tilimbike ife ndi kumchotsa
m'mtima mwathu.
6. Pa la Mulungu tibwera kulandira
zidazo;
Mphamvu yanu ndi chikondi
zititsogolere
ife;
Machitidwe ndi mkhalidwe zikokere ena
kwanu.

## 204

1. AULENDO amayenda
Muusiku wo'psyawo,
Namaimba nyimbo zawo
Kunka kwawo m'Mwambamo.
2. Kuunika kuoneka
Koingitsa mdimawu;
Mbale amakondwerera,
Osaopa konse 'yi.
3. Mlugu amaunikira
Anthu ake onsewo,
Namachotsa mantha omwe,
Nayeretsa m'njira mbee!
4. Anthu osaŵerengeka
Amtamira onsewa,
Nagonjetsa zosautsa
Pomtamira Mbuyeyo.
5. Pakufika tsidya lija,
Zotibvuta zonse phe!
Mfumu yathu yopambana
Idzatikondwetsadi.
6. Nthaŵi yina adzadzuka
Ogonera m'mandamo,
Kuthaŵatu mphamvu zonse
Zotibvuta pansipa.

## 205

1. TADZUKA mzimu wanga'we
Ugwire ntchito zakozi;
54
Kukondwa ukutengedi,
Pemphero ulikwezedi.
*Pemphero, pemphero,*
*Pemphero ulikwezedi*
*Pemphero, pemphero,*
*Pemphero ulikwezedi.*
2. E, nthaŵi ya mamaŵayi
Umtamandire Mbuyeyo,
Nuyese lero ngatitu
Tsiku lakumalizalo.
3. Munkhani zako zonsetu
Unene molungamadi,
Nudziŵe kuti Mbuyako
Adziŵa zachinsinsizi.
4. Pa tsikuli, Mbuyanga 'Nu,
Munditsogolere m'njiramo;
Ulemerero wanuwo
Undilimbitse monsetu.
5. Timlemekeze Mlunguyu
Wa madalitso onsewo;
Timlemekeze tonsefe,
Atate, Mwana, Mzimunso.

## 206

1. KRISTU wakuyeratu,
Kristu wakuŵalayo,
Wolungama mdzuketu,
Muingitse mdimawo.
Dzuŵa lathu m'Mwambamo
M'wale m'kati m'mtimamo.
2. Konse kuli mdima bii
Kosakhala Inutu;
Nlosakondwa tsikuli
Mosaŵala Inu 'mu.

Ndionetu m'katimo
Mwakuŵala kwanuko.
3. Mudze, mloŵe m'mtimamu,
Mchotse monse mdima bii;
Mdzaze ndi kuyeraku,
Mchotse zosamverazi;
Ndi kuyera kwanuku
Ndikaone bwinotu.

# 207

1. AMBUYE munapatsa tsiku
Limene langopitali,
M'mamaŵa nyimbo zathu zomwezo
Mukhale nafe nthaŵiyi
*Mukhale, mukhale,*
*Mukhale nafe nthaŵiyi;*
*Mukhale, mukhale,*
*Mukhale nafe nthaŵiyi.*
2. Tipempha kuti Mpingo wanu
Ukhale ponse m'dzikoli;
Mumdima monse muŵaletu,
Kuŵala kwanu kudzedi.
3. M'maiko monse, zisi zomwezo,
Kuŵala kumafikanso;
Kupempha sikuleka konse
Kuyamikira Yesuyo.
4. Pogona ife, amadzuka
Abale akutaliwo;
Panthaŵi yonse anthu ena
Alemekeza Mbuyeyo.
5. Ufumu wanu, Mbuye Yesu,
Ukhale nthaŵi zonsedi;
Magulu onse adzagonje,
Naloŵe m'njira mwanumu.

# 208

1. MUKHALE ndine, dzuŵalo laloŵa,
Wagwa usiku, bwenzi lindisoŵa;
Ndilibe wina wakundithandiza,
Wamphamvu ndinu, mkhale ndinetu.
2. Kamoyo kanga katha lero lino,
Zidzachokanso zinthuzo za dziko;
Zimasinthika zonse zooneka,
Simusinthika, mkhale ndinutu.
3. Koma kalelo mnakhalitsa pano,
Mukhale ndine, msandichokerenso,
Sin'pempha kuti Mbuye mungotsotse,
Komatu mukhalitse ndinetu.
4. E, tsiku lonse Inu ndifunitsa;
Ndi mphamvu yanu yokha ndisungika;
Mukatsogola ndidzadikha m'mtima;
55
Usiku, msana, mkhale ndinetu.
5. Adani sindiopa mukalipo
Muletse tsoka ndi chisoni chino;
Ikadza imfa n'dzalimbika m'mtima;
M'moyo ndi m'imfa mkhale ndinetu.

# 209

1. ATATE ndiyamika, mwandisamalira leroli;
Mulungu wandikonda, mndisungenso m'mdima muno bii.
2. Mundikumbutse, ndikapanda tulo, za Kumwambako;
Zoganizira zoipitsa m'mtima muchotseremo.
3. Zochimwa za usana uno mndikhululukire
'ne;
Mtendere wanu muloŵetse m'mtima ndikagone phee.
4. Mundilimbitse ndikayese manda ngati mphasayi,
Nditagonamo ndikadzuke tsiku lomalizalo.
5. Tiyamike Mlungu wotipatsa zachifundozi,
Amyamikire onse a Kumwamba ndi apansipa.

# 210

1. DZUŴA lapitira,
Wadza mdimawo,
Mthunzi wamadzulo
Wagwa m'mwambamo.
2. *M'mwambamo nyenyezi*
*Zithwanima mbee;*
*Zonse zili m'tulo*
*Pansi pali duu.*
3. Yesu mutipatse
Tulo toti phee;
Ndi mdalitso wanu
Mndigonetse 'ne

4. Mpatse ana ’ng’ono
Alotemo mbee;
Anthu aulendo
Msungesungebe.
5. Mutonthoze mtima
Wopwetekawo;
Akutsata tchimo
Mletse onsewo.
6. Wonsewu usiku
Andisunge ’ne
Amithenga anu
Akuyera mbee.
7. Ndidzukanso m’maŵa,
Kucha koti mbuu,
Ndiyeretu mtima
M’maso mwanumo.
8. Titamadi ’Tate,
Mwana wakeyo,
Mzimu Woyeranso,
Nthaŵinthaŵizo.

## 211

1. *DZUŴA lapita*,
Dzuŵa lapita,
Mlungu, mutigonetse phee.
2. *Mdima wafika*,
Mdima wafika
Mutisunge tonse bwino.
3. *Tibvomereze,*
Tibvomereze
Zakuchimwa zathu zonse.
4. *Mkhululukire,*
Mkhululukire
Zoipa zathu zonse.
5. *Lero tigone,*
Lero tigone,
Tigonemo mumtendere.
6. *Ndife ananu,*
Ndife ananu,
’Tate Mlungu wotikonda.
7. *Aleluya!*

Aleluya!
Aleluya, Aleluya!

## 212

1. MADZULO aja kalelo
Odwala anagona duu;
Opwetekedwa nthendazo
Munachiritsa Inutu.
2. Tsopano lino kwada bii,
Nafenso timva m’mtimamo;
Simuoneka, komatu
Tidziŵa muli nafedi.
3. Wopulumutsa mudzetu;
Adwala ena m’mtima bii,
Ena sakukondani ’Nu,
Ena sasamalira ’yi.
4. Ndi ena sanamvera ’yi
Enanso alemedwatu,
Zoopsya nazo tifadi;
Mukadza tidzaposatu.
5. Wopulumutsa, Inunso
Munasauka kalelo;
Muona zoda m’mtimamo
Tibisa ndi manyaziwo.
6. Mutichiritse ifenso,
Mutiphunzitse zanuzi;
Timve tsopano mawuwo
Ochiza nthenda yathuyi.

## 213

1. MPULUMUTSI, tikagona
Mtidalitse m’mtimamo;
Tingolapa zakuipa,
Muzichotse zonsezo.
Kukadetsa bii usiku,
Inu mutipenya ’fe;
Simulema, simugona;
Anthu anu msungabe.
2. Atipsinjadi masoka,
Mibvi iponyekatu;
Atisungadi angelo,
Moyo mutipatsa ’Nu.
Ngatitu usiku uno
Ikabwera imfayo,
Mtiukitse m’maŵa kwanu,
Mpatsenso zoyerazo.

## 214

1. MULUNGU wanga, Dzuŵatu
La mtima wanga ndinudi;
Palibe mdima ngatitu
Mukaŵalira inedi.

2. Muchotse zonse zoti bii
Zobisa nkhope yanuyo;
Mudzazetu mtimangawo
Ndi kuunika kwanuko.
3. Madzulo ano mkhaletu
Pafupi ndine, Yesudi;
Ndisanagone tuloto,
Ndilingalira Inudi.
4. Kapena wina leroli
Wasokerera m'njirayi
Ya Inu Mbuye, mbwezetu,
Mumpulumutse iyedi.

## 215

1. LERO mwatipatsa moyo,
Wadza mdima, kwada bii;
Mtigonetsetu usiku,
Mchotse zakuipazi.
Yesu mutisunga ife;
Tidzakhulupirabe.
Yesu mutisunga ife;
Tidzakhulupirabe.
2. Ndife anthu aulendo,
Tili ndi adaniwo;
M'manja mwanu mtigonetse,
Mtichotsere manthawo.
Ndipo pakumuka ife,
Kwanu tidzapumabe.
Ndipo pakumuka ife,
Kwanu tidzapumabe.

## 216

1. KWACHA lero kwati mbee,
Tsiku la Mulunguli;
Dzuŵa liŵaliradi
Thambo ndi zapansipa
Upumira mpweyawu
57
Wa Mulungu konseku.
2. M'nyumba yanu, Mlungu, 'yi
Tisonkhana teretu,
Ndi mitundu yonseyi
Tikulambireni 'Nu:
Yesu Mbuye wathuyo
Ndiye Mfumu ponsepo.
3. Inu Mlungu kalelo
Mutalenga zonsezi
Munapuma tsikulo;
Tipumadi ifenso.
Mommo tilandiratu
Zopumitsa mtimawu.
4. Yesu munadzukanso
M'manda lero lomwetu;
Ntchito munayambayo
Yakudzutsa anthu 'fe,
Kuti ndi mitimayi
Tigwirebe ntchitozi.

## 217

1. AMBUYE, tasonkhana
Tsiku lino lopatula,
Tidzapembedza Inu
Tsiku lino lopatula.
Bwenzilo lakufatsa,
Mbweretu kutipatsa
Mtima wakumvesetsa
Tsiku lino lopatula.
2. Sitinanyalanyaza
Tsiku lino lopatula.
Tigwadirira m'mantha
Tsiku lino lopatula.
Mbwezetu maganizo,
Mtimvetse malangizo;
Tchimo mufafanize
Tsiku lino lopatula.
3. Timvere Mawu anu
Tsiku lino lopatula
Muŵadalitse ndithu
Tsiku lino lopatula.
Mtiperekeze kwathu,
Msunge mitima yathu;
Mpatse chisomo chanu
Tsiku lino lopatula.

## 218

1. DZUŴA la Mulungu
Ladzatu labwino;
Ndi chimwemwe ife
Tiliona lero.
Lithaŵitsa nkhaŵa,
Lichotsanso mantha
Ndimo m'mtima mwathu
Likhalitsa bata.
2. Tikondwera kuti

Tipumula lero;
Tazileka ntchito
Kuti tipemphere.
Koma ntchito zathu
Za palero lino
Nzakumvera Yesu,
Kumlandira bwino.

## 219

1. NDI lokoma m'Mwambamo,
Mbuye, Bwalo lanulo;
Ndi mwabwino muli 'Nu
Dziko losachimwali;
Mtima wana wonsewu
Umakhumba m'Mwambamo
Nkhope ya Mbuyathuyu,
Mlungu wa chisomoyo.
2. Zimbalame zonsezi
Zimayamikira 'Nu;
Anthu amakondwanso
Okhumbira m'Mwambamo;
Njiŵa yosapumayo
Inafika m'chombocho;
Okhulupirira 'Nu
Amapuma kwanuno.
3. Anthu opembedzawo
Amakondwa m'mtimamo;
Munapatsa madzitu,
Munagwetsa manawo;
Mumakoma mtimatu
Tidzayamikiratu,
Pachimpando chanucho
Mkhale Mfumu yathudi.

## 220

58

1. YESU mkhale nafe
Nthaŵi yomweyi,
Kuti mphamvu zanu
Tilandirezi.
2. Mzimu Wakuyera
Mutipatsetu,
Mtima wathu wonse
Usakhale duu.
3. Moyo watsopano
Ulimbitse 'fe,
Mlungu wathu yemwe
Timdikirabe.

## 221

1. ANTCHITO a Mulungu 'nu
Olinda m'nyumba mwakemo.
Myamike, muimbiretu
Mlungu Mbuye wathuyo.
2. Mugwade pansi m'nyumbayo
Mpembedze nonse Mlungutu;
Mugadamire m'mwambamo.
Mtamande Mbuye wanutu.
3. Yehova adalitse 'nu,
Ndiye wachifundocho,
Asunge moyo wanuwu;
Amtame anthu onsewo.

## 222

1. KWEZANI mitu yanuyo,
Zipata zamuyaya,
Ikaloŵemo Mfumu ya
Ulemereroyo!
Amfumu awa ndaniko?
Ambuye ndiyeyo,
Mulungu wogonjetsa onse,
Wolimba mphamvu njo!
Mulungu wogonjetsa onse,
Wolimba mphamvu njo!
2. Tatsegukani inutu,
Zitseko zosathera,
Amfumu akumwambako
Aloŵe mwanumo.
Amfumu awa ndaniko
Wolemereroyo?
Mulungu wa makamu ndiye,
Wolemereroyo.
Mulungu wa makamu ndiye,
Wolemereroyo.
*Aleluya, aleluya, aleluya, aleluya, aleluya.*
*Amen, amen, amen.*

## 223

1. MLUNGU ali muno,
Tonse timgwadire,
Mantha omwe timchitire;
Ali mukachitsi,
Tonse tili chete,

Ndi ulemu timpembedze;
Ndiye yekha Mlungu wathu
Atipulumutsa,
Tidzamlemekeza.
2. Mwini madalitso,
Mndikonzere m'mtima,
Mbuye, ndingokhulupira.
M'Mwambamo angelo
Agwadira inu,
Ife tigonjanso kuno;
Mpingo wonse uchiitse
Chifuniro chanu.
Ponse pansi pano.
3. Yesu Mbuye wanga,
M'khale m'mtima mwanga,
Ndiwotu kachisi wanu.
Ikafika imfa,
Mundisunge kwanu
Kuli inu ndi angelo.
Moyo wanga ulimbike
Kufikira ine
Ndidzakupenyani.

# 224

1. MTSINJE woyerawo
Wotuluka m'nyumbayo
Ya Mlungu wathuyo
Uyeretse tonsefe.
*Ife tifikeko*
*Tibatizidweko,*
*Tiyeretsedwedi*
*Ndi Ambuye leroli.*
59
2. Mwa anthu onsewo
Umayenda mtsinjewu,
Nuŵachiritsadi
Okhulupirirawo.
3. Tikondwereratu
Pakumvera Yesuyo,
Abwere onsewo
Ndi kuloŵa m'mtsinjewu.

# 225

1. ATATE, muwapenya
Anzathu ali pano,
Abvomereza Inu
Ambuye Mfumu yawo;
Alonjezetsa lero
Kutsata Mbuye onse
M'ŵathangatire iwo
Asabwerere konse.
2. Tsopano alandira
Chizindikiro chanu
Munachiika ndinu
Cha Ubatizo wanu
Mulembe dzina lanu
M'mitima mwa onsewa;
M'ŵabatizenso Mbuye,
Ndi Mzimu Wakuyera.
3. Muŵalimbitse onse
Akhazikike m'mtima,
Akhale chikhalire
Oyera ndi olimba;
Mutithandize tonse
A Mpingo wa Mulungu
Tikhale oyenera
Ndi okondana ndithu.

# 226

1. MONGA zomera zonsezo
Zikula ponsepo,
Mulungu mumeretsazo,
Momwemo anawo.
2. Munali mwana, Yesu 'Nu
Wamng'ono kalelo,
Ndi munakula m'msinkhu ndi
Kutama 'Tatewo.
3. Ndi ife tinga, mbewuzo
Zomera m'mundawo;
Mumtima mutidyetsedi,
Tikule bwinomo;
4. Ndi kutsukidwa m'mwazimo
Mumtima mwathu mbee,
Tionetsedwe konseko
A Mlungu ana 'ke.

# 227

1. USIKU uja kalelo
Anampereka Yesuyo,
Usiku womwe m'manja mbuu
'Natenga mkate Iyeyo.
2. Natamandira Mlunguyo
Wolamulira pansipa,
Natema mkate, natitu

Kwa omwe anatsatawo;
3. “Ndi thupi lopatsidwali
La Ine, mtenge, mudye, ndi
Muchite ichi nonsenu,
Ndi chikumbutso changatu.”
4. Ndiponso m’manja chikhocho
’Nakweza, natamandamo
Mulungu, mtima wake mya,
Nanena mawu omwewa:
5. “Chikho cha mwazi wangachi
Chitsuka mtima woda bii,
Cha mapangano omwewo
Chisomo cha Kumwambako.
6. “Chikho cha mwazi wangachi
Chitsuka mtima woda bii,
Cha mapangano omwewo
Chisomo cha Kumwambako.

## 228

1. SINDILI woyenera ’ne,
Ambuye, kudzamo;
Munene mawu, ndimvebe
Okondweretsawo.
2. Sindili woyenera ’ne,
Mumtima mwanga zi;
Munene, ndikachiradi,
Ndilibe moyo ’yi.
60
3. Sindili woyenera ’ne;
Pamtanda panupo
Munamaliza mlandu phe
Ndi mwazi wanuwo.
4. Ndilaŵako tsopanoli
Zakudya zanuzo;
Mudzaze mtima wanga ndi
Kukonda kwanuko.

## 229

1. MONGATU mawu anuwo,
Ndi Mtima chete phee,
Mbuyanga kufa kwanuko
Ndikumbukire ’ne.
2. Chakudya chakumwambachi
Ndi thupi lanudi;
Chikho cha chipanganochi
Ncha mwazi wanuwo.
3. Getsemane ndionako
Ndi nkhope yanu dwii,
Thukuta la pamphumilo
La myazi yanuyi.
4. Ndi mtanda uli m’maso mbuu,
Ndiona m’menemo,
A Yesu kufa kwanuko,
Kuthetsa imfazo.
5. Pamene padzakhalapo
Milomo yanga phee,
Mukadza ndi Ufumunso,
Mukumbukire ’ne.

## 230

1. MUDZE, anthuni, talaŵani ’nu
Mkate ndi chikhocho cha Mbuyathu.
2. Khristu ndi mwini moyo wathuwu,
Pamtanda anafera ifetu.
3. Anatifera nsembe Iyeyo,
Ndiye Wansembe wake Iyenso.
4. Imfa ndi mdima zinathaŵa zii!
Ndipo chisomo chikuŵala mbuu.
5. Tadzanitu, okhulupiradi,
Talandirani zachinsinsizi.
6. Ndiye wa moyo wonse Mwiniyo,
Moyo wosatha atipatsa ’fe.
7. Ndiye wodyetsa anthu omwewo,
Napatsa mwazi, moyo wakewo.
8. Yesu Mbuyathu, Inu nomwe ’Nu,
Tsopano mkhalebe ndi ifetu.

## 231

1. MOMMUNO, Mbuye tionanetu,
Mommuno ndizikhudza zanu phee,
Mommuno zachinsinsi zanu mbuu,
Mwa Inu mtima ndipumirabe.
2. Mommuno, Mbuye, mkate wanuwu,
Mommuno vinyo wakumwambako,
Mommuno zolemera zanga du,
Chisomo chanu ndidzalaŵanso.
3. Ndilibe wondithangata ‘ne ’yi,
Ndilibe wina wondisunga ’ne;
Zikwaniratu mphamvu zanuzi,
Ine, Ambuye, mphamvu nzanudi.
4. Tsopano nthaŵi yake phwandoli,
Loyala ili m’gome mwanumu;
Ndidye ndimwere zakukomazi,
Ndiyanjanabe nanu, Mbuyathu.

5. Chakudya ichi chidzapita du,
Chizindikitsa za Kumwambazo;
Zosapitazo tidzalaŵatu,
Za Yesu mwini wakukondako.
6. Tikadya phwando zaka zonsezi,
Ndipo zakudya zimalozatu
Kuphwando lija la Kumwambako,
Komwe tidzadya kwa Mulungutu.

## 232

1. NDIMAMVA njala, Yesu,
Ya mtima wakusoŵa;
Mdidyetse ngati mana
Anagwa m'chipululu.
2. Ndimamva ludzu, Yesu,
61
Muloŵe mwanga lero;
Mndimwetse ngati madzi
Anatuluka m'mwala.
3. Ndi mkate wanu, Yesu,
Ndi thupi lobvulala,
Mndilimbikitse, Mbuye
Mundikhutitse mtima.
4. Mwa chikho chokumbutsa
Chikondi chopambana,
Mndipatse moyo wanu,
Ndikayanjane nanu.
5. Mndidyetse m'chipululu
M'ulendo wanga wonse;
Mdimwetse, ndipirire
Osalefuka konse.

## 233

1. A!YESU, ndapangana
Kutumikira 'Nu
Ndi moyo wanga wonse,
Mbuyanga ndinutu;
Mukhaletu pafupi
Masiku onsewo,
Sindidzaopa konse,
Mutsogolereko.
2. Ndikufuna kumva Inu,
E, Mawu anuwo,
Ndisamve za satana
Zonyenga zakezo;
Adani anga onse
Andizingiratu;
Mukhaletu pafupi,
Mundithangate 'Nu.
3. A! Yesu mwapangana
Ndi anthu anuwo
Adzakhala ndinu
Ku Dziko lanulo;
Inenso ndapangana
Ndisabwerere 'yi;
Mndipatse mphamvu yanu
Ambuye ndinudi.
4. Mundionetse, Yesu,
Mapazi anuwo,
Ndidzapondera awa
Munjira monsemo;
Ndithangateni ine
Ndisalefuke 'yi;
Mundilandire m'Mwamba
Ndikamwaliradi.

## 234

1. MUNDIMVERE, Mbuye wanga
Nkana ine ndimalakwa,
Koma ndinu moyo wanga;
Mbuye, mkhale ndine.
2. Ndine mlendo pansi pano,
Msanditaye m'dzanja lanu,
Mundisunge mwana wanu;
Mbuye, mkhale ndine.
3. Munafera ine kale
Kuti mukandimasule,
Lero lino mndinyamule;
Mbuye, mkhale ndine.
4. Mundidzaze ndi chikondi,
Mndiyeretse m'mtima monse,
Chifuniro changa mthyole;
Mbuye, mkhale ndine.
5. Imfa ikandifikira,
Inu ndidzakangamira
Ndikaloŵa ine m'mdima,
Mbuye, mkhale ndine.

## 235

1. ANU Mbuye ndifetu!
Mutimvere kwanuko;
Anu tikhalirebe
Kuno ndi Kumwambako.
2. Anu Mbuye ndifetu!

Mwanu tipumiredi;
Ndinu Mbale wathu ’fe,
Mutusunge nthaŵizi.
3. Anu Mbuye ndifetu!
‘Dikireni tonsefe;
Moyo ndinu, n’choona,
M’njiramo tiyendebe.
4. Anu Mbuye ndifetu!
Ndife nkhosa zanuzi;
62
Mwanu tibisalemu,
Mwanu mosungikadi.
5. Anu Mbuye ndifetu!
Tsogolani nthaŵizo;
Mtiyendetse m’moyomu
Kunkabe Kumwambako.

## 236

1. AMBUYE, Mwini zonsezi,
Ulemu tiperekadi;
Chikondi tionetsanji?
Mwapatsatu.
2. Dzuŵa ndi mvula yonseyo
Ndi mame mwatipatsanso,
Masika ’dzera kwanuko;
Mwapatsatu.
3. Mwapatsa Mwana wanu, ndi
Mwapulumutsa dzikoli;
E, zaulere zonsezi
Mwapatsatu.
4. Tibwezeretu bwanjiko
Ziperewera zathuzi;
Ndi moyo tili nawowo
Mwapatsatu.
5. Ambuye zathu zonsezi
Kwa Inu tibwezeredi;
Tingopereka zanuzi,
Mwapatsatu.

## 237

1. PETURO ’nafunsa Hananiya:
“Zopereka zili kuti?”
Hananiya ananena:
“Zopereka ndinapereka.”
*Munthu aganize*
*Zimene anachita Hananiya*
*Munthu aganize*
*Njira yakuunika.*
2. Mbiri ya Hananiyayo
Inali yodabwizatu;
Ananyengatu Peturo;
“Zopereka ndinapereka.”
3. Ife tonse tichenjere
Tingadzachite zomwezo:
Tisaname ndi kunena:
“Zopereka ndinapereka.”
4. Mulungu akondadi leroli
Wopereka mokondwera;
Tikapereka motero
Tidzalandira dalitso.

## 238

1. MBUYE wathu, mutipatsa
Zonse tili nazozo,
Mutikomeratu mtima
Osaleka konseko,
Mutikonda, mutisunga,
Mutisamalira ’fe.
2. Dzuŵa, madzi, kudya, mpweya,
Moyo, zonse nzanuzi,
Si za ife, nzaulere,
Tingozilandiradi;
Zifumira kwa Aate
Wotikondakondatu.
3. Monga tilandira, Mbuye,
Mtiphunzitse tonsefe
Tipere chuma chathu
Ndi kusangalalatu;
Zakukhala m’manja mwathu
Tiziyese nzanudi.
4. Tikhaletu nawo, Mbuye,
Mtima wosauma ’yi
Ndi wofatsa ndi wabwino
Ndi woyerayeradi,
Kuti tiyenere Dzina
La Mbuyathu Yesuyo.
5. Tisaiwalire ’bale
Athu osadziŵa ’Nu,
Akulira ndi odwala
Tiŵapemphereratu;
Titsanzenso Mbuye Yesu
Ndi k’ŵathangatira ’wo.
6. Dalitseni, Mbuye, zonse

Zomwe taperekazi,
Mzilandire, nsembe yathu,
Mziyeretse Inudi
63
Ndi mitima yathu yonse
Tikuyamikirani.

## 239

1. POLENGA dzikoli
Pakumva Inudi,
Kwayeratu;
Mumve pempheroli,
Ndipo pamenepo
Palibe mawuwo,
Muŵaletu.
2. Inu wakudzatu
Kuŵachiritsadi
Anthendawo,
Kupatsa moyowo,
Kuona m'masomo,
Pa anthu onsewo
Muŵaletu.
3. Mzimu woonadi
Ndi wachikondicho,
Idzanitu;
Muunikirepo
Pali zamdimazo,
Pa dziko ponsepo
Muŵaletu.
4. Inu atatuwo,
Wodala Mlunguyo,
Timveretu;
Pa dziko ponsepo
Muchotse mdimawo,
Mutume Mawuwo,
Muŵaletu.

## 240

1. ADZAPAMBANA Yesu ponse
Pakuyenda dzuŵalo;
Adzamverabe namgwadira
Pa dziko lonse pansipa.
2. Sadzalekeza kuyamika
Ndi kuimbaimbabe;
Adzapemphera nsiku zonse
Natchula Dzina lakelo.
3. Pomveka konsekonse mbiri
Yake ya Wokondayo,
Ang'ono akwezanso mawu
Poimba nyimbo zawozo.
4. Ufumu wake udalitsa
Osauka onsewo;
Otopa amapuma chete,
Magoli amathyoka thyo!
5. Zolengedwa zonse zidze
Kugwadira Mfumu yathu,
Amlemekeze akumwamba,
Tiimbe pansipa; Amen.

## 241

1. ANTHU akum'maŵa
Nanka msangako,
Nzeru 'nali nazo,
Nafatsansowo;
Nanka kuli Mwana
Anabadwayo;
Anatsogozedwa
Ndi nyenyeziyo.
2. Anapeza Mwana
Ali m'kholamo,
Nagwadira Iwo
Mbuye wawoyo;
Anthu onse omwe
Ali pansipa,
Azitsata Mbuye
Ndi nyenyeziyo.
3. Mu ulemerero,
Yesu m'Mwambamo
Muli eni ake;
Anthu onsewo
Osadziŵa konse,
Akutalinso,
Akokedwe iwo
Ndi nyenyeziyo.
4. Akukhala kunja,
Osokeranso,
M'ŵaŵalire Mbuye,
Asagone'wo;
Amumdima omwe,
Olemedwanso,
Mtsogoleri wawo
Ndi nyenyeziyo.
5. Paulendo wathu

Tili pansipa,
Muŵalire tonse
Tili m'njiramo;
Mutitsogolere
Anthu tonsefe,
Mutifitse tonse
Ndi nyenyeziyo.

# 242

1. Timva mawu omwewo
Atitu: Yesuyo
Mpulumutsi ndiyedi,
Yesuyo, Yesuyo.
Pita m'midzi monsemo,
Dziko lonse limvetu,
Pita iwe konseko,
Mveratu mbuyeyo.
2. IMbadi za iyeyo,
Amvetu anthuwo
Kuti Yesu 'nafadi
Kalelo, kalelo.
Atikonda ifetu,
Natifera indedi
Kuchotsera chimoli,
Yesuyo, Yesuyo.
3. Bukitsani mawunso
Konseko, konseko!
Kaitane anthuwo
Ponsepo, ponsepo.
Kodi wina samvatu?
Pitako, pitako 'we;
Angofuna onsewo
Yesuyo, yesuyo.

# 243

1. ZIPATA zachitsulo zitseguke zonse mbee!
Ambuye wa Kumwambako alowê momwemo.
2. Mbendera yake ikupiza m'mlengalengamo,
Kufana ndi nyenyezi younika m'mdimamo.
3. Ankondo a Mulungu 'nu,
Yendani m'njiramo,
Mitima yanu yonseyo iyeretsedwe mbuu!
4. Tsatani Mbuye Yesuyo ndi mtanda wakewo;
Mlaliketu Uthenga kwa anthu onsewo.
5. Musamaopa kanthu 'yi tamani Yesuyo;
Kaimbireni nyimboyi ndi mphamvu zonse.
6. Zipata zatsegudwa mbee! za m'dziko monsemo;
Ambuye wapambanatu ndi mtanda wakewo.

# 244

1. PAMAIKO pali mdima,
Penya mtima chetetu,
Leroli malonjezano
Angokwaniridwatu.
Kondwerani, kondwerani,
Yesu mulitsetu.
2. Adze amitundu yonse,
Adze akutaliwo;
Ayang'ane mtanda uja
Woti nji paphiripo
Mbiri yanu, mbiri yanu
Ibukitse ponsepo.
3. Ponse padakhala mdima
Pakaŵale dzuŵali;
Kumalire konsekonse
Muthaŵitse mdima bii!
Mpulumutsi, Mpulumutsi,
Muyeretse zonsezi.
4. Ibukitse mbiri yanu,
Ifikire konseko,
Iŵagwire anthu mtima,
Iŵathyole m'katimo
Mphamvu yanu, mphamvu yanu,
Idziŵike konseko.

# 245

1. MBWERE Mlungu Mbuye wathu,
Msunge zakuonazo,
Mudalitse anthu onse
Ndi chifumu chanucho.

2. MMbwere Yesu Mwini moyo,
Ukuletu 'lemuwo;
Gonjetsani anthu onse,
Mpatsenso mtenderewo.
3. Mbwere Mzimu Wakuyera,
Mutitsitsimutseko;
Muthaŵitse mdima wonse,
Muŵalitse m'mtimamo.
4. Anthu onse taukani,
Imbirani Mlunguyo;
Zichuluke zomtamanda
Pansi ndi Kumwambako.

## 246

1. ANYAMATA a Mulungu,
Muzigwira nkhondoyo,
Mumenyane ndi Satana
Mzimu wakunyengayo.
2. Komwe asauka anthu
Akukhala m'mdimamo
65
Osadziŵa Mpulumutsi,
Phunzitsani konseko.
3. Pomangidwa anthu nayo
M'yambo yoipitsayo,
Pomwe amaopa chabe,
Masulani golilo.
4. Walitsani nyali yanu
Ikachotse mdima bii!
Mpaka ikainga zonse
Zosautsa m'dzikoli
5. Akutopa ndi ofoka
M'ŵatonthoze mtima phee!
Osokera, onyozeka
Muŵafunefunebe.
6. Achisoni obvutidwa,
M'ŵathandize msangatu;
Zosautsa zawo zonse
Yesu azichotsadi.
7. Anyamata limbikani,
Gwiranitu nkhondoyi;
Yes salephera mwini,
Sitiiŵalira 'yi.
8. Isaleke ntchito yake
Mpaka anthu onsewo
Alambira Mfumu yathu,
Nagonjera konseko.

## 247

1. Anthu ali m'mdima akuitanitsa
Unikani! Unikani!
Alikumwazika mungawalanditse,
Unikani! Unikani!

*Tumizani kuunikako*
*Kuoneketu kwa onsewo;*
*Tumizani kuunikako,*
*Nthawi zonsedi kuwaletu.*

2. Tamva aku makedonyako atero,
Unikani! Unikani!
Tititu, Mbuye tizinka komweko,
Unikani! Unikani!
3. Tisaleme pakuchita zabwinozi,
Unikani! Unikani!
Tidziunjikire ngale
zakumwamba,
Unikani! Unikani!

## 248

1. MUNENE Mbuye, 'nenetu,
Nditsanze mawu anuwo;
Munandifuna Inetu,
Ine ndifune zanuzo.
2. Nditsogolere m'njirayi
Nkhosazo zisokerazo;
Ndidyetse Mbuye, zanuzi
Zimene zifa njalayo.
3. Ndilimbikitse, Mbuye, nji!
Pamwalapo ndiimebe;
Onse alibe mphamvu 'yi
Omwe ndithangate 'ne.
4. Ndiphunzitseni, Mbuyetu,
Ndidziŵitse nzeru zanuzo;
Munole mibvi yangayi,
Ipyole yonse m'mtimamo.
5. Ndipumulire panupo,
Ndinene motonthoza phe!
Ndi mawu opumitsawo
Olema ndikanenebe.
6. Ambuye, ndi chikondi tho!
Mudzaze mtima wangawu;
Ndinene zachikondicho,

Ndiyamikire monsemu.
7. Ndichitireni, Mbuye 'ne,
Monse mufuna mwanumo;
Kumwamba tionane mbee,
Maso ndi maso kwanuko.

## 249

1. MULUNGU wa Kumwamba bwera kunoku
Ndi mtima wokondwera kulowâ m'nyumbayi;
Chifukwa cha zabwino mwatichitirazi
Tikukuyamikirani leroli.
*Inde, tikuyamikani, Atate, leroli,*
*Mwatimangira 'fe kuno kachisi wanuyu!*
*Ndi ulemerero wanu mudzaze* m'nyumbayi;
*Muyeretse, mudalitse munomu.*
2. Tikondwa tonse ndi kukuthokozani 'Nu
Poyamba kupemphera ndi kuimbiramu;
Mommuno nsiku zonse mukhale nafetu,
Monga ndi angelo anu m'Mwambamo.
3. Ikhale ngati nyali yoŵala nyumbayi,
Yakutsogoza onse ophunthwa m'mdima bii;
Akunja ndi Akristu m'ŵapulumutse ndi
66
Kuunika kotuluka munomu.

## 250

1. KRISTU ndiye Mwala wathu,
Kristu timangirapo;
Wosankhidwa ndi Mulungu,
Atimange tonsefe;
Iye ndi Mthandizi wathu,
Timkhulupirira 'Ye
2. Mudalitse nyumba yathu;
Mbuye, nthaŵi zonsetu
Muthandize anthu onse
Odza kuphunzira 'mu,
Ndi antchito anu omwe
Odza k'ŵaphunzitsa 'mu.
3. Tiyamike Mlungu 'Tate,
Tiyamike Mwanayo,
Tiyamike Mzimu wake;
Onse omwe Mmodzitu,
Waulemerero wonse
Ndi wamphamvu ponsepo.

## 251

1. ANAKWATIRA kale
Pa Eden pajapo;
Ulipo lero lino
Mdalitso womwewo.
2. *Aŵiri aimamu,*
*Mwamuna ndi mkaziyu;*
*O! Mzimu Wakuyera,*
*Mdalitso mpatsetu.*
3. Mulunzanitse awa,
Atate, leroli;
Munakwatits' Adamu
Ndi Hava kalelo.
4. Mukhale nawo, Yesu,
Mongatu kalelo
Ukwati mnadalitsa
Pa Kana pajapo.
5. M'ŵasunge, m'ŵayendetse
Munjira yanuyo,
Akhale ndi kudala
Pabanja pawopo.

## 252

1. YEHOVA Mlungu wathu,
Amene mumapatsa
Zipatso za chikondi
Polenga anthu anu,
Mupatse awa 'ŵiri
Mitima yokondwetsa,
Yofana m'munda muja
Munayendamo kale.
3. Mbuyathu wokondedwa,
Pokhala m'dziko muno
Munadza ku ukwati,
Naŵadalitsa onse;
Ukwatiwu mukonze,
Mukhale nafe pano;

Iwowa m'ŵadalitse
M'chifundo chanu chonse.
4. Ndi Mzimutu Woyera
Mufike nayo mphamvu,
Mukatsangane nawo
Akupangana omwe;
Mupatse 'wo chisomo
Chokometsetsa mtima;
Chikuletu chikondi
Chitsazo nchanu chomwe.
5. Mulungu mwa Atatu,
Atate, Mwana, Mzimu,
Tikhaletu wokondwa
Ndi Inu m'chiyanjano;
Titama Inu Mlungu,
Wokonda ife ndinu;
M'ulendo wathu wonse
Tiyende m'chikondano.

## 253

1. MULUNGU wa Yakobo Inu, mdyetsa anthu anu,
Kalelo munatsogolera makolo athuwo.
2. Tsopano tipereka mapemphero athu ano.
Mulungu wawo mukhalenso Mlungu wa anawo.
3. Tikasokera m'njira mutilondolere ndithu,



Chakudya ndi chobvala mutipatse tsiku n'tsiku.
4. Mtifungatire ndi mapiko paulendo pathu,
E, tikafike okondwera kwa Atate wathu.
5. Tipempha madalitso ano mpatse ife tonse;
Tisankha Inu ndinu Mlungu wathu nthaŵi zonse.

## 254

1. MLUNGU wathu mwatifitsa
Kufikira leroli;
Moyo wathu munasunga
M'njira yonse yathuyi;
Mtsogoleri wathu ndinu
Paulendo pomwepo
Tingakutameni bwanji
Kaamba zonse zanuzo?
2. E! Chisomo chosaleka
Tachiona kalelo;
Masungidwe ndi chikondi
Zikalimo momwemo;
Pausana, pausiku,
Muli nafe ponsepo;
Madalitso anu omwe
Tiri ndi ambiriwo.
3. Tinayenda muli mdima
Wotidetsa nkhaŵawo,
Pena tinangosauka
Ndi zobvuta zathuzo;
Koma Inu munalimo
Mumitambo yomweyo,
Nafe tinathandizana
Ndi mdalitso wanuwo.
4. Ena atsagana nafe
Natsiriza njirayo,
Nafikira kuli Inu,
Natilindirirako;
Tithadi ulendo wathu
Ndi kupita komweko,
Mutitsogolere 'Tate
Kukuŵala kosatha.

## 255

1. MBUYE, tikuthokozani,
Ndinu mwatitsogolera;
Zaka zonse mwatisunga;
Tiyamika mokondwera,
Zotibveka, zotidyetsa,
Mphamvu, moyo, zonsezi;
'Tate tikuthokozani
Chaka chatsopanochi.
2. Ndinu mwatithangatira
Pakuona zosautsa;
Polefuka ndi podwala
Ndinu mwatitsitsimutsa.
Munatiteteza bwino
Tili ana kalelo,
Ndipo zomwe mwazichita
Chaka chotitheracho.

3. Chaka chino mutipatse
Mphamvu zosachimwa konse,
Zoipitsa ndi zodetsa
Mtima mtichotsere zonse.
Mtithandize tizimvera
Kuyambira leroli,
Ndi kugwira ntchito zanu.
Chaka chatsopanochi.
4. Inde,’Tate, mtiyendetse
M’njira yolungama yanu,
M’mtima mwathu mtiyeretse
Kuti tikondane nanu.
Zaka zonse muli nafe,
Sitiopa konse ’yi
’Tate tikuthokozani
Chaka chatsopanochi.

## 256

1. TILIMALIMA m’minda,
Tibzala mbewu zathu,
Komatu zibvumbidwa
Ndi Mlunguyo wamphamvu.
Dzuŵalo aŵalitsa
Namatumiza mphepo,
Mbewuzo nameretsa
Mulunguyo wabwino.
*Mphatso zonse zathu*
*Zifuma kwa Mulungu,*
*Tilemekeze Mbuye wathu,*

*Atikondadi.*
2. Wolenga ndi Yemweyo
Wa zinthu zonse zathu;
Maudzu ameretsa,
Nayatsanso nyenyezi.
Mphepo zonse zimva,
Nyamazo aziŵeta;
Sadzaiŵala konse
Anake kuŵadyetsa.
3. Tiyamikira ’Tate,
Zabwino zonse zino,
Kubzala ndi kukunkha
Ndi moyo tili nawo.
Kuninkha Inu Mbuye
Tilibe mtulo wina,
Komatu tipereka
Mitima yoyamika.

## 257

1. YAMIKANI nonse ’nu,
Pomwimbira nyimbozi Za
masika athuwa;
Potumiza mvulayi,
Mlungu wathu yemwedi
Atipatsa zonsezi;
Timwimbire m’nyumbayi
Za masika athuwa.
2. Dziko lathu lonseli
Nla Mulungu yemweyu;
Atumiza mphatsozi
Zakutilimbitsadi,
Mmera wathu wonsewu,
Mbewu zathu zonsezi;
Timtamande Mbuyeyu
Wotipatsa zonsezi.
3. Nthaŵi yina Mbuyeyu
Adzafika pansipa,
Nadzakonza zonsetu;
Zosakondweretsazi
Naziponya m’motowo,
Koma m’nkhokwe mwakemo
Mudzadzala mbewu tho!
Zokomera bwinotu.
4. ’Dzani Mbuye msangatu,
Msonkhanitse zonse phe;
Anthu anu onsewa
Muŵapulumutse ’wo;
Zopweteka zawozo
Ziŵathere zonse phe;
’Dzani mu Ufumu ndi
K’ŵasonkhetsa onsewo.

## 258

1. OYAMIKA Mlungu mbwere,
Za masika mudzaimbe;
Dzinthu zathu takolola,
Sizionongeka m’minda.
Mlungu Mlengi asamala,
Zotisoŵa akonzera;
Mloŵe m’nyumba ya Chauta,
Mkweze nyimbo zamasika.
2. Dziko lonse nla Mulungu
Kuti limbalire dzinthu;

M'munda zonse zimamera
Zakukoma ndi zoipa;
Mmera udza, bwino ngala,
Maso omwe amakhwima;
Mutilole, Mwini dzinthu,
Tikakhale dzinthu zanu.
3. Adzabwera Mbuye wathu
Kukolola dzinthu zawo;
M'munda mwawo akachotse
Minga ndi zoipa zonse.
Adzatumanso angelo
Minga akaponye m'moto,
Koma tirigu amsunge
M'nkhokwe yake nthaŵi zonse.

## 259

1. CHIFUKWA cha zokoma mtima zonse za ulerezo,
Timlambire Mbuye;
Tikweze nyimbo yathu yakukondwa kuli 'Ye,
Tigwadiretu.
2. Dzinja lokondweretsa lafikanso, litapumatu,
Timlambire Mbuye;
Mvula igundanso, Mulungu wotikonda 'fe,
Tigwadiretu.
69
3. Dziko lonse lilikukondwa, mlengalenga mpheponso,
Timlambire Mbuye;
Zapansi pano zonse zimtamandire Mlungu wathuyo,
Timgwadiretu.
4. Maluŵa abwino aphuka m'mapiri ndi m'madambomo,
Timlambire Mbuye;
Masamba aŵisi ang'ono agwedezekanso,
Timgwadiretu.
5. Zanu zapansi nzokoma Mbuye;
Tikondwera 'fe,
Timlambire Mbuye;
Koma kwanu Kumwamba komwe Kwapambanatu,
Timgwadiretu.
6. Nafenso tidzadzuka kwa 'kufa ngati maluŵawo,
Timlambire Mbuye;
Oyera mtima adzabvala mbuu! pakudza Kristuyo,
Timgwadiretu.
7. Tidzakhala naye nthaŵi zonse ndi kuimbako,
Timlambire Mbuye;
Kumene moyo wa anthu okhulululukidwa uli wokomatu,
Timgwadiretu.
*Aleluya, Amen!*

## 260

1. MLENGI wathuWakuyera,
Mutimvere 'fe,
M'ŵasungire akutali,
Bwinodi.
2. Mbuye Yesu, myandikire
M'ŵakondwetsebe;
Mulimbitse mphamvu zawo
Zonsezo.
3. Akaona masautso
Mkhale nawodi;
Akondwere mwa chikondi
Chanucho.
4. Mpulumutsi wakukoma,
Muŵagwirize;
Nsiku zonse akulemekezeni,
*(Akuleme-keze.)*
5. Mzimu wanu Wakuyera,
Aŵayeretse;
Agonjetse ndi chisomo
M'nkhondoyi.
6. 'Tate, Mwana, Mzimu ,ndinu
Mlungu mmodzitu,
Muŵasunge m'fupi mwanu
Ponsepo.

## 261

1. YESU, munditsogoza
M'njira yanga yonseyo;
Wakunditsogozatu
Ndinu, mundisungetu;
Inde, paulendowo

Mundisunge kolimba.
2. Monga may'asusunza
Mwana wake polira,
Wakunditonthozatu
Ndinu, munditonthoze,
Ine, m'njira yanuyi
Munditsogoleretu.
3. Mbuye, ndinu wamphamvu,
Mumatola ananu.
Anthu onse pansipa
Ali otaikatu;
Muchitire chifundo,
Muŵatole onsewo.

## 262

1. MLUNGU alinane;
Amadziŵazi
Ndizinena, penanso
Za mumtimamo.
2. Mlungu alinane
Ndi usikuwo,
Nandiona momwemo
Mu usanamo.
70
3. Mlungu alinane;
Zachinsinsizo
Zosaonekerako
Azidziŵatu.

## 263

1. MLUNGU, Inutu,
Mwalenga dzuŵali,
Nyenyezi, mwezi mbee,
Ndi dzikoli.
2. Koma ineyu
Simuiŵala 'yi;
Mundisamala 'ne
Ndisagwe 'yi.
3. Mbuye, Msungi 'Nu,
Mutuma indedi
Za moyo wangawu
Zokomazi.
4. Yesu Mwanatu
Anafa imfayo
Achotsa zoti bii;
Nadzukanso;
5. Kuti m'Mwambamo
Ndikatamandetu
Wondisamalabe,
Mbuyangayu.

## 264

*1. A! MULUNGU*
A! Mulungu
Anatuma mwana wake
Uja, ndiye Yesu
2. *Anabadwa,*
Anabadwa
Ndi Maria Mbeta ija
M'Betlehem muja.
3. *Ndi angelo*,
Ndi angelo
Anaimba: "Ndiye Yesu
Mpulumutsi wanu."
4. *Alanditsa,*
Alanditsa
Ife anthu muzoipa
Zonse tazichita.
*5. Yesu Mfumu*
Yesu Mfumu,
Timagonja, mutisunge
Moyo wathu wonse.
6. *Mutisuke,*
Mutisuke
M'mwazi wanu, tikakhale
Ana anu tonse.

## 265

1. Taonani m'kholamo
Mwabadwira Mfumuyo
Yakulonjezedwadi,
Nsembe yathu ndiyeyu.

*Kondwerani nonsenu*
*Pomvetsedwa mbiriyi*
*Yakumveka m'msindomo;*
*"Wabadwira m'betelehemu."*

2. Adagona m'ndyeromo
Wachokera m'mwambayo,
Adasiya mpandowo
Yesu Kristu Mfumuyo.
3. Falitsani mbiriyi,

Inudi abusa ‘nu;
Nkhosa zanu zonsezo
Mwasiy’ranji mphirimo?
4. Pochezera m’dambomo,
Tinaona ‘ngelotu
Oimbira mawuwo
A mtendere pansipa.
5. Mwana wakuyera ‘Nu,
Munakonda ifedi;
Munasiya kwanuko
Ndi kufika pansipa.
6. Mtiphunzitse bwinotu,
Mwana wakuyera ‘Nu,
Tifanane nanudi
M’makhalidwe anuwo.
7. Tamverani, aitana;
“Ana, munditsatetu.”
Yesu, tisapite kwina,
Tizikutsatani ‘Nu.
8. Posachedwa tilekana
Osalankhulananso,
Koma tidzaona tonse
Wina mzake m’mwambamo.

# 266

1. TIIMBE ndi kulalikira
Mthenga wa chikondicho
Anamva Mlungu m’Mwambamo
Kulira kwathu pansipa.
*(Ndikhulupirira Yesu*
*Wobadwira m’kholamo;*
*Iye ndiye Mfumu yathu,*
*Timtame nthaŵi zonse.)*
2. Kwa ife lero anabadwa
Mwana wa Mariyayo,
Pamsinkhu, ine mng’ono koma
Mwini dziko lonseli.
3. Anadza nazo mphatso zake
Anatikonzeratu;
Anatitseguliradi
Pakhome pa Ufumuwo.
4. Ambuye takutamandani
Tsiku lakubadwali,
Mwa Inu tonse tikondwera,
Tiseke tonsefe.
5. A! Yesu Mbuye wakuyera,
Munagona m’kholamo;
Mudzikonzere leronso
Mogona m’mtima mwangamu.
6. Ulemerero m’Mwambamwamba
Ndi mtendere pansipa;
Tiimbe nafe nyimboyi,
Timyamikire Mbuyathu
*(Yesu ndiye Mfumu,*
71
*Yesu ndiye Mfumu!*
*Ndikhulupirira Yesu wobadwira m’kholamo.)*

# 267

1. ANA inu, ana inu,
Taukani ndi kumvera
Amithenga akumwamba;
Anafika kalelo,
Natiuza Mpulumutsi
Anabadwa pansipa.
Zaka zonse, tsiku lomwe
Umamveka mthengawu.
2. M’nyumba zonse ponseponse
Zimamveka nyimbo izi,
Kuti Yesu anabadwa,
Anagona m’kholamo,
Anafika Mpulumutsi
Wotikondweretsadi,
Kondwerani, kondwerani
Inu nonse ana ’nu.
3. Taukani, taonani
M’mwamba monse mwakuyera;
Amithenga a Mulungu
Aimbabe nyimboyo.
Yesu Kristu anatsika,
Anachoka kwawoko;
Lero lonse tiimbenso
Nyimbo yathu yomweyo.

# 268

1. KALE m’mzinda wachifumu
Munalimo m’kholamo,
Momwe mkazi anaika
Mwana wake m’ndyeromo.
Ndiye mkaziyo Mariya,
Yesu Kristu Mwanayo.
2. Uyu ’natsikira kuno,

Mlungu Mbuye wathuyo;
Anabadwa uyu m'khola
Anagona m'ndyeromo.
Mwa osoŵa ndi oipa
Yesu anakhalamo.
3. Mwa ubwana wake wonse
Anakula m'mtima phee!
Anakonda, anafatsa,
Amay' wake namvabe;
Ndipo ana nonsenu,
Mukamtsate bwinotu.
4. Ndipo Mwana uyu Yesu
Anakulakulabe;
Ndi wamng'ono ndi wofoka,
Anagona enawo.
Nsoni zathu anazimva
Ndi chimwemwe chathunso.
5. Ndi chifukwa atikonda,
Tidzampenya masowa,
Kuti Mwanayo wofatsa
Ndiye Mwini m'Mwambamo;
Atengera ana ake
Komwe adapitako.
6. Koma sitimpenya m'khola
Muli ng'ombe momwemo;
Ayi, tidzamwona m'Mwamba
Muli Mlungu 'Tatewo.
Ana akuyera mbuu
Adzamzunguliratu.

## 269

1. Usikuwo oyerawo!
Mwana adamlerayo
Akakhale Mfumuyo.
Anabadwa mkholamo,
Mfumu ya mamfumu
Ndi ya anthuwo.
2. Mwanayo wa Mulunguyo
Andikonda inetu,
Nan'tayira chumacho
Nadzagona m'udzumo.
Ndiyamika mbuye
Wanga Yesuyo.
3. Usikuwo woyerawo!
Wadzatu mtendere
Ife tonse anthuwo
Attenga Mlunguyo.
Mlemekeze "Tate,
Mwana, Mzimunso."

## 270

1. Kale anthu m'kholamo
'Napembedza mwanayo.

*Ndiye Mbuye, Mfumu yanga,*
*Ndiye Mbuye wa kumwamba,*
*Amgwadira anthuwo,*
*Timtamande Mfumuyo.*

2. Wosauka iyedi
Anagwira ntchotozi
3. Ndani kodi mbuyathuyo
Woyesedwa m'bwinjamo?
4. Analira ndaniyo
Pomwalira Bwenzilo?

*Aleluya! Aleluya!*
*Timwimbire Yesuyo.*
*Aleluya! Aleluya!*
*Timwimbire Yesuyo.*

5. Iye anachoka kwawo,
Anakhala pansipa.
Kale ana 'namwimbira
Namukondweretsadi.
6. Anafika 'kazi omwe
Ndi tiana tawoto;
Yesu anatiyangata,
Anatidalitsatu.
7. Amithenga akumwamba
Amamuyamikiratu;
Zikwi zosawerengeka
Zimtamanda Mfumuyo.
8. Ana inu yamikani
Bwenzi lanu lomweli;
M'mwamba momwe mudzampenya
Ndi kumtamandirabe.

## 271

1. KULI kaphiri m'talimo

Kunja kwa mzindawo,
Kwapachikidwa Yesuyo
Nafera ifetu.
*(Kuli kaphiri m'talimo*
*Kunja kwa mzindawo,*
*Kwapachikidwa Yesuyo*
*Nafera ifetu.)*
2. Zoopsya sitidziŵapo
Anazitengazo,
Komatu tidziŵitsa 'fe
Anatiferapo.
3. Anatifera tonsefe
Tiwomboledweko,
Tifike momwe m'Mwambamo
Ndi mwazi wakewo.
4. Kulibe wokwanira 'yi
Kulipa mlanduwo,
Wina wakutsegula 'yi
Pakhomo pakepo.
72
5. Anatikondakonda 'Ye,
Timkonde ifenso;
Tizimtsatira, tithetu
Zintchito zakezo.

## 272

1. ANA inu, myamikeni
Mpulumutsi Yesuyo,
Kaamba ka chikondi chake
Ndi chipulumutsocho
*Aleluya! Aleluya!*
*Timwimbire Yesuyo.*
*Aleluya! Aleluya!*
*Timwimbire Yesuyo.*
2. Iye anachoka kwawo,
Anakhala pansipa.
Kale ana 'namwimbira
Namukondweretsadi.
3. Anafika 'kazi omwe
Ndi tiana taoto;
Yesu anatiyangata,
Anatidalitsatu.
4. Amithenga akumwamba
Amamyamikiratu
Zikwi zosaŵerengeka
Zimtamanda Mfumuyo.
5. Ana inu, yamikani
Bwenzi lanu lomweli;
M'Mwamba momwe
Mudzampenya
Ndi kumtamandirabe.

## 273

1. ANANU, ziimbani,
Aleluya, Amen.
Ambuye tamandani,
Aleluya, Amen.
Kwezani mawu anu,
Patsani mtima wanu,
Afuna kumva inu,
Aleluya Amen.
2. Bwerani, kondwerani,
Aleluya, Amen.
Ambuye akumvani,
Aleluya, Amen.
Amatitsogolera,
Kalelo natifera,
Kukonda salekera,
Aleluya, Amen.
3. Mbuye timlemekeze,
Aleluya, Amen.
Kwawo tikabwereze,
Aleluya, Amen.
Kumwamba timtamire,
Tikamgwadire ife,
Tikhale chikhalire,
Aleluya, Amen.

## 274

1. MNANDIDZERA, Ambuye,
Kumwambako,
Munasiya akuluwo;
Koma m'mudziwotu
Munabadwamo
Munasoŵa pogonapo.
*Idzani mumtima mwanga,*
*Muli malo a Inu 'mo.*
2. Amithenga 'naimba pamlengapo,
Nalalika ulemuwo;
Koma Inu munadza mofatsatu,
Munabadwa mukholamo.
3. Zili nazotu nkhwimba zirombozo,
Ndi mbalamenso zisatu;

Koma Inu Ambuye mwapandadi
Potsamira mutu duu!
4. Munanenatu mawu a moyonso
Omasula ochimwawo;
Koma omwe ochimwa
’Nanyozatu,
Nakuphani pamtandapo.
5. Pakubweranso Inu m’Ufumuwo
Ndi zamphamvuzo zanunso,
Mundimvetse za kwanu
Kumwambako
Kuli malo a ine ’ko.
*Ukondwere mtima wanga*

*Pakumvera zokomazo.*

# 275

1. AKAZI anadza kwa Yesu
ndi anawo,
Anaŵaletsa anyamata nawakana
ndithu;
Ambuye naŵapezadi,
Anati: “Musatero ’yi
Lolani ana abwere kwa Ine,
Lolani ana abwere kwa Ine.
2. “Ndidzaŵalandira, k’ŵasunga
M’manja mwanga;
Ndi Mbusa wao Inetu, msachotse
ana anga;
Akandipatsa mtimawo,
Adzanka ndine Kwathuko;
Lolani ana abwere kwa Ine,
Lolani ana abwere kwa Ine.”
3. Wokoma Mbuyathu kwitana ana
onse;
Atsalanso ambiri ena sanamvera
zake;
Sanamva mawu akewo,
Sadziŵa kuti ’natinso:
“Lolani ana abwere kwa Ine,
Lolani ana abwere kwa Ine.”
4. Afike masiku akuti anthu onse
Adzamva mawu anu ndi kutsata
Inu nokha;
Muwale m’mtima mwawomo,
Adziŵe muŵakondanso;
Kopani anthu abwere kwa Inu.

# 276

1. ANA a Yerusalemu
Anatama Mbuye wawo;
Lero lomwe ife ana
Timwimbira nyimbo yawo.
*Mverani, aimba anawo,*
*Mverani aimba anawo*
*Zakutama, zakutama,*
*Zakutama Mbuyeyo.*
2. Tamva tikondane naye,
Tiŵerenge Mawu ake,
M’njira mwake tiyendemo,
Tiziimba nyimbo zake.
3. Aphunzitsi, ana omwe,
Ndi akulu, t’imbe tonse;
Nyimbo zathu zidzakwera
Zikamveke m’Mwamba monse.

# 277

1. OSANATU, osana,
’Naimba anawo;
M’kachisi wa Mulungu
Mwamveka nyimboyo.
’Nalemekeza Yesuyo
Wak’ŵadalitsayo;
Anamuyamikira
M’ubwana wawowo.
2. Kuphiri la ’Zitona,
Mumpingo wa ’nthuwo,
’namkupizira mnjedza
Naimba nyimboyo,
Angelo akumwambako
Napokerezanso:
“Osana m’Mwambamwamba
Kwa Mlungu wathuyo.”
3. Zitsamba zakuyera
’Naponya pansipo;
Kukondwa kunamveka
Paphiri ponsepo.
Ambuye yemwe Mfumutu
Nakwera cheteko;
Tiana toyamika
Sanatinyozato.
4. “Osana m’Mwambamwamba!”
Nyimboyi t’imbenso,

Pokhala Kristu Mfumu
Ndi Mpulumutsiyo.
Timtamandire Iyeyu
Ndi mtima wonsewo;
Tipite kwawo komwe
Tikaimbirenso.

## 278

1. NGOLIZO zilira
Za ’mithengawo,
Ndi zipata zonse
Zatsegudwa mbee!
74
Kristu, Mfumu yathu,
Mbuye wathudi,
Wapambana monse,
Alamulabe.
*Ntchito zake zatha,*
*Timwimbiretu;*
*Yesuyo wakwera,*
*Timtamandetu.*
2. ’Natipulumutsa
Natiferako,
Ali mfumu ndithu
Kwa Atatewo;
Osasautsidwa,
Osafanso ’yi
Yesu, Mfumu yathu
Adakweradi.
3. Atipempherera
M’malo ’dalawo,
Tinke kwathu komwe
Ndi chisomocho;
Akonzera malo
Ana akewo;
Yesu alipobe,
Atikondanso.

## 279

1

## 280

1. NDIKONDA mbiri yomwe
Ya amithengawo
Ya Mbuye, Mfumu yathu
Pofika pansipa;
Zochimwa zindizinga,
Koma ndidziŵatu
Anawombola ine
Pakundikondadi.
2. Ndikondwa kuti Yesu
’Nakhala mwanatu,
Chitsanzo atipatsa
Cha moyo wakewo;
Ndikati ndimtsatire
Zochita zakezo,
Sadzandinyoza konse
Pakundikondadi.
3. Pakumyamika Iye
Ndidzamwimbiratu;
Ngakhale sindimwona
Amandimveradi;
Pakuti walonjeza
Adzalandira ’ne
Ndiimbe ndi angelo,
Pakundikondadi.

## 281

1. YESU andikonda ine,
Amatero m’Buku Iye;
Akafoka mwana wake
Adzamlimbikitsa Mbuye.
*Yesu akonda,*
*Yesu akonda*
*Yeu akonda,*
*Atero m’Bukumo.*
2. Anandifera Mbuye wanga
Anditsegulire m’Mwamba,
Ndi machimo anga onse
Adzandichotsera konse.
3. Mbuye Yesu andisunga
M’njira ya Kumwamba kuja;
Andigwira m’dzanja langa
Ndingagweremo m’makwaŵa.
4. Yesu andikonda ine;
Ndikadzafa tsiku lina
Atengera ine kuno,
Ndikakhale naye Kwawo.

## 282

1. YESU Mbuye ’Nu wofatsa
Muyang’anedi kamwana,
Mndichitire chifundo;

Mundilole kwanutu.
2. Ndimalira kwa Inutu,
Mpatse mtimawo wabwino;
M'Dziko lanu loŵalalo
Mulandire mwana wanu.
3. Yesu, E, ndikufunani,
Ndinu chuma change chonse;
Mtima wanu ngwofatsadi;
Kale munali kamwana.
4. Wonga Inu ndikhaledi,
Mtima wanu mundipatse;
75
Yesu ndinu wokomatu,
Mndiphunzitse kukonda 'Nu.
5. Yesu Mbuye 'Nu wabwino,
M'manja mwanu ndikhalemo;
Mzimu wanu mundipatse,
M'mtima mwangatu mukhale.

# 283

1. YESU, ndikabwera
Mundikondweretsa,
Nsoni zanga mun'chotsera
Zonsezo.
*Ndikabwera, Mbuye;*
*Ndidzakondwera ine;*
*Muitana ana onse*
*Onga 'ne*
2. Yesu, ndikabwera,
Mumva mapemphero
Mundikonda, mnandifera
Inetu.
3. Yesu, ndikabwera
Dzanja mdzandigwira
Nokha mdzandilongolera
Njirayo.
4. N'takafika kwanu
Ndidzakhala bwino,
N'dzaonana ndi ananu,
Ndi Yesu.

# 284

1. YESU wa Kumwamba,
Mutimvere ife;
Tikugwadirani,
Mwana wa Mulungu.
2. *Ndinu wakuyera*
*Mfumu yakumveka*;
*Ife sit'yenera,*
*Koma mutimvere.*
3. Ndife akuchoka,
Mwina tisokera;
M'njira ya Kumwamba
Mutitsogolere
4. Mutiletse, Mbuye,
Lero tisachimwe;
Tikondane ndinu
Mutitsuke m'mtima.
5. Mukatiitana
Tikakhale kwanu,
Tidzayankha, "Mbuye,
Tsopano tili pano."
*(Yesu, Yesu,*
*Tikugwadirani*
*Mwana wa Mulungu!)*

# 285

1. MPULUMUTSI, Mbusa wathu,
Mutitsogolere ife;
Mutiŵete, mutisunge,
M'khola mwanu mtilandire
Yesu wathu, Yesu wathu,
Mnatigula ana anu.
2. Ndife ana, mutikonda,
M'njira mutiperekeze;
Mchotse nsoni ndi zoipa,
Osokera muŵabweze:
Yesu wathu, Yesu wathu,
Mumve mapemphero athu.
3. Munanena mulandira
Osauka ndi oipa;
Inu ndinu wachifundo
Ndi wamphamvu yolanditsa
Yesu wathu, Yesu wathu,
Tidzatu tiana tanu.
4. Tifunitsa Inu tere,
Chifuniro chanu ndicho;
Mbuye wathu, Mpulumutsi,
Mutikonzetu m'katimo;
Yesu wathu, Yesu wathu,
Mutikondebe ana anu.

# 286

1. MZINDA woyerawo

Konse nkotsekako;
Kanthu koipa,
Kanthu koipa,
Sikangaloŵemo.

76

2. Yesu ndafikatu,
Mbuyanga kwanuku;
Mundiyeretse,
Mundiyeretse,
Mnditsuke m'mtimamu.
3. Mbuye, ndikhaletu
Mbuye wokonda 'Nu,
Ndi wosungidwa,
Ndi wosungidwa,
Ndi mphamvu zanuzo.
4. Mpaka ndabvala mbuu!
Wowomboledwatu,
Woyera mtima,
Woyera mtima,
Kwanu Kumwambako

## 287

1. MBUYE, tili ana anu,
Tiyamike Inutu;
Zinthu zonse zili zanu,
Tingadike m'mtimamo.
Tiganize zake Yesu,
Za Kumwamba kuli 'Ye;
Tisachite zomsautsa,
Aziona zonsezo.
2. Amakumbukira zonse
Tizichita zomwezo.
Tidzamukomana tonse,
Sitinyazitsidwako.
Mukhululukire ife
Tchimo lathu lonselo.
Mutitsogolere ife
M'njira ya Kumwambako.

## 288

1. YESU, muli pa chimpando
Chakuŵala mbee! Kumwamba;
Mutipenye ife ana;
Mutimvere, Yesu.
2. Ife ana sitiopa,
Mukabwera mutiona,
Tamva kale mutikonda;
Mutimvere, Yesu.
3. Ife tikondana nanu,
Tiimbira nyimbo zanu,
Tiyamika mphamvu yanu;
Mutimvere, Yesu.
4. Lero mkhale nafe ndithu,
Poseŵera ndi pantchito,
Popemphera ndi poimba;
Mutimvere, Yesu.
5. Mutiletse tisaname
Ndikunena zotukwana,
Mtiphunzitse kukondana;
Mutimvere, Yesu.

## 289

1. YESU atiuza tiŵale 'fe.
Monga nyali m'mdima
tiunike mbee!
Pansi pali mdima ŵalanitu,
Inu m'malo mwanu ndi ine 'mu.
2. Yesu atiuza tiyambemo,
Ationa bwino ndi kuŵalako;
Ayang'ana pansi poŵala 'fe,
Inu m'malo mwanu ndi ine 'mu.
3. Yesu atiuza tiŵale pa
Anthu ali m'mdima osaukawa;
Tiŵalire onse, tonsefetu,
Inu m'malo mwanu ndi ine 'mu.

## 290

1. ANYAMATA inutu,
Anamwali inunso,
Muti: "Tingachitenji,
Ang'ono ndifetu,
Kuthandiza Ufumu
Wa Yesu?"
2. Aphunzitse anthuwo,
Aŵalalikiredi,
Akukhala moipa
Mumdima wakunja,
Aloŵetu m'Ufumu
Wa Yesu.
3. E! ang'ono ndifetu,
Nzeru sizimafika
Kuti tingaphunzitse;
Titani tonsefe
Kuthandiza ufumu

77
Wa Yesu?
4. Inu nonse anzanga,
Tiziganiza bwino,
Tinganene mofatsa,
Timverenso Mbuye
Kuthandiza Ufumu
Wa Yesu.
5. Pothandiza amathu,
Pak'ŵakonda anzathu,
Pakusiya zoipa,
Pokhaladi bwino,
Tithandiza Ufumu
Wa Yesu.

# 291

1. TIANA ife tingofoka,
Sitikhala 'mphamvu 'yi;
Tikhoza kukachitiranji
Yesu kumkondwetsadi?
2. Tiana ta Ambuye tili
N'ntchito yaikuludi,
Kudzichepetsa ndi kusiya
Tchimo lili lonseli.
3. Kapena m'mtima ndimakwiya,
Nditukwana mnzangayo,
Kapena ndidzitama - izi
Ndilekere Mbuyeyo.
4. Ndileke kulimbana ndi
Kuŵanamiza enawo;
Ndinene zakufatsa,
Zakukondweretsa Yesuyo.
5. Tizikondana, tisekere
Tsiku lonse kwathuko,
Muyere m'mtima popeza
Yesu ndi Woyerayo.
6. Palibe mwana wakuchepa
Kunyamula mtandawu;
Ambuye Yesu mutipatse
Mtima wokondanatu.

# 292

1. USACHIMWE konse,
Lekatu kukwiya;
Uli mwana wake,
Mwana wa Mbuyathu.
2. Yesu ndi wofatsa,
Yesu ndi woyera;
Ana ake omwe
Aziyera m'mtima
3. Mzimu wakuipa
Ukusuzumira,
Umakuyesera
Kuti ukachimwe.
4. Koma usalole
Mawu a Satana;
Bweza tchimo lake,
Chita zolungama.
5. Yesu ndi Mbuyako,
Mbuyeyo ngwabwino;
Ana ake omwe
Aziyera m'mtima.

# 293

1. TCHIMO musalole, musadziipitse,
Myese kudzikana, muzilimbikadi;
Mwamphamvu mpirire, mgonjetse zabiizi;
Mpenye kuti Yesu adzakusungani.
*Mpemphe Mbuye asunge,*
*Atonthoze m'mtimamu,*
*Alikukufunani,*
*Akasunge inutu.*
2. Mleŵe oipawo, ayi musatukwane,
Dzina la Mbuyathu muzilikwezadi;
Khalani achangu, oona, abwino;
Mpenye kuli Yesu, adzakusungani.
3. Yesu alandira akupirirawo;
Chikhulupiriro chiŵathandizadi
Mbuye athangata onse akumvera;
Mpenye kuli Yesu, adzakusungani.

# 294

78
1. NTHAŴI yaubwana yatha,
Sukulu yathu yathanso;
Nkhaŵa ndi zoŵaŵa zomwe
Zitibisaliranso.
2. Yesu wakufatsa mtima
Mlendo pansi pano 'Ye,

’Natifera, natisunga,
Atitsogolere ’fe.
3. Tamverani, aitana;
“Ana, munditsatetu,”
Yesu, tisapite kwina,
Tizikutsatani ’Nu.
4. Posachedwa tilekana
Osalankhulananso,
Koma tidzaona tonse
Wina mnzake m’Mwambamo.

## 295

1. YESU ndiye Mbusa,
Mbusa wakukoma,
Anyamula ana
Ake akuopa;
Tizitsata Yesu,
Atitsogolera,
Kwina kuli mdima,
Kwinanso koyera.
2. Yesu ndiye Mbusa
Atipenyetsetsa,
Mawu ake onse
Atikondweretsa.
Mwina alangiza
Mwana wakulakwa;
Atsogola bwino,
Ife tizimtsata.
3. Yesu ndiye Mbusa,
Anafera kale
Kuyeretsa ana
Nawo mwazi wake,
Tsono awalemba
Ndi chizindikiro;
“Ana anga onse
Andikhulupira.”
4. Yesu ndiye Mbusa
Wakutisunga ife,
Ali wachifundo
Chachikulu ndithu;
Sitiopa imfa
Akakhala nafe,
Yesu Mbuye wathu
Alandira ife.

## 296

1. POMPANO pandikonda
Poyendayenda ’ne;
Paŵala mosekera
Ndi dzuŵa loti mbee!
Ndikondwa nsiku zonse
Ndikali m’dzikoli,
Potsata Yesu m’njira yake
Yonseyi.
2. Ulendo ungoyamba
Wakunka kwathuko;
Amati: “Udzapeza
Zakusautsa ’mo”
Zobvuta ndi chisoni
Sindiziopa ’yi;
Ndidzangomtsata Yesu m’njira
Yonseyi.
3. Zoipa ndi zabwino
Zakundigwerazo,
Ndingonka nazo zonse
Ndimuze Yesuyo;
Zoŵaŵa adzachotsa
Zondiliritsazi;
Ndikangomtsata Yesu m’njira
4. Zondipingitsa zonse
Zoloŵa m’mtimamo
Achotsa, nandisunga
M’ulendo wonsewu.
Sindidzaopa kanthu,
Ngakhale imfayo,
Pomtsata Yesu yekha kunka
Kwathuko.

## 297

1. MPULUMUTSI Yesu,
Mumve nyimbo yathu;
Tikuyamikani
Mumitima mwathu
Zonse tili nazo;
Thupi, mzimu womwe,

Inde, moyo wonse,
Tipereka zonse.
*Komwe ndi Chimwemwe*
*Tidzaimba tonse,*
*Tidzatama Mbuye*
*Osalema konse.*
2. Tiyandika, Mbuye,

M’fupifupi ndinu,
Tikugwadirani,
Mutilandire bwino.
Inu munatsika
Kutifera ife;
Inu munakwera
Kuti titsatire.
3. Haya! Tipitenso
M’njira yomwe ija
Ana a Mulungu
Onse adaponda.
Tizisiya zonse,
Tiziyenda msanga,
Tisamachewuka
Mpaka tipambana.
4. Tero tidzakwera
Kwawo kwa Mulungu,
Tidzaziiŵala
Zotibvuta ife.
Komwe ndi Chimwemwe
Tidzaimba tonse,
Tidzatama Mbuye
Osalema konse.

## 298

1. Ine ndine mlendo
Wa Kumwambako;
Pansi pandikonda,
Koma mpoipa.
2. Kwathu nkopambana,
Nkosachimwako;
Zosautsa zonse
Sizikhalamo.
3. Koma azibvala
Mwana zoti mbuu!
Wosachimwa konse
M’mtima mwakemu.
4. Yesu, mndiyeretse,
Mndimveretsedi;
Mzimu, mndiyendetse
Mn’jira yanuyi.
5. Ine ndine mlendo
Wa Kumwambako;
Kundiyandikira
Kwathu komweko.

## 299

1. M’MANJA a Yesu wanga
Ndilikugonamo,
Mommo aphimba ine
Nacho chikondicho.
Mvera! Mudzera m’Mwamba
Mawu a Yesu wanga:
“Mwana, ndidzakusunga
Pano pamtima panga,”
*M’manja a Yesu wanga*
*Ndilikugonamo,*
*Mommo aphimba ine*
*Nacho chikondicho.*
2. M’manja a Yesu wanga
Nkhaŵa zonsezo zi!
Momwe zoipa zanga
Sizindibvuta ’yi
Mmomo mulibe nsoni,
Mommo mokoma monse
Sindiliramo msozi,
Ndikondwa m’mtima monse.
3. Mtima umabisala
M’manja mwa Yesumu;
Mbuye, musunge ine,
Munandifera ’ne.
Ndilinda mopirira
Mpaka wochoka mdima.
Ndikaonana naye
Yesu Ambuye wanga.

## 300

1. YESU ndiye Bwenzi lathu,
Kumwamba kuli kwao;
Amatikonda tonse,
Akulu ndi tiana;
Anzathu sapirira
80
Amalekana nafe,
Komabe kutiyanja
Saleka Yesuyo.
2. Ana ake adzapuma
Kumwamba mokondwera,
Amene anamkonda
Namtsata Yesu yekha;
Sauko ndi zobvuta
Zotitopetsa kuno,
Sitiziona konse

Kumwamba kwathuko.
3. Tidzalandirabe komwe
Zobvala za mitima
Yoyera, ndi kubvula
Zakale za kuchimwa;
Chimwemwe ndi chikondi
Tidzangokhala nazo,
Za ndewu ndi chisoni
Sitizipeza 'yi.
4. Woyenera ndani kunka
Kukhala ndi Atate,
Kuimba nyimbo zake,
Za Mpulumutsi wathu?
Tidzamka ife tonse
Tamtsata pansi pano;
Tiyeni ana onse,
Yambani leroli.

# 301

1. yesu adza kuwerenga
Ana ake abwino.
Ndikuvala zachifumu
Zakuwlazo ake.
*Ana ake angonga*
*Nyenyezi zamwamba,*
*Adzawala m'ufumu*
*Wa ambuye yesu.*
2. yesu adza kukundika
Ana ake ankhosa.
Ndiye mbusa wakufatsa
Namalizatu lero.
3. kudzachera tsiku lijalo
Msangatu msanga,
Kudzawala m'mawa wake
Pompano

# 302

1. KWA Yesu ndi kwabwinoko,
Nkoti mbee! Nkoti mbee!
Kulibe zoipitsako,
Nkoti mbee! Nkoti mbee!
Kuimba amaimbako,
Ndi amithenga omwewo
Akondwerera kokhako.
Nkoti mbee! Nkoti mbee!
2. Zochimwa sizilowâko,
Mwayitu! Mwayitu!
Misozi m'maso mwawo yi.
Mwayitu! Mwayitu!
Chisomo chili m'mtimamo,
Aona nkhope yakeyo
Ya Yesu adalitsawo.
Mwayitu! Mwayitu!
3. Oipa tili tonsefe;
Mwaziwo, mwaziwo,
Wa Yesu watigulatu;
Mwaziwo! Mwaziwo!
Tiyeretsedwa nawowo,
Mtendere wa Mbuyathuyo
Ukhala nafe komweko.
Mwaziwo! Mwaziwo!

# 303

1. DZIKO lilipolo
Lokondwatu
Oyera 'khalamo,
Abvala mbuu!
Tamvani nyimboyo:
"Mfumu tiyamikeyo,
Mkwezeni Dzinalo
Mwimbenibe."
2. Tiye kudzikolo,
Tiyeni 'nu;
Musakayikebe,
Muchedwatu.
Tikondwekondwedi,
Tchimo ndi zoipa zii!
Mbuye timwona ndi
Kukondwabe.
3. Maso a m'dzikomo
Onse nga mbuu!
Mkono wa 'Tatewo
Ngwosungatu.
Tiye ku dzikolo,
Mgwire 'nu ufumuwo.
M'mwamba mwa dzuŵamo
Tikhalebe.

# 304

1. DZUŴA liŵala, m'tulotu
'Tate chikondi chanucho
Chindidalitsapo.
2. Dzuŵa la lero lonseli
Mundisungire 'ne;
Mchotse zoipa zangazi,
Nanu ndikhalebe.
3. M'mtima mwangamu mloŵemo,
Mwini chifundocho,
Kuti ndikafananetu
81
Ndinu Mbuyangayo.

## 305

1. Yesu Mbusa, mutimvere,
Dalitsani ifetu,
Ndi usiku mutisunge,
Tidzukenso bwinotu.
2. Lero lino mwatipatsa
Zonse tili nazotu,
Moyo womwe; miyamiko
Landireni Mbuye 'Nu.
3. Tchimo lathu lonse, Yesu,
Mukhululukire 'lo;
Mtitengere kwanu komwe
Kumpumulo wanuwo.

## 306

1. TILIKUIMBA nyimbo yomweyi,
Yakuyamika Mbuye wathuyo;
Mtendere wake tiufunadi,
Titapemphera tinke kwathuko.
2. Titanka kwathu mkhale nafeko,
Tikufunani Yesu Mbuyathu;
Musunge ife nthaŵi zonsezo,
Mutiyeretse m'mtima mwathu mbuu!
3. Usiku uno mutisungedi,
Khalani m'fupi m'nyumba mwathumo;
Mamaŵanso mudzatidzutse nji!
Kuti tigwire ntchito zathuzo.
4. Mtitsogolere nthaŵi zonsezo;
Kuyenda tokha sitikhoza 'yi,
Ngati mukhala Mbuye m'fupimo,
Sitidzaopa kanthu kena 'yi.

## 307

1. AMBUYE, mtidalitsetu,
Musunge Mawu m'mtimamu;
Muyatse moto wanuyo,
Chikuletu chikondicho.
*Pokhala moyo imfanso,*
*Ambuye mtiŵalirepo.*
2. Laloŵa dzuŵa, kwada bii!
Mwapenya ntchito zathuzi;
Taletsa mwini tchimolo,
Mwinanso tangolakwapo.
3. Mufafanize m'bukumo
Zolakwa zanu zonsezo,
Ndi kutipatsa ifetu
Mtendere wanu m'katimu.
4. Chimwemwe chomwe mpatseko
Ndikukondana ndinunso
Tifuna kufananadi
Ndi Yesu Bwenzi lathuli.

## 308

1. TIKUTHA kupemphera,
Tipita kwathu tonse;
Mtiperekeze Mbuye,
Panjira zathu zonse;
Titamva Mawu anu,
Mawuwo ndi amoyo,
Aloŵe m'mtima mwathu,
Akhazikikemo.
2. Ambuye, Mzimu wanu
Atikumbutse tonse,
Atithandize lero
Kumvera Mawu onse.
Kumudzi mkhale nafe,
Musatisiye konse;
Machimo onse mletse,
Tiyere m'mtimamo.

## 309

3. TIMYAMIKIRE Mlunguyo,
Anthu ndi zinthu zonsezi,
Ndi onse a Kumwambako
Mlungu amyamikiredi.

## 310

1. MULUNGU akhale nawo
ulemerero ndi dalitso,

Ndiye Atate, Mwana,
Mzimu Woyera, Mlungu mmodzi;
2. Tsopano, poyamba paja,
Masiku onse alinkudza
82
Mphamvu, ulemerero,
dalitso, chipambano.

# 311

1. YEHOVA, Mbusa wangadi,
Ndilibe kusoŵa;
Andigonetsa bwinoli
Mumsipu wokoma.
2. Ku madzi ake odikha
Anditsogolera;
Ndi moyo wanga wofoka
Aulimbikitsa.
3. Anditsogolera m'njira
Zakulungamazo;
Chifukwa changa ay', koma
Cha dzina lakelo.
4. Ndipyola kodi chikhwaŵa
Cha mthunzi wa imfa?
Ndilibe mantha ngati 'Nu
Mundiperekeza.
5. Chakudya changa chabwino
Mwandikonzera pha!
Pamaso pa adaniwo
Mudyetsa mtimanga.
6. Mwadzoza mutu wanga ndi
Mafuta okoma;
Mwadzadza chikho changadi,
Inde, chisefuka.
7. Zokoma ndi zakuyanja
Zidzanditsatako;
Ndikhala m'nyumba ya Mlungu
Ku nthaŵi zonsezo.

# 312

1. MULUNGU, anthu 'fe
Mutidalitsetu;
Chisomo chiŵalire 'fe
Cha nkhope yanuyo.
2. Potero onsewo
Okhala pansipa
Adzamva bwino msangatu
Za njira yanuyi.
3. Ayamikire 'Nu
Padziko ponsepa,
Mitundu yonse ipfuule
Mokondweratu.
4. Pakuti mfumuyo
Ndi Inu nokha 'Nu;
Mudzalangiza bwinotu
Mafuko onsewo.
5. Zipatso zakezi
Labala dzikolo;
Adzadalitsa ifetu
Mulungu wathuyu.
6. Adzadalitsa 'fe
Mulungu mwiniyo;
Padziko ponse anthuwo
Adzamuopatu.

# 313

1. NONSE okhala pansipa,
Muyamikire Mlunguyo;
Ndi nyimbo mtumikire 'Ye;
Mubwere mokondweratu.
2. Yehova ndiye Mlungudi,
Anatilenga yekhayo;
Amatidyetsa ake 'fe,
Ndi nkhosa zake ifetu.
3. Loŵani m'Nyumba mwakemu
Ndi nyimbo zokondweretsatu;
Mumyamikire Mlunguyo.
Mulemekeze Dzinali.
4. Pakuti Mbuye Mlunguyo
Wokoma mtima ndiyedi,
Woona adzakhalabe
Kunthaŵi nthaŵi zonsetu.

# 314

1. MULI ndi ludzu, idzani
Kumadzi amoyo
Imwani monse kolere
Kuchitsime konko.
2. Munka kangati kulaŵa
Madzi onyengera?
Musataye mphamvu yanu,
83
Musataye chuma.
3. Imvani, Yesu akuti;
"Chuma ndili nacho,

Landirani, yemwe amva
Akhale ndi moyo.”
4. Funani Mlungu tsopano.
Akulindirani;
Iye ndiye wachifundo,
Akulandirani.
5. Ali wokhululukira;
Imvani ananu:
Mtima wake usiyana
Ndi mitima yathu.
6. Monga m’Mwamba mupambana
Zonse pansi pano;
Choncho maganizo ake
Apitira athu.
7. Anthu onse a padziko
Adzamvera Mlungu:
Adzakhala ndi chimwemwe,
Nadzamtama ndithu.

# 315

1. *TIYAMIKE Mlunguyo*,
Tiyamike Mlunguyo,
Watidzera ndi mtendere
(Ndi mtendere).
2. *Anatuma, Mtetezi*,
Anatuma Mtetezi,
Ndiye Mfumu Yesu Kristu
(Yesu Kristu).
3. *Tifunafunatu,*
Tifunafunatu,
Osapeza Mpulumutsi
(Mpulumutsi).
4. *Tifunafuna m’phirimo,*
Tinafuna m’phirimo,
Koma osampeza mommo
(Osampeza).
5. *Tinafuna m’nyanjamo*,
Tinafuna m’nyanjamo,
Koma osampeza mommo
(Osampeza).
6. *Yesu ndiye Mtetezi,*
Yesu ndiye Mtetezi,
Wina saoneka ayi
(Saoneka).
7. *Dzina lake Yesuyo,*
Dzina lake Yesuyo,
Lidzakhala nthaŵi zonse
(Nthaŵi zonse).
8. *Tonse timyamiketu,*
Tonse timyamiketu,
Mpulumutsi wamuyaya
(Wamuyaya).

# 316

1. AITANA, aitana dziko lonse,
Imvani mukhaliranji chete?
Aitana,
Aitana aitana dziko lonse.
2. Mfumu iyi, Mfumu iyi ya Kumwamba
Ndi Yesu, ndi Mpulumutsiyo wa anthu onse.
Anthu onse, anthu onse, tinke kwawo.
3. Aitana,aitana inu mayi,
Ndi Yesu, amene anakhetsa mwazi wake;
Mwazi wake unagwera inu mayi.
4. Aitana, aitana inu ’tate,
Ndi Yesu amene anakhetsa mwazi wake;
Mwazi wake unagwera inu ’tate.
5. Yesu ati, Yesu ati; “Muzisiye
Zoipa zimene muzichita, muzisiye,
Muzisiye, muzisiye inu nonse.”
6. Titi bwanji? Titi bwanji ife anthu?
Ndi Yesu anatifera ife akuchimwa;

Akuchimwa, akuchimwa tinke kwawo.

# 317

1. *’TATE, ’Nu.*
’Tate ’Nu, mtione ’fe
Tadza kupemphera kwa Inu.
2. *Imvani,*
Imvani Amfumu ’Nu
Mawu athu tinena lero.
3. *Tipempha,*
Tipempha mdalitsetu
Mpingo wanu woyera uno.

4. *Imvani,*
Imvani akunjawo
Akulira opanda Yesu .
5. *Ayenda,*
Ayenda munjirazo
Zakupita kuchitayiko.
6. *Ambiri,*
Ambiri akufadi
Osadziŵa za Kristu Yesu.
7. *Auke,*
Auke akristuwo,
Akakhale antchito anu.
8. *M'ŵatume,*
M'ŵatume antchitowo
Alalike Uthenga wanu.
9. *Ubwere,*
Ubwere Ufumuwo,
Uoneke padziko ponse.

## 318

1. PEREKANI mtima wanu,
Yesu aitana nonsenu;
Osauka, amasiye,
Yesu anakuferani 'nu.
*Perekani, perekani*
*Mtima wanu nonsenu;*
*Yesu akulindirani,*
*Perekani mtimawo.*
2. Tsegulani mtima wanu
Nonse, Yesu akaloŵemo;
Akuchimwa, Iye adzaloŵa nazo zakukomatu.
3. Mtembenuke mtima wanu,
Inu osamvera Mlunguyo;
Yesu aitana ife
Tikamtsate m'njira yakeyo
4. Perekani mtima wanu
Kwa Mbuyathu Mpulumutsiyo,
Ndiye wakudziŵa kuchiritsa
Anthu akuchimwatu.

## 319

1. YESU, Bwenzi la ochimwa,
Yesu wondikondable,
Ena samandikwanira,
Yesu salephera 'yi.
*Aleluya Mpulumutsi!*
*Aleluya Bwenzilo!*
*Amakonda, amasunga;*
*Ndimufuna Yesuyo.*
2. Yesu ndiye mphamvu yanga,
Andilimbikitsatu;
Poyesedwa ndi adani
Andipambanitsadi.
3. Yesu atonthoza mtima
Ndikadera nkhaŵa 'ne
Pakukhala ndi chisoni
Andisangalatsabe.
4. Yesu ndiye Mtsogoleri
Pakuyenda m'njiramo,
Ndipo ndikafuna kugwa
Andigwira dzanjalo.
5. Yesu ndimafuna Inu,
Mwapambana zonsezo;
Mlamulire mtima wanga,
Mndikhalitse wanutu.

## 320

1. ŴALIRA Yesu m'dziko linoli,
Ŵalira Yesu m'ntchito zakozi,

Ŵalira Yesu pofanana ndi
Ambuyathu Yesu Kristu.
*Tiŵaliretu, tiŵaliretu*
*Ambuye Yesu wotikonda 'fe;*
*Mlemekeze 'Ye tsiku lonseli,*
*Ine tiŵalire Yesu.*
2. Ŵalira Yesu pazobvutazo,
Ŵalira Yesu pakukondwanso,
Ŵalira Yesu, imbirani 'nu
Ambuyathu Yesu Kristu.
3. Ŵalira Yesu wolimbitsayo,
Ŵalira Yesu m'moyo monsemo
Ŵalira Yesu; tidzaonatu
Ambuyathu Yesu Kristu.

## 321

1. ZAMBIRI zogona m'kholamo,
Zosungika bwino 'mo;
Koma imodzi inasokeradi,
Nitayika m'thengomo
Kutali kuphiri loopsalo,
Kutali ndi mbusa wakeyo.
2. Ambuye, muli nazo zambirizi,

Kodi sizifikirazi?
Koma Mbusa nanena, “Yangayo
Yatayika naneyo;
Ngakhale njira njoopsadi,
Ndilinga kuphiri kuipezanso.”
3. Koma zina sizinadziŵa ayi,
Makwaŵa ’napyola ’ye,
Ndi mdima woopsa WA usikuwo
Ambuye nailonda yake.
Anamva kulira kutaliko,
Naipeza yofoka, yakufayo.
4. Ambuye, wakuti ndi mwaziwo
Panjira ponsepo?
“Ndaukhetsa potsata iwetu,
Kukubweza ku kholalo.”
Ndi m’manja mwalaswa
Bwanjimo?
“Ndalaswa ndi minga pofuna
Iwe.”
5. Ndi ponse paphiri ndi padambopo
Ndi makwaŵa, indetu,
Kunakwera kupfuula
Kumwambako,
“Kondwani, ndaipeza yanga!”
Nd’ angelo a Mlungu
nabwezanso,
“Kondwani, Ambuye ’napeza
yawo.”

# 322

1. MUTHIRE, Yesu, m’mtimanga
Kukonda kwanuko:
Mwa Mlungu ndidzalimbika,
Ndisasokerenso,
Ndisasokerenso.
2. E, moto wanu woyera
Uyake mwa ine;
Utenthe zonse zoti bii,
Undiyeretsedi,
Undiyeretsedi.
3. Munagwa pa Atumwiwo;
Dzazani mwa ine;
Mzimu wamoto Woyera,
Ndipempha mudzetu,
Ndipempha mudzetu.
4. Ndikhazikike inetu,
Maumtima muli mwai;
Ndi Yesu ndikondanetu,
Si kanthu kena ’yi,
Si kanthu kena ’yi.

# 323

1. ATATE Wamkulu ndi
Wamphamvu zonse,
Atate Wamkulu ndi wamphamvu
Zonse,
Khalani ndi chifundo ndi ife lero.
2. Ifetu kuchimwa timachimwa,
Mbuye,
Ifetu kuchimwa timachimwa,
Mbuye,
Mutume Mzimu wanu
Atiphunzitse.
3. Mwa Mzimu mulowe mumitima
Yathu,

Mwa Mzimu mulowe mumitima
Yathu,
Zoipa zathu zonse mtiululire.
4. Tafika Kwa inu mutiunikire,
Tafika kwa inu mutiunikire,
Chifundo chanu chonse taleka
lero.
5. Tifuna kuchita chifuniro chanu,
Tifuna kuchita chifuniro chanu,
Chifundo cha Mulungu
nchabwino chokha.
6. Atate, mupatse zomwe
tapemphazi,
Atate, mumpatse zomwe
tapemphazi,
Tapempha m’Dzina lake la
Mpulumutsi.

# 324

1. ONA Mwanawankhosayo
Wakuseza zakuipa zathu zonse.
*Mwanawankhosa*
*Watisenzera*
*Zakuipa zathu zonse.*
2. Anazenza m’thupi mwake;
Pakukhomedwa pa mtanda anali
duu.

3. Ona pamtanda Yesuyo
Anabvutika chifukwa cha anthu
’fe.
4. Imva kulira kwa Yesu
Pamene anasiyidwa muimfayo.
5. M’mwazi wake tisambamo;
Zichotsedwa zakuipa zathu zonse.
*(Ona Mwanawankhosayo*
*Wakusenza zakuipa*
*Zathu zonse.)*

## 325

1. YESU analikhanda
M’Betlehemumo;
M’ngelo anasimba za
Kubadwa kwake.
*Kubadwa kwa Yesu*
*M’Betlehemumo;*
*Khandalo linagona*
*M’khola la ng’ombe.*
2. Mngelo anatumidwa
Kuŵasimbira
Abusa a nkhosa za
Kubadwa kwake.
3. Anapita nasiya
Nkhosa zawozo;
Anapita kumudzi
Kukamlambira.
4. “Tadodoma, abusa,
Kwachitikanji?
Mwazisiyira yani
Nkhosa zanuzo?”
5. “Posunga nkhosa ife
Kubusa kwathu
Mngelo anasimba za
Kubadwa kwake.”

## 326

1. ATATE, tifika pamaso panu;
Mukomane ndi ife, Mbuye wathu.
2. Mitima yathu iyi nayo njanu,
Muiyeretse, muikonze Mbuye.
3. Ndi maso athu awa nawo nganu,
Muŵapenyetse zinthu zanu zokha.
4. Ndi manja athu awa nawo nganu,
Agwiretu ntchito yanu yokhayo.
5. Ndi miyendo yathu iyinso njanu,
Ithamange m’ntchito yanu
Yokhayo.
6. Ndi milomo yathu iyinso njanu,
Ilalike Mawu anu kwa onse.
7. Ndi makutu athu awanso nganu,
Muŵamvetse Mawu anu okhawo.
87
8. Tidziperekadi konse Kwa Inu
Tikakhale anthu anu okhawo.

## 327

1. ATATE, ndipempha
Tsopano mundimvere,
Ndipempha kuti mundithandize.
2. Ine ndili munthu
Wochimwa pansi pano,
Munditsuke Mbuye, ndiyeretu.
3. Ndalema ndathodwa
Ndi zinthu zapadziko,
Zakhalatu goli londimanga.
4. Yesu Mfumu Inu
Mumandiuza kuti:
“Pemphera, ndipo udzalandira.”
5. Ndipempha, Ambuye,
Mundidzaze n’chikondi,
Mtima wangawu ukukondeni.

## 328

1. DZIKO lonse mlambire
Yesu Mbuye wathuyo,
Muimbire ndi chimwemwe
Dzinalo.
2. Mbwere nonse muone
Zomwe achita Yesu:
Nzozizwitsa, nzodabwitsa
Ntchitozo.
3. Aweruza ndi mphamvu
Ku nthaŵi yamuyaya;
Dizo Lake Lisamala
Am’dziko.
4. Mbwere mudzamve nonse
Zamphamvu za Yehova;
Mumwibire, mumyamike
Yehova.
5. Tisonkhane tonsefe,
Tigwadire Ambuye;
Timlambire, timlambire

Yehova.

## 329

1. Mlungu akuyanganiradi

Kufikira tionana.
Azasunga nkhosa zake;
Mlungu akuyang'aniredi

E! Tidzakomananansotu
*Pamapazi a yesu,*
E! Tidzakomananansotu

2. Mulungu akuyan'ganiredi.
Mulungu akuyan'ganirenidi
M'dzanja mwake akulere,
Ndi mapiko akubise;
Mulungu akuyan'ganirenidi.

## 330

1. POTULUKA m'mudzimo
Yesu anasenza mtanda,
Pokwera ku Gologota
Kukampachikatu Mbuye.
Pilatoyo, mfumu yawo,
Inampereka kwa 'Yuda,
Kuti ampachiketu
Kufera zoipa zathu.
*(Atate 'nu amayi 'nu, nonsenu,*
*Onani Yesu wasenza mtanda;*
*Atate 'nu, amayi 'nu, nonsenu,*
*Onani Yesu wasenza mtanda.)*
2. Zoopsya zopambana
Zinachtika pamtanda
Kuti mdima unadza,
Dzuŵa linabisikanso.
Chinsalucho cha m'kachisi
Chinang'ambika pakati,
Myala inaswekanso,
Dziko linagwedezeka.
3. Pomwalira Mbuyeyo
Anapfuula kokweza
Naitana atate
Kupereka mzimu wake:
"Mlungu wanga, Mlungu wanga.
Mwandisiy'ranjitu Ine,
Mundikweze m'Mwambamo,
Landirani mzimu wanga."
4. Ankhondowo Poona
Zinachitika pamtanda,
Anabaya m'nthitimo,
Munatuluka magazi.
Paphirilo la Golgota
Anaferapo Mbuyeyo
Nasauka koopsya
Ndi zoipa zathu izi.

## 331

1. TUMPHATUMPHA moyo wanga,
Sangalala ndi Mtetezi;
Kuwombola Kwa Yehova
Kwatuluka m'dziko lako.
*Mulungu wakwezekatu,*

*Mpulumutsi m'dziko lako,*
*Wakwezekatu Chitetezo.*
*Wabvundikira iwedi*
*Mzimu wanga'we wafunda,*
*Lulutiratu moyo wanga.*
2. Bvinabvina moyo wanga,
Lulutira mtima wanga;
Wa mawuwo a Yehova
Watuluka m'dziko lako.
3. Imbirira moyo wanga,
Mtendere wako wafika;
Mbendera ya Chitetezo
Waikwezetsa ndi Yesu.
4. Ukondwere moyo wanga,
Kuunika kuoneka,
Ndi mdimawo uthaŵatu;
Lulutira moyo wanga.
5. Usekere moyo wanga,
Ndi Yehova akufuna;
Wakwezatu mbenderayo
Ya Chitetezo, sekera.

## 332

1. PAKUONA imfayo
Chisonicho chikula

Ndilira misozi.
*Ndilira, ndilira,*
*Ndilira Mbuye Yesu wangadi.*
*Ndaimba ndi kulira ndi kusisima,*
*Ndaimba ndi kulira ndi kusisima,*
*Ha! Ha! Aleluya!*
*Ha! Ha! Aleluya!*
*Mwasiyiranji Ambuye Yesu?*
2. Ndinasiya amayi,
Ndinasiya atate,
Abale komweko.
3. Kazembe wanga m'matenda,
Ndili m'manja mwa Mbuye.
Abale tsalani.
4. Zoipa zakanikadi,
Sizikhoza kuchotseka,
Ndilira misozi.
5. Angelo aitana,
Aitana Kumwambako,
Tiyeni, tikwere!
6. Munafera pa mtanda
Chifukwa cha inedi, Si
cha wina ayi.

## 333

1. LIDZE msanga dzuŵa lanu
Lolonjezedwa, Ambuye.
Mnalinena polaŵira
Kwa anyamata, Ambuye.
*Kuli chimwemwe m'dzuŵalo*
*Lakufika Ambuye.*
*Ha! Ambuye bwerani.*
*Ha! Ha! Ambuye bwerani.*
2. M'dziko lino chimwemwecho
Chakudza ndi Yesu Mbuye.
Mfumu yathu ya Kumwamba
Ndi dziko lonse lapansi.
3. Adzakhala pampando
Wakuweruza makamu;
Amitundu adzaima
Pamaso pa Mbuye Yesu.
4. Adzanena kwa anthuwo
Akudzanjatu lamanja,
"Loŵani 'nu m'chikondwero
Cha Atate nthaŵi zonse."

## 334

AMEN, Amen, Amen.

## 335

1. NDIDZE pafupi pa
Mlungu wanga,
Ngakhale pamtanda
Mundikweza;
Koma ndiimbabe
Mbuye mndikhalitse,
Mbuye mndikhalitse,
M'fupi Ndinu.
2. Ngakhale kuthengo
89
Ndasokera,
M'mdima ndigonapa
E, pamwala;
Koma m'kulotako
Ndiyandikizanso,
Ndiyandikizanso
M'fupi Ndinu.
3. Pajapo ndipenya
Pokwerapo,
Angelo atsika
Kumwambako,
Ndiwo akodola
Kuti ndikabwere,
Kuti ndikabwere
M'fupi Ndinu.
4. Tsopano poukanso
Wokondwatu,
Ndipeza pomwepo
Pali Mlungu;
Ndipo masautso
Andisendezanso,
Andisendezanso,
M'fupi Ndinu.
5. Pena pakufadi,
N'kwera m'Mwamba,
Dzuŵa ndi nyenyezi
Zitsalira;
Pomwe ndiimbanso,
Ndidza pafupi pa,
Ndidza pafupi pa
Mlungu wanga.

## 336

1. Munasiyatu

Dziko lanulo,
E! Chifukwa cha tse;
Ndi ku betlemuko
Pakubandwa inu.
Nyumba zao nakukanani.

*Mbuye yesu lowani m'mtima,*
*Nyumba yanu ndimtimanga*
*. Mbuye yesu lowani m'mtima,*
*Nyumba yanu ndimtimanga.*

2. Akumwambawo
naimbitsatu,
kukulemekezani
koma monga mwana,
mziko munabadwa,
munadzichepesadi.
3. nyama za mthengo
Ndi mbalamezo,
Zili nazo zogonamo.
Koma mwana wa mulungu
Analibe nyumba,
M'mapululu nagonatu.
4. munadzera ndi
mau amoyo,
Akupulumutsa anthu;
anakanidza,
anatsautsa,
anapichika inu.
5. M'mene mubwera
Kutiweruza
Ndi angolo oimbira,
Mundiitane,
Muti "idza'wo,
Khala nane kumwamba.

## 337

1. KASUPE ali wodzaza
Ndi mwazi WA Yesu;
Omwe asamba mwa uyu
Ataya zoipa.
*Ataya zoipa,*
*Ataya zoipa;*
*Omwe asamba mwa uyu*
*Ataya zoipa.*
2. Woba wakufa 'napenya
Kasupe, nakondwa,
Ndimo inenso mwa uyu
Ndisamba ndiyera.
*Ndisamba ndiyera,*
*Ndisamba ndiyera;*
*Ndimo inenso mwa uyu*
*Ndisamba ndiyera.*
3. Mwazi wa Yesu wokondwa
Ukhala wamphamvu
Kwa ana onse a Mlungu,
Uchita kwombola.
*Uchita kwombola*
*Uchita kwombola;*
*Kwa ana onse a Mlungu*
*Uchita kwombola.*
4. M'mene ndapenya mwazi wa
Mabala anuwo,
Kukonda kwathu nditama
Kwa kutha kwa moyo.
*Kwa kutha kwa moyo,*
*Kwa kutha kwa moyo;*
*Kukonda kwanu nditama*
*Kwa kutha kwa moyo.*
5. Kumwamba ndikaimbanso
Zimphamvu za Mlungu,
Zopulumutsa onsewa
Omvana ndi Yesu.
*Omvana ndi Yesu,*
*Omvana ndi Yesu;*
*Zopulumutsa onsewa*
*Omvana ndi Yesu.*

## 338

1. Yesu and'itana
Adzandiyeretsa,
Ndi mwazi wake wkhetsa,
Paphiri gologota.

*Ndlikudzatu,*
*Ndidza Kwa inu;*

*Munditsuke m'mtimamo*
*Ndi mwazi wanuwo*

2. Ndafoka, ndaipa,
Mundilimbikitsetu;
Mundiyeletse konseko,
Ndiyereyere mbuu.
3. Atero ndaniyo?
Ndi yesu wabwino;
Apatsa mvanu mtendere
Ndimphamvu m'mtimamo.
4. Yesu akhzika,
Zonse za m'katimo;
Nalonga mzimu woyera
Munafoipamo.
5. Nditam mwaziwo!
Nditama chifundo!
Nditam yesu ambuye,
Nditenga mphamvu "ko.

## 339

1. Ndi misozi ndi chisoni
Ndiliratu Kwa inu yesu.
Ndichifundo chandi gwira
Ndirila kuti ndine wanu.

*E! kwa inu, E! kwa inu,*
*Ndirila kuti ndine wanu.*

2. Mbuye yesu ndi atate,
Mundiona ndili wosowa
Ndimasowa mzimu wanu
Kuyinga zonse za mumtima.
3. Mtendererewo wosanyenga
Ndirila ine m'mtima mwanga.
Kondimvets chimwemwetu
Ndirila ine m'mtima mwanga.
4. Kalekale ndinathawa,
Ndinakana kumvera inu;
Koma lero ndamva kuti
Muli mwini wake wa moyo.

## 340

1. MALO alimo m'nyumba ya Yesu,
Ndi nyimbo zake zakuitana:
*"Loŵa, loŵa,*
*Tsopano loŵatu."*
2. Mdima ufika, dzuŵa laloŵa,
Nthunzi zilipo, wadza usiku.
3. Nyumba yodyera ilikudzaza;
Idza nuloŵe, Mkwati anena:
4. Chakudya ichi ndi cha iwenso,
90
Madzi amoyo umwe kolere.
5. Onse am'Mwamba Ali momwemo,
Ndipo Angelo akuitana:
6. Mawu a Yesu ati: "Msangatu
Idza, wochedwa, loŵa
m'nyumbamo."
7. Msanga adzachitseka chitseko,
Adzakuuza: "Choka, chokatu."
*Choka, choka,*
*Anena chokatu.*

## 341

1. PAMTANDAPO, pamtanda,
Yesu 'nafera;
Pamutupo chilemba,
Chisoni ine.
Analira, "Eloi, Mlungu wanga!
Lama Sabakatani,
Mwandisiyiranji?"
2. Kumandako, kumanda
Yesu nauka;
Anaposa imfayo,
Watha zonsezi.
Ndikondwera, Mbuyanga
'Naukadi;
Sekerani nonsenu,
Yesu ngwamoyo.
3. Pakukwera Kumwamba
Yesu anati,

"Musachoke m'mudzimu,
Pempheranitu;
Mzimu Wakuyeradi adzabwera,
Kuthangata nonsenu,
Kuti msafoke."
4. Uzanitu abale,
Onse alongo,
Ndi amitundu yonse
Adzakondwera.
Musaope ntchitoyo yokomadi,
Mphotho yake Kumwamba,
Moyo wosatha.

## 342

1. M'DZIKO lino tikhalamo
Utibvuta moyo,
Koma dziko la mtendere
Lili kwa Mulungu.
2. Watitsogolera Mbuye,
Komwe Kwa Atate,
Ndimo tidzatsata naye
Moyo wathu wonse.
3. Ndi tsopano tilindira
M`dziko lathu lino;
Ntchito atipatsa Mlungu,
Tizigwira bwino.
4. Ngati zakuipa zathu
Zikatisautsa,
Tithaŵire kwa Mbuyathu,
Atipulumutsa.
5. Timpemphere kutipatsa
Mtima watsopano,
Kutithandizira kunka
Paulendo uno.

## 343

1. kuli dziko la bwino mwamba
Lakuwala kopotsa dzuwa;
Yesu atikonzera malo
Pokarila Ife komweko.

*Bwinoli tipita*
*Tikomana mwadzikolija,*
*Bwinoli tipita*
*Tikomana mwadzikolija.*

2. Tidzaimba komwekonyimbo
Za abwino omvero yesu.
Sitizamva chisoni Ife.
Tidzakondwe masiko onse.
3. Tidzatama atate wathu
Kuti iye napatsa yesu
Kuchotsera zochimwa zonse
Ndikutidalitsira Ife

## 344

APITA anzathu dzuŵa lino
Kosaoneka,
Apita anzathu dzuŵa lino,
Apita anzathu dzuŵa lino
Kosaoneka.
*A! Kumwamba*
*A! kuli a Yesu.*

## 345

1. INE ndili ndi manyazi
Kuti kale lomwelo
Ndinanyoza kudza komwe
Kwa Mtetezi wanga Yesu,
Ndati, Sindimfuna `yi.
2. Koma Iye wandipeza;
Ndamuona m`mtandamo,
Mwa kufera ine momwe;
Ndipo ndati m`mtima mwanga:
Mbuye, ndikufunani.
3. Nsiku zonse kwanja kwake
Kunandithandizatu,

Kunandichiritsa mtima;
Ndipo ndati: Mpulumutsi,
Ndinu Mbuye wangatu.
4. Sindifuna Mbuye wina,
Koma Yesu yekhayo;
Ine ndili munthu wake,
Iye anandigonjetsa
Ndi kukonda kwakeko.

## 346

1. KONDWANI nonsenu,

Mpulumutsi anadza;
Onani kukhola,
Ndi mtanda ndi manda
*Mlemekeze, bukitsani,*
*Naferatu kale;*
*Kondwerani, mlemekeze*
*Akhaladi moyo.*
*2.* Kondwani nonsenu,
Anakhetsatu mwazi,
Natiwombola nawo,
Tikhale ana ’ke.
*3.* Kondwani nonsenu,
Atikhulululukira,
Wosachimwa nafera
Anthu ’fe oipa.
4. Kondwani nonsenu,
Mfumu yathu yakwera;
Kwa Atate Kumwamba
Atipempherera.
5. Kondwani nonsenu,
Adzabweranso Yesu,
Waulemu, wamphamvu,
Kuweruza dziko.

## 347

1. TATE ndili mwana wanu,
Nkana ndinachimwa,
Ndingolirira kwa Inu;
Khululukireni.
*Machimo anga ngambiri*
*Osaŵerengeka,*
*Ndingoyang’ana kwa Inu;*
*Khululukireni.*
2. Ndinachimwa poganiza
Ndi polankhulanso,
M'ntchito zanga ndachimwanso;
Khululukireni.
3. Ndinachita mphulupulu,
Ndinakunyozani,
M'ntchito zanga ndalephera;
Khululukireni.
4. Zonse ndinakonda kale
Ndi zopanda pake,
Sindinakhuta nazotu;
Khululukireni.

## 348

1. MEMA nkhondoyo, wadza
Mdaniyo,
Kweza mbendera ya Mbuye.
Bvala zidazo, imba nyimboyo,
Khazikikatu pa Mulungu.
*Haya, anzathu, itilinda nkhondo;*
*Limbanitu, nkhondo nja Yesu.*
*Musafoke, m’thyole linga lawo;*
*Mbuye ndiye Wopambanayo.*
2. Mlungu mverani, mphamvu
Patseni,
Tithandizeni, tipempha.
Nkhondo itatha, titapambana,
Tidzalandiratu korona.
3. Mlake mdaniyo, mwimbe
m'njiramo
Mpaka nkhondoyo ileka.
Zida konzani, mantha tayani,
Pitikitsani adaniwo.

## 349

1. M'MANDA, nagonamo
Yesu Ambuye,
Anadikiratu
Tsiku lija.
*M'manda naukamo*
*Napambana ’'dani akewo;*
*Anauka kupambana imfayo,*

*Ali moyo ndi oyeramtimawo.*
*Wauka, wauka!*
*Aleluya wauka!*
2. M'manda munalibe
Yesu Ambuye,
Nadikira chabe
Alondawo.
3. Imfa yalephera
Kumutsekera,
Anachotsa zonse
Zomzingazo.

## 350

1. YENDANI, Mfumu yamtendere
Anthu akuimbirani;
Apfuuletu Hosana,
Agonjeranso anthuwo.
*Yendanitu m'ulemudi,*

*Pulumutsani anthuwo.*
2. Yendani, Munthu Wachisoni,
M’mudzi wa Yerusalemu;
Angelo amapenya ’Nu
M’mene mwafera anthuwo.
3. Yendanitu, Wansembe wathu,
Mtanda wanu mwanyamula
Watisandukira dalo,
Watitengera moyowo.
4. Yendani mwaulemerero,
Akulindirani mphotho,
Moyo wanu wosatha
Watilonjezera moyo.

# 351

1. KAMWANA Yesu ’nabadwa,
Ndi Iye Mlungu Wamphamvu;
Angelo anapembedza
Mwana wakhanda Iyeyu.
2. Kamwana kaja ’nayamba
Kuonetsera Atate,
Lero anena Kumwamba:
“Tiana tidze Kwa Ine.”
3. Tibwera ndi tianato
Kukabatiza ’menewa;
Muŵachitire chifundo.
M’ŵapatse Mzimu Woyera.
4. Angelo anu asunga
Tiana tathu tofoka;
Pa njira yanu tiyenda,
Mulembe m’Mwamba maina.
5. Mukonda nyimbo za ana,
Kokoma amaimbatu;
Ndi ana athu atama
Atate, Mwana ndi Mzimu.

# 352

1. YESU Mbuye, onani
Tadza poitana Inu;
M’dzina lanu tifika
Osekera Kwa Atate;
Mkhale nafe Inu nokha
Tikaimba nkupemphera.
2. Mbuye, Mzimu Woyera
Munapatsa ana anu
Kukalonga mumtima
Mawu ndimo mvanu womwe:
Zinthu zonse pansi pano
Sizikondweretsa ife.
3. Mzimu, mlonge m’mtimamo
Maphunziro achifundo;
Timve lero ndi maŵa
Ndi masiku onse Yesu.
Ndimo m’Mwamba tidzaona
Tidazimva pansi pano.

# 353

1. PEMPHERO ndiko kufuna,
Kulakalakatu;
Ndi monga moto liyaka
Mumtima wa munthu.
2. Pemphero ndiko kulira,
Ngakhale misozi,
Kupenyetsetsa Kumwamba,
Mulungu mpafupi.
2. Pemphero ndiko kufuna
Kwa mwana wamng’ono;
Ndiponso mawu amphamvu
93
A munthu wamvanu.
3. Pemphero ndiwo mweyawo
Apuma akristu;
Ndi mapemphero tiloŵa
Dziko la imfalo.
4. Mutiphunzitse, Mbuyathu,
Kupempha kotero,
Kuyandikira kwa Mlungu
Ndi mtima wabwino.

# 354

1. Ndisauka, ndinachimwa,
Koma inu mnandifera,
Ndimo ndamva mnd’itana
Mwana mlungu ndingubwera.
2. Ndisauka, ndimasowa
Mpamvu ya kuyera m’mtima
Mwazi wanu wanditsuka;
Mwana mlungu ndingubwera
3. Ndisauka, sindikhoza
Kuiletsa nkhondo m’mtima,
Ndichisoni, mantha, nkhawa
Mwana mlungu ndingubwera
4. Ndisauka, sindiona

Ndingudwale, ndilefuka,
Zonse ndizitaya Kwa ‘nu,
Mwana mlungu ndingubwera

5. Inde yesu mulandira.
Muchilitsa, mpulumutsa
Mau anu ndivomera
Mwana mlungu ndingubwera.
6. Inde, yesu, mundikonda
Zonse zina ndizitaya;
Tsono kukakhala wanu,
Mwana mlungu ndingubwera.

# 355

1. YESU, ndipemphera
Mndithangate
Kukonda Inutu,
E, kwambiri.
Koposa zonsezo
Za pansi panopo,
Ndikondane
Ndinu Mbuye.
2. Kale ndinafuna
Za pansipa,
Tsopano ndilira
Inu nokha.
Ndifuna kukonda
Inu kopambana
Zinthu zonse
Za pansipa.
3. Inu ndidzatama
Nthaŵi zonse,
Imfa ikafika
Ndidzanena:
“Ndifuna kukonda
Inu, Mbuye wanga,
Kopambana
Zonse zanga.”

# 356

1. PANALITU wakudwala
Amene akakhala
Pakhomo la sunagoge:
Kuti anthu ena
Amuone iye.
*Yenda iwe, yenda.*
*Yenda iwe, yenda,*
*Siliva ndilibe;*
*Mwa Yesuyo, yenda!*
2. Kukondwa kwa wodwalayo
Kunali kopambana;
Iye anatumphatumpha,
Kuzungulira
Sunagoge yense.
3. Lero lino Mbuye Yesu
Aitana nonsenu;
Mukamvera ndi kumtsata,
Mudzakondwera
Ndi mdalitso wake.

# 357

1. YESU watidzera, watidzera,
Way’tana anthu onse.
Udzimvere wekha.
*Aleluya, Aleluya!*
*Aleluya, Aleluya!*
*Udzimvere wekha.*
2. Kudziŵa ukudziŵa, ukudziŵa,
Kulibe zachisoni.
Udzimvere wekha.
3. Atumwi atumika, atumika,
Akulalika Yesu.
Udzimvere wekha.
4. Yesu Mpulumutsi, Mpulumutsi
WA dziko lili lonse.
Udzimvere wekha.
5. Kumva ulikumva, ulikumva,
Ungonyalanyaza.
Udzimvere wekha.
6. Bwerani inu nonse, inu nonse,
Mudzalandire moyo.
Mudzimvere nokha.

# 358

1. MUDZE Kwa Yesu, musachedwe.
Kalata ilozera njira;
Amaitanatu tonsefe,
Bvomerani Iye.
*Tidzakondweradi m’Mwambamo*

*Posonkhana komwe kuli 'Ye;*
*Tidzakhala naye komweko Ku*
*Dziko losafa.*
2. Lolani ana, mumve Mlungu,
Tsegulani mitima yanu,
Sankhani Iye, Bwenzi lanu;
Musachedwe, mudze.
3. Ganizansoni, ali pano,
Mthenga wake mverani lero;
Mawu okoma ati lero,
Musachedwe, mudze.

# 359

1. MWA ine, moyo wanga ndi Yesu
(*Yesu)* Yemwe anafera ine,
Ndiye anandiwombola;
Yesu, Yesu.
2. Mwazi wake ndi chitsime changa,
*(Yesu)* Pamene ndikasambamo
Zochimwa zanga zidzatha;
Yesu, Yesu.
3. Yesu Mfumu, ine ndingadzafe
*(Yesu)* ngati mundisiya ndekha,
Kukhala ndekha sinditha;
Yesu, Yesu.
4. Yesu Mfumu, ine ndisekere
*(Yesu)* Inu Mpulumutsi wanga
Pamene mukhala nane;
Yesu, Yesu.

# 360

1. LEKANI kubvutika ndi zinthu za Padziko,
Musekerere kuti tidzaimbira Yesu.
*Imbira!*
*Timwimbire Yesu,*
*Mpulumutsi wathu!*
*Imbira!*
*Timwimbire Yesu,*
*Tonse tidzakondwera.*
2. Musadziunjikire chuma cha Padziko
Dzimbiri ndi njenjete
Zimachiononga.
3. Koma mudziunjikire chuma cha Kumwamba
Kumene anapita Mtsogoleri wanu.
4. Aliponso adani am'kati ndi Akunja;
Yesu watisekera, tidzakuimbirani.
5. Aliponse mabvuto, ena ndi oipa;
Yesu mutimasule Kwa adani athu.

# 361

1. Ndine mbusayo wabwino
Ndinafera nkhosazo;
Yotaika ndaifuna,
Mpaka ndataya moyo.

*Mbulu wandi'gamba nthiti*
*Wandin'gambanso m'manja,*
*Wandin'gambira zbvala,*
*Ndasala waumphawi.*

2. Nkhosa zanga zimandimva,
Ndikaziitanazo;
Ndimazipatsa moyowo,
Atate nazisunga.
3. Atate wondipatsazo
Ali nayo mphamvutu,
Kuzidyetas, kuzisunga
Palibe wolandazo.
4. Mudzaona zovalazo
M'kati ali fisiyo;
Mananyengedwa anthuni,
Ine ndine mbusayo.
5. Tamverani anthu inu,
Ine ndine mbusayo;
Ndine njira, ndine khomo
Thawani mimbuluyo.

# 363

1. TIYAMIKE mbuye Yesu
Yemwe anatifera
Imfa ija yoopsetsa
Kuwombola tonsefe.
*Ife*
*Tapulumukadi,*
*Ife*
*Tapulumukadi,*
*Imfa,*

*Imfa yoopsa ija yapamtanda,*
*Imfa,*
*Imfa yoopsa ija yapamtanda.*
2. Panalibe mwa abale
Yemwe akadakhoza
Kupereka moyo wake
Kuwombola tonsefe.
3. Tikondwera ife tonse
Pakuona ntchitoyo
Anachita Mbuye Yesu
Kuwombola tonsefe.

# 364

1. MZIMU ndi mtogoleri
M'njira yachikristuyo,
Atitsogoleratu
Paulendo wathuwu.
M'yoyo ikondweratu
Pomva mawu akewo,
Pakunena Mzimuyo,
"Osokera, bwerani."
2. Bwenzi lathu ndinutu,
95
Mkhale m'fupi nafetu;
Msatisiye tokha 'fe
Pakuyenda m'mdimamu;
Pakuwomba mphepozo
Timaopa m'mtimamo,
Tsono timve mawuwo:
"Amantha 'nu, bwerani."
3. M'mene ntchito yathatu,
M'mene tidikira 'Nu,
Pakukhumba m'Mwambamo,
Tsono tipempherabe.
Nthaŵi ya mabvutowo
Tikhulupirira 'Nu,
Tsono timve mawuwo,
"Okondedwa, bwerani."

# 365

1. MASO ndi maso ndi Kristu,
Kodi ndidzachitanji
M'mene ndidzaona Yesu,
Yemwe anandifera?
*Ndidzamwona maso ndi maso*
*Kuseri kwa mitambo;*
*Posachedwa ndidzamwona*
*M'ulemerero wake!*
2. Tsopano ndimwona Iye
Mwa chizimezimetu;
Tsiku lija ndidzaona
Ulemerero wake.
3. M'mene masautso onse,
Nthenda, imfa, zidzatha,
Dziko likadzakonzedwa,
Ndidzakondwa koposa.
4. Lodala tsiku lomwelo
Ndidzamwona Yesuyo,
Mpulumutsi wanga yemwe
Anandikonda ine.

# 366

1. MVERANI mbiri yozizwitsa
Ya Yesuyo kalelo;
Iyeyo 'nadza pansi pano
Kutipulumutsa 'fe.
*Ndani anatiwombola?*
*Mwana wa Mlungu pa mtanda.*
*Anatani?*
*Anafera.*
*Ali kuti?*
*Akhaladi m'Mwamba*
*Kutipempherera.*
2. Palibe m'modzi akanatha
Kuloŵa m'malo mwake;
Ngakhale anali wamkulu
'Nasiyidwa namnyoza.
3. Kodi mudzampembedza Mbuye
Mpulumutsi wathuyo?
Kodi inu mudzaloŵamo
Mu Ufumu wakewo?

# 367

1. Ufuna kowomboledwa kodi?
Ilipo mphamvu m'mwazi wake,
Ufuna kugonjetsa zoipa?
Muli mphamvu m'mwazi wake.

*Muli mphamvu yodabwitsatu*
*M'mwazi WA yesuyo*
*Muli mphamvu yodabwitsatu,*
*M'mwazi wamwana WA nkhosa.*
2. ufuna kuleka kunyadako?

Ilipo mphamvu m'mwazi wake,
3. idzatu pa mtanda nutsukidwe.
Muli mphamvu m'mwazi wake.
3. ufuna kuyera kopambana?
Ilipo mphamvu m'mwazi wake,
Zoipa zonse azayeretsa
Muli mphamvu m'mwazi wake.
4. ufuna kugwera ntchito yake?,
Ilipo mphamvu m'mwazi wake,
Ufuna kumuimbira iye?
Muli mphamvu m'mwazi wake.

## 368

1. MPULUMUTSI Wokondedwa,
Mwandipulumutsa ine;
Ndine wanu, wanu nokha,
Wotsukidwa m'mwaziwo.
*Aleluya, Aleluya,*
*Mwanawankhosa ndinutu:*
*Mwazi wanu wanditsuka,*
*Aleluya kwa Yesu.*
2. Mtima wanga wabvutika,
Zaka zonse ndingochimwa;
Tsono sindikangalika,
Ndingopuma mwa Yesu.
3. Mwandipatulira ine,
Kwa Inu ndidzipereka,
M'moyo, m'imfa mboni yanu
Ya chipulumutsocho.
4. Aleluya, mwandigula,
Ndipo mudzandisungabe;
Mwazi wanu ndi wamphamvu
Kuyeretsa konseko.

## 369

1. MLENDO ali pakhomo,
Mloŵetseni
*(Mloŵetsenitu),*
Wadza kalekalelo,
Mloŵetseni
*(Mloŵetsenitu);*

Mtsegulire msangatu,
Wakuyerayerayo,
Mwana wa Mulunguyo,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu).*
2. Utsegule mtimawo,
Mloŵetseni
(*mloŵetsenitu),*
Ukachedwa achoka,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu):*
Ndiye Bwenzi lakolo,
'Dzapulumutsa 'we;
'Dzakusamaliranso,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu).*
3. Imva mawu akewo,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu),*
Sankha Iye leroli,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu);*
Wangoima pa khomo,
'Dzakusangalatsa 'we,
Udzamlemekezatu,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu).*
4. Mlendo wa Kumwambayo,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu),*
'Dzakupatsa zonsezo,
Mloŵetseni
*(mloŵetsenitu);*
'Dzakhulukira 'we,
Ndipo potsirizapo
'Dzakutenga m'Mwambamo,
Mloŵetseni
*(Mloŵetsenitu).*

## 370

1. NDIPEREKA zanga zonse
Mwaufulu Kwa Yesu;
Ndidzamkonda kopambana,
Tsiku lili lonsetu.
*Ndiperekatu*
*Zonse Kwa Yesu;*
*Ndipereka zonse Kwa 'Nu,*
*Dalitsenitu.*
2. Ndipereka zanga zonse
Pamapazi a Yesu;

Zapadziko ndazikana,
Nditengeni Yesu 'Nu.
3. Ndipereka zanga zonse,
Ndipo n'khale wanutu;
Mzimu wanu 'ndidziŵitse
Kuti ndine wanudi.
4. Ndipereka zanga zonse,
Ndili wanu ndense 'ne;
Nditamanda Dzina lanu,
Aleluya, Ambuye.

# 371

1. Kwathu sipaziko, ndingopitilira
Ndazikundikira chuma kumwambako
Mungelo akodola pakhomo la mwamba
Ndipo dziko la pansi sindiyetsa kwathu.

*Muye, ndinu bwenzi langa ndithu*
*Ndichitenji ngati kumwamba sikwathu*
*Mungelo akodola pakhomo la mwamba*
*Ndipo dziko la pansi sindiyetsa kwathu.*

2. Andiyembekeza aulithuchi ndidziwa
Mpulumusi wanga wondikhulululukira
Adzandi pyolesa pamene ndafoka.
Ndipo dziko la pansi sindiyetsa kwathu.
3. Mayi watsogola ku ulemelero,
Ndfuna kugwira dzanja Lake Konko.
Andi dikhilanso pakhomo la m'mwamba
Ndipo dziko la pansi sindiyetsa kwathu.
4. Mu ulemelero tidzakhala m'yaya,
Oyeramtimawo alikulambira.
Ati, "aleluya kwa mlungu wa mphamvu'
Ndipo dziko la pansi sindiyetsa kwathu.

# 372

1. Chisomo chodabwitsacho,
Chapulumutsa ne'
Woipa wapambanatu
Ndapeza moyo ne'
2. Chisomocho chachotsatu
Mantha a infa,
Pakukhulupirira ye'
Ambuye yesu.
3. Chiso chandisungadi,
Panjira yangayo,
Chisomo chidzasunga ne'
Mpakatu kwathuko.
4. Kwathu tizaimba nyimbo
Ya chisomo chake,
Yolemekeza mlunguyo
Munthawi zosatha.

# 373

1. CHITETEZO chachikulu
Chotuluka m'mwaziwo
WA Ambuye Yesu Kristu,
Mpulumutsi wathuyo.
Mpulumutsi, chitetezo
Chipezeka m'mwaziwo.
2. Ndi chimwemwe ndimaona
Mtsinjewo wa mphamvutu;
Zonditsutsa zachotsedwa,
Yesu wanditsuka mbuu!
Mpulumutsi, chitetezo.
Chindisangalatsatu.
3. Tchimo lonse ligonjera
Chikondicho cha Yesu,
Maganizo 'yeretsedwa;
Ndingofuna zakezo.
Mpulumutsi, chitetezo
Chigonjetsa mtimawu.
4. Ndili nawo moyo w'satha
Wochuluka mwa Yesu,
Mzimuyo wadzaza mtima
Ndi chimwemwe chakecho.
Mpulumutsi, chitetezo,
Chiyanjano chomwenso.
5. Mantha, nkhaŵa, ndi chisoni
Zachotsedwa zonsezo;
Mbuyeyo ndimkhulupira,
Anditsogoleratu.
Mpulumutsi, chitetezo,
Ndimkondadi Yesuyo.

# 374

1. AMBIRI tikondwera mwa Yesu,
Nanga inu? Nanga inu?
Tapeza chipulumutso ndithu;
Nanga inu?

*Masiku onse timakondwera*
*Pakumva Mawu ake a Yesu;*
*Wolalikira tidzamumvera;*
*Nanga inu?*
2. Ife tiyembekezera YESU,
Nanga inu? Nanga inu?
Chimwemwecho chili
Mumtimamu;
Nanga inu?
3. Titasokera tinabwerera,
Nanga inu? Nanga inu?
Tidziŵa kuti ndiwo uchimo;
Nanga inu?
4. Tinachoka munjira ya imfa,
Nanga inu? Nanga inu?
Takopeka ndi Mawu a Yesu;
Nanga inu?

# 375

1. MBUYE dalitsani Afrika,
Itukulidwe nyanga yake;
Mverani mapemphero athu,
Ndipo mtidalitse ife ana anu.
*Mbwere Mzimu,*
*Mbwere Mzimu, mbwere!*
*Mbwere Mzimu*
*Mbwere Mzimu,mbwere!*
*Mbwere Mzimu*
*Woyera, Woyera.*
*Mbuye, dalitsani*
*Ife ana anu.*
2. Dalitsani mafumu athu,
Akumbukire Mlengi wawo;
Aope ndi kunjenjemera,
Ndipo m'ŵadalitse iwo ana anu.
3. Dalitsani mafuko onse,
Aweruze bwino maiko;
Adzichepetse ndi kuopa,
Ndipo mtidalitse tonse ana anu.

# 376

1. MLUNGU dalitsani Malaŵi,
Mumsunge m'mtendere;
Gonjetsani adani onse,
Njala, nthenda, nsanje;
Lunzitsani mitima yathu
Kuti tisaope,
Mdalitse Mtsogoleri, nafe,
Ndi Mayi Malaŵi.
2. Malaŵi dziko lokongola,
La chonde ndi ufulu,
Nyanja ndi mphepo ya m'mapiri,
Ndithudi tadala;
Zigwa, mapiri, nthaka, dzinthu,
Mphatso zaulere;
Nkhalango, madambo abwino,
Ngwokoma Malaŵi.
3. O! Ufulu tigwirizane
Kukweza Malaŵi;
Ndi chikondi, khama, kumvera,
Timutumikire;
Pankhondo nkana pa mtendere
Cholinga n'chimodzi,
Mayi, Bambo, tidzipereke
Pokweza Malaŵi.

# 377

1. ANTHU m'maiko onse
Akhala mitundu;
Kapena m'dziko lino
Akhala anzathu;
Agona mwa zoipa,
Apulukiradi,
Ati, Mutilangize
Abale, bwerani.
2. Ngakhale alemera
Ndi chuma cha dziko,
Kodi akakondwera
Opanda Mulungu?
Kodi akhala mwaŵi
Otsata zawozo?
98
Iyai, awonongeka,
Apeza tsokalo.
3. Ndi ife akudziŵa
Chikondi cha Mlungu,
Kodi tidzaŵamana
Kuŵala kwa Kristu?
Chipulumutso! Inde,
Tichibukitsetu,
Kuti mitundu yonse
Ibwere kwa Yesu.
4. Akristu nyamulani

Maneno a Mulunguyo,
Ndi moyo lalikani
Pa dziko lonselo;
Ndi Yesu Mpulumutsi
Anatiferatu;
Adzabvomera onse;
Ndi Mwana wa Mlungu.

## 378

1. PADZIKO pano tikhalira
M'moyo wosauka;
Komatu kwa Mulungu kuli
Dziko lakudala;
Mbuyathu Yesu wapitako,
Iye 'natsogola;
Tidzamtsatira ife tonse,
Tsiku lomaliza.
*Tiyeni, tiyeni,*
*Ku dziko lakudala;*
*Tidzafikira m'dziko ilo*
*Tsiku lomaliza.*
2. Masiku tikatsala ife
M'dziko mwathu momwe
Mulungu watipatsa ntchito,
Tikazigwiritse.
Pamene zakuipa zathu
Zisautsa ife,
Tikapemphere Mbuye wathu,
Atipulumutse.
3. Ulendo wathu ukadzatha
Tidzafika kwathu,
Adzatifitsa ife komwe
Yesu Mbuye wathu.
Sitidzapeza masautso
M'dziko la Mulungu,
Tidzakondwera chikondwere
Nthaŵi zonse zathu.

## 379

1. POZUNZIDWA inu ponseponse
Ndi kufoka m'mtima nazo
zonsezo,
Ŵerengani madalitso anuwo
Ndipo mudzazizwa potsirizapo.
*Ŵerengani madalitsotu,*
*Anakupatsani Mlungudi.*
*Ŵerengani lina linanso,*
*Ndimo mudzazizwa potsirizapo.*
2. Kodi muvutidwa naye katundu?
Ngwolemera mtanda muusenzatu?
Ŵerengani madalitso anuwo,
Ndimo mudzaimba dzuŵa
lonselo.
3. Poyang'ana ena ndi ndalamatu,
Ganizani kuti Mbuye wanudi
Adzakupatsani zake zonsezo,
Chosagula chuma chanu
chonsenso.

## 380

1. YESU Mbuyetu, mwafera
Mphulupulutu zanga,
Ndimo ndamva mund'itana,
Mutitu, Msachedwa.
2. Zonse za m'dziko zidzatha,
Koma za moyo m'Mwamba
Zomwe zidzakhalitsatu,
Chakatu ndi chaka.
3. Nyengo ifika, chenjera!
Adzakukana m'Mwamba.
Lapa zoipa zakozo,
Kuti ukaloŵe.

## 381

1. TAMANDANI Mbuye,
Inu atate,
Mpatse Yesu mitima yanu.
99
2. Tamandani Mbuye,
Inu mafumu,
Mpatse Yesu mitima yanu.
3. Tamandani Mbuye,
Inu abale,
Mpatse Yesu mitima yanu.
4. Tamandani Mbuye,
Inu nonsetu,
Mpatse Yesu mitima yanu.
5. Tamandani Mbuye,
Mipingo yonse;
Aleluya, Aleluya!

## 382

1. MVERA mtima wanga 'we
Akufunsa Ambuye;

"Wosauka WA'mphaŵi,
Kodi undikondadi?"
2. "Ndakupeza womanga,
Ndamasula zinsinga,
Ndakulonda kutali,
Kodi undikondadi?"
3. "Akaleka amake
Kusungira mwanake,
Ine sin'kuleka 'yi,
Kodi undikondadi?"
4. "Ndakukonda ku imfa
Ndi chikondi chosatha,
Kwaulere, kwambiri,
Kodi undikondadi?"
5. "Msanga ndidzabweratu,
Udzaona ulemu,
Udzakhala ndi Ine,
Kodi undikondadi?"
6. Mbuye ndisaukadi,
Chimachepa chikondi,
Mtima wanga mudziŵa,
M'ndipunzitse kukonda.

## 383

1. MBUYE mtsitsimutse
Ntchito zonse zanu!
Utsani anthu akufa
Ndi mawu a mphamvu.
2. Mbuye mtsitsimutse
Ntchito zonse zanu!
Tauzirani pa ife
Ndi mweya wa Mzimu
3. Mbuye mtsitsimutse
Ntchito m'mitimamo!
Mumvetse njala kwa Inu—
Mutikhutitsenso.
4. Mbuye mtsitsimutse
Ntchito m'kati mwa anthu!
Chikondi chawo chikule
Muchikolezetu.
5. Mbuye mtsitsimutse!
Mawu alimbike,
Pamene aphunzitsidwa
Onsewa amvere!
6. Mbuye mtsitsimutse!
Mzimu adzazetu!
Kwa ife kudzakhala mwayi,
Kwa Inu ulemu.

## 384

CHIKHULUPIRIRO chathu
Tatchulachi pakamwapo,
Mulungu athandize 'Fe
Chikhale cha mumtimamo.__

## Reference

***Christian literature association of Malawi***

**P.o box 503 blantire [© 1974]**

*EDITED BY: ELIAS MUTEYA*
*RCZ LILANDA CONGREGATION*
*NO: 0972580751*

